

MPHAMVU YANGWIRO MU

CHIFOOKO CHANGWIRO



Mmawa, abwenzi. Ndi chabwino kutulukanso mmawa uno pa mmawa wamvula uwu, wachipale, mmawa wosokonezeka. Ndikudziwa kuti ambiri a inu mwakhala ndi nthawi ndithu yoyendetsa, kuchokera kutali. Ndipo ife tiri ndi ena...abwenzi ofunika awa amene akuchokera ku Chicago ndi Alabama ndi Georgia ndi Tennessee ndi Illinois ndi kuzungulira konse, mmasiku awa, chotero ife tiri... ndikudalira kuti Mulungu akupatsani chitetezo Chake pamene mukuyenda. Ndipo ndi pemphero lathu kuti Iye akutetezereni panjira, mmisewu yowopsya imeneyi pamene iyo imaterera mu nyengo yachisanu. Ndipo lino limakhala dziko loipa mu nthawi yachisanu. Ilo limadzakhala dziko lokongola kwambiri limene liripo mu chirimwe kapena mu ng'amba, koma mu nyengo yachisanu ndi nyengo ya dzinja zimadzakhala zoipa kwambiri.

² Tsopano, ine sindikuganiza kuti iwo ayamba kale kujambula kumeneko. Ndipo ndikungofuna ndipange neno lokhudza Lamlungu lathali, mu uthenga. Chifukwa chimene ine—ine ndinaigwira tepiyo ndipo sindinawalole iwo kuti akagulitse tepiyo, kuitulutsa iyo panja, chabwino, chinali chifukwa chakuti ine ndimayenera kuti ndiyiyang'anenso iyo poyamba. Chifukwa nthawi zambiri, mwanjira imeneyo, ine ndimatha kunena zinthu mu tchalitchi muno zimene sindingaziyeke pamaso pa anthu onse monga choncho, chifukwa nthawizina zimapangitsa zopunthwitsa. Ndipo nthawizina izo zimapereka mafunso pakati pa anthu athu kuno ku kachisi. Ndipo izo ndi... .

³ Ine sindimanena izi...kunena zinthu zimenezo kuti ndikhale wosayanjanitsika, koma nthawizina pansi pa kudzoza umadziwa zinthu zimene iwe sunga...sungayerekeze kuti uwauze anthu. Ndiye nthawizina pansi pa kudzoza chinachake chimakupulumuka, inu mwaona, ndipo iwe sungachizindikire icho. Ndipo chimodzi mwa zinthu zimene ine ndikukhulupirira kuti chinanenedwa (Lamlungu lapitali) chimene chingampangitse wina...pamene ine ndinanena kuti ine sindimakhulupirira konse mu kuyitanira paguwa. Mukuona?

⁴ Ine ndikufuna ndinene izi ndiponso momveka kuchitira kuti mumvetsetse. Panalibepo konse kuyitanira paguwa kumene kunachitika mu Baibulo lonse. Mulibemo chinthu choterocho mu Lemba. Palibe paliponse kudutsa mu mibadwo pamene izo zinapangidwa kufikira m'badwo wa Methodisti, pafupifupi zaka thuu handirede zapitazo, mwaona.

⁵ Kuyitanira paguwa ndi pamene anthu amabwera ndi kudzayesera kuwachonderera ndi kuwakoka anthu, “Tabwera, John. Iwe ukudziwa, iwo. . . Amayi ako anamwalira, akukupempherera iwe. Tabwera, John.” Kumeneko sikukhudzika, abwenzi. Ayi. Iwo—izo zoterozo, ine. . . kawirikawiri simumamva wina amene amapita patali kwambiri. Ndipo, mmenemo, umapeza chirichonse. Ndi chifukwa chimene mpingo wasokonezeka momwe uliri lero, ndi chifukwa cha zinthu zoterozo.

⁶ Kukhudzika, iwe sumasowa kuti uchite kunena kanthu, m’bale, Mulungu ali pamenepo ndipo wachita kale ntchitoyo. “Petro akanali chiyankhulire Mawu awa, Mzimu Woyera unadzagwa pa iwo amene anamva Mawu.” Mukuona? Mukuona? Mukuona? Panalibepo kuyitanira paguwa, mwaona, palibe chinthu choterocho.

⁷ Tsopano, guwa ndi malo opemphererapo pamene munthu aliyense wobwera ku tchalitchi akuyenera kubwerapo poyamba, kudzagwada pa guwa, kupemphera mwakachetechete kwa Mulungu ndi kupereka pempho lawo la pemphero ndi—ndi la okonedwa awo, ndi kumuthokoza Mulungu pa chimene anawachitira iwo, kenako nkubwerera pa mpando wawo.

⁸ Ndipo kenako mtchalitchi ndi malo amene Mawu a Mulungu. . . “Ndipo chiweruzo chimayambira Mnyumba ya Mulungu,” kumene chiweruzo cha Mawu chimatulukirako. Ndiye. . . Koma lero, ife—ife timazisintha zimenezo motembenuza kwambiri.

⁹ Tsopano, ine ndiribe kalikonse kotsutsa aliyense amene amapanga kuyitanira paguwa, mwaona. Ndizo. . . Ndipo ine ndapangapo kochuluka inemwini, ndipo mwinamwake ndidzapanga kwina kochuluka ngati ndizipitirirabe. Koma kwa ine ndekha. . . Mwaona, iwe—iwe—iwe umawasonkhanitsa ochuluka kwambiri. Ndipo palibe chotsutsa izo, palibe choyipa mwa icho. Izo nzabwino. Mukuona?

¹⁰ Chifukwa, mvetserani, Yesu anati, “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine azadza kwa Ine.” Uko nkulondola. Chotero ndiye, mwaona, iwo ali. . . Izo zimaponyera kuyitanira paguwa kwanu kunja kwathunthu palimodzi. Mukuona? Mukuona izo? “Onse amene Atate. . .” Inu. . .

¹¹ Wathu—udindo wathu ndi “kulalikira Mawu.” Baibulo linati, “Onse amene anakhulupirira anabatizidwa.” “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku, chikhululukiro cha machimo.” Chiyani? “Batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, mwaona, ndipo mudzalandira kenako mphatso ya Mzimu Woyera.”

¹² Koma pamene muwanyengerera ndi kuwakokera ndi kuwawopsyeza anthu, ndi kuwayankhula anthu kuti abwere. . . Anthu ayenera azibwera akuganzira, mwabwinobwino, pansa pa kukhudzika, ndi kudzambulandira Khristu. Kenako chinthu choyamba chimene iwo amachita iwo akangomulandira Khristu atakhala mmipando yawo, chinthu chotsatira ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo amenewo kuti iwo atsimikizika kuti iwo ndi wolakwitsa. Umo ndi momwe iwo amachotsedwera machimo awo, mwaona. Chifukwa iwo alapa; abatizidwa monga chikumbutso kwa anthu, kuti, “Ndalandira Khristu ngati Mpulumutsi wanga”; zikatero ndiwe woti ulandira Mzimu Woyera.

¹³ Ndipo, tsopano, anthu ambiri amapitirirabe, kuwachonderera ndi kuwayitanira pa guwa, ndi zina zotero monga choncho, zimene ziri zabwino. Ine ndipita ndi zimenezo, zimenezo ndi zabwino mwangwiro momwe ine ndikudziwira, aliyense amene akufuna kuti azichita zimenezo. Koma, kwa ine, izo si za Mwamalemba, inu mwaona, ndipo chotero ine—ine ndimangokonda kukhala ndi Lembu.

¹⁴ Ndipo chotero ndi chifukwa chake ine ndinaigwira tepiyo chinali chifukwa chakuti mukaitulutsa iyo ife tingakhale ndi makalata faivi handirede pa sabata oti tiwayankhe. Aliyense. . . Kungoponda pa mwambo waung’ono umene wina ali nawo, ndipo ndizo zonse zimene inu muyenera kuchita, ndiye izo zonse zimabwereranso.

¹⁵ Ndipo ine ndikuganiza, nthawi zambiri, kuti ndimakhala wotsutsa kwambiri pa zinthu zosiyanasiyana monga zimenezo. Ndipo ine sindimatanthauza kuti ndikhale mwanjira imeneyo, koma nthawizina maudindo amakukokera iwe mbali imeneyo, inu mwaona, iwo—iwo amakupangitsa iwe kutsamira mbali imeneyo. Ndipo chotero ine ndikutsimikiza anthu akumvetsa izo.

¹⁶ Tsopano, ndife oyamikira kwambiri kuti tikadali ndi Atate Akumwamba achifundo Amene—Amene amayang’ana pa zolakwitsa zathu ndipo samaziwerengera izo kwa ife.

¹⁷ Ine ndimawerenga mu Bukhu la—la Aroma, mutu wa 4, kumene Paulo analemba—ndemanga ya Umulungu ya moyo wa Abrahamu. Tsopano, ife tikudziwa kuti Abrahamu nthawi zambiri ankakhala ngati wokhumudwa monga ife timachitira. Koma pamene a. . . ndemanga yake inalembedwa, panalibe zokhumudwitsa zake zirizonse zimene zinatchulidwa, inu mwaona, sizinatchulidwepo nkomwe. Anati:

Abrahamu sanagwedezekere pa lonjezo la Mulungu mwa kusakhulupirira; koma anali wamphamvu. . . akupereka mayamiko kwa Mulungu;

¹⁸ Mwaona, ndipo umo ndi momwe ine ndikuyembekeza kuti wanga udzalembedwere Kumeneko, si zolakwitsa zanga ndi chirichonse, koma basi zimene ine ndimayesera kuchita, cholinga cha mtima wanga kuti ndiwachitire anthu a Mulungu.

¹⁹ Ndipo tsopano ife tabwera mmawa uno kuti—kuti tidzayesere kubweretsa uthenga waung'ono apa umene mwina Ambuye ayika pa ife kuti tiwupereke kwa anthu. Ndipo ndikudalira kuti zikuchitirani inu ubwino ndi kundichitira ine ubwino, chifukwa ife tiri limodzi ndipo tikukhala mu nthawi yopambana, ndipo masiku otsiriza. Chotero basi ife tisanakhale ndi pemphero, ine ndikufuna kuti ndiwerenge malo angapo mu Mawu; amodzi tisanapemphere, ndipo amodzi tikapemphera. Ndipo poyamba, kuti titsegule msonkhano wathu, kapena, gawo ili la iwo, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Bukhu la Ahebri. Mutu wa 11 wa Ahebri, ndi sarte- . . . Ndime ya 32, kuyambira, kuyankhula za *chikhulupiriro*.

Tsopano ine ndidzanenanso china chiyani? kapena nthawi idzandithera kuti ndinene za Gideoni, . . . za Baraki, . . . Samsoni, . . . Yefita; . . . Davide . . . Samueli, ndi za aneneri:

Amene mwa chikhulupiriro anagonjetsa maufumu, anachita chirungamo, analandira lonjezano, anatseka pakamwa pa mikango,

Anazimitsa chiwawa cha moto, anathawa lupanga lakuthwa, ndipo mu kufooka . . . analimbikitsika, anakhala amphamvu pankhondo, anathamangitsa alendo, magulu a nkhondo a alendo.

Akazi analandira akufa awo ataukitsidwa ku moyo . . . ndipo ena anzunzidwa, osalola chiwombolo; kuti akalandire chiwukitsiro chabwinoko:

Ndipo ena anali ndi mayesero . . . kunyoza kwankhanza . . . kukwapulidwa, eya, komanso a nsinga . . . kuponyedwa mndende:

Iwo anagendedwa miyala, iwo anachekedwa pakati, iwo anayesedwa, . . . ophedwa ndi lupanga: . . . ankayendayenda mu zikopa za nkhusa ndi zikopa za mbuzi; kukhala opanda pokhala, . . . ndi kuzunzidwa;

²⁰ Taonani mikutiramawu iyi:

(Za amene dziko lapansi silimali lowayenera:) iwo ankayendayenda mu zipululu, ndi mmapiri, ndi mmapanga ndi mmapanga a dziko.

. . . onsewa, atalandira umboni wabwino mwa chikhulupiriro, sanalandire lonjezano:

Mulungu atatikonzera ife chinthu china chabwino kwa ife, kuti iwo popanda ife asapangidwe kukhala angwiwo.

21 Pamene ndiwerenga nkhani zimenezo za asirikali olimba amenewo, ine ndimadabwa pamene umboni wathu wawung'ono uti udzayime ndi anthu amenewo pa Tsiku limenelo.

22 Tisanapemphere, kodi alipo angafune kuti akumbukiridwe ndi Mulungu? Ingokwezani mmwamba dzanja lanu, ndipo chirichonse chimene inu mukuchisowa mulole Iye achiwone ndi kumva ndi kuchipereka icho kwa inu tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

23 Athu achisomo, Atate achikondi, ife modzichepetsa tikuyandikira Mpandowachifumu Wanu mmawa uno mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu, kuti tidzapereke pemphero kwa ife eni ndi ena. Inu choyamba, Ambuye, mutikhululukire ife zolakwa zathu zonse ndi mphulupulu zathu. Ndipo kenako ife tipempherera ena, Ambuye, kuti nawonso akhululukidwe.

24 Ndipo Mpingo Wanu ubweretsedwe pafupi ndi Inu. Pakuti moona, Ambuye, mu mtima mwathu tikukhulupirira kuti ndinu wokonzeka kugwira ntchito ndi Mpingo Wanu, wokonzeka kuwutulutsa Iwo kuchokera mdziko ndi kusinthidwira kukalowa mu Ufumu wa Mulungu. Koma, Ambuye, tithandizeni ife kuti tidzikonzekeretsere tokha ku ora limenelo. Mulole mmawa uno ukhale nthawiyo, Ambuye, kuti kuchokera kwa mmodzi mpaka kwa tonsefe “tisiye pambali cholemetsa chirichonse ndi tchimo limene mophweka silimachedwa kutifooketsa ife, kuti tikhoze kuthamanga ndi chipiriro mpikisano umene wayikidwa patsogolo pathu.”

25 Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, lero, kuti Inu muchize odwala ndi osautsika. Ambiri akuvutika kudutsa fukoli, ndi miliri, ndi “tizilombo” monga adokotala amaziikira izo. Ndipo ine ndikupemphera kuti ukoma Wanu wa machiritso, Ambuye, ukhale kwa anthu amenewo.

26 Kenako ubwere kwa osonkhana athu apang'ono pano mmawa uno. Ambiri ayendetsa kwa ma mailosi mahandirede, kuyambira usiku wathawu ndi kudutsa usiku ndipo mpaka mmawa, lero, ndi kuyendetsa molimba kuti apite ku kachisi. Ndipo nkwachisanu komanso pa msewu. Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu makamaka muwadalitse iwo. Mosakayika ambiri ayenera kuti apereke gawo lalikulu la chakudya chawo cha sabata ikudzayi, kapena chirichonse chimene chikanakhala, kapena zinthu zimene iwo akanakhoza kuwonongerapo ndalama zawo, pa mafuta ndi zinthu, kuti abwere.

27 Mulungu, iye amene abwera kwa Inu wopanda kanthu adzapita ali wodzaza. Inu munalonjeza zimenezo. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mudzaze mitima yawo ndi madengu awo (ya miyoyo yawo) yodzaza kwambiri ndi zinthu zabwino za Mulungu kuti iwo achoke akungotumphuka nazo ndi “chisangalalo chosaneneka ndi ozadza ndi Ulemelero.” Basi

mulole zikho za anthu ofunika awa zisefukire, ndi zinthu zauzimu ndi zabwino zochokera kwa Mulungu.

²⁸ Mudalitse dzanja lirilonse, Inu mukudziwa chosowa chimene chinali kuseri kwa dzanja limenelo, Ambuye. Ine ndikupempha kuti Inu muwadalitse iwo mwapadera. Ife takuonani Inu mu sabata yapitayi momwe Inu munayankhira pemphero modabwitsa mu mphindi zochepe, nthawi zadzidzidzi ndi matenda ndi mavuto. Inu ndinu Mulungu, wopezeka paliponse, woima ndi antchito Ake. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muyime pafupi ndi awa mmawa uno. Mupereke kwa iwo chokhumba chawo, Ambuye, cha mtima wawo. Ine sindikuhulupirira kuti zinali za chinthu chirichonse chodzikonda, chirichonse—cholinga chirichonse choipa kumbuyo kwake. Ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo.

²⁹ Ndipo tsopano, Atate, ndikumbukireni ine, ife, lero, ndipo mulole ine ndikhoze kudzichotsa ndekha panjirayi. . . Tonse a ife, kuyambira kwa abusa mpaka mmusi kwa—ana, mulole ife tithe kudziyika tokha pambali pa guwa la Mulungu ndipo mutsegule mitima yathu ndi kumvetsera kwa Mzimu Woyera pamene Iye aziyankhula kwa ife. Mutembenuze zotengera zathu za Wanu mda- . . . kuti tilandire madalitso Anu, ndi mbali yakumanja mmwamba. Kenako mutsanulire mphamvu ya Mafuta odzozera mwa iwo. Ndi kutipatsa ife mphamvu, Ambuye, zimene ife tikuzisowa za masiku amene ali mtsogolo. Perekani mdalitso uwu. Ife tikupempha izo mu Dzina la Yesu. Amen.

³⁰ (Hmm, ine sindikudziwa. Inu mungotenga nambala yake ya foni ndikumuuza kuti ndimuimbira tikaweruka ku tchalitchi. Ine sindikudziwa.)

³¹ Mundipempherere ine. Ine . . . M'bale Jack Moore pa foni, ndipo akundikakamizabe kuti ine ndikakhale kumeneko sabata ino. Mukuona? Ine sindikungomverera basi . . . mpaka kwa izo, mwaona, ndipo chotero ine sindikudziwa choti ndichite. Ine ndimamukonda M'bale Jack. Ndipo msonkhano waukulu umenewo ukubwera kumusi uko ndipo iye awakana amuna, monga Booth-Clibborn ndi iwo, kubwerako. Chotero akudikirirabe, wayika kulengezetsa kwake ndi zonse monga choncho, akudikirirabe kuti ine ndibwere. Chotero ine—ine ndimakonda kumverera kupsyinjika kwenikweni kuti ndipite, inu mwaona. Ndipo ine . . .

³² Ndipo, tsopano, pamene ife tikutsegulanso tsopano ku Akorinto Wachiwiri, ndipo ife tiyambira ndime ya 12 ya Akorinto Wachiwiri, ndi kuwerenga ndime imodzi ya Lemba kwa mutu, ngati Mulungu ati alole. Akorinto Woyamba, a . . . Kapena Akorinto Wachiwiri, kani, mutu wa 12 ndi ndime ya 9. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge chiganizo choyambacho . . . Kapena chiganizo chachiwiri cha ndime ya 9, gawo la icho:

Ndipo iye anati kwa ine, chisomo Changa ndi chokwanira kwa iwe: pakuti mphamvu yanga imapangidwa yangwiro mu kufooka. . .

³³ Ndiroleni ine ndiwerenge Ilo kachiwiri tsopano kuti mutsimikize kuti mwapeza mutuwo:

Ndipo iye anati kwa ine, (Uyu ndi Mulungu akuyankhula kwa Paulo), Chisomo changa ndi chokwanira kwa iwe: pakuti mphamvu yanga imapangidwa yangwiro mu kufooka. . .

³⁴ Ndiye ngati ndingawutchule iwo mutu, ndikufuna kugwiritsa ntchito uwu, mphamvu. . . *Mphamvu Yangwiro Mu Chifooko Changwiro*. Ngati ife tikhala ndi chifooko ife timakhala ndi mphamvu. Ndi mutu wosazolowereka pa. . . mu msonkhano wa Chipentekoste, kupanga. . . kutenga mutu wa *chifooko*, chifukwa nthawizonse timachitira umboni “ndife amphamvu kwambiri.”

³⁵ Ndipo ine ndinanenapo kale, kuti, ine ndimangoyesera kupemphera kudutsa mu sabata ndi kufufuza chimene chingakhale chabwino choti ine ndichibweretse pamaso pa osonkhana. Ngati zikanangokhala kubwera kuno kuti ndizamvedwe, ine ndikanakonda ndikanamumva winawake mmawa uno atayima pano.

³⁶ Moona mtima, mpaka masiku angapo apitawo, ine ndinali uko mu Kentucky ndi anthu a M’bale Gabehart kumeneko. Pamene ine ndinachoka pa malo awo, m’bale wofunika uyu ndi mkazake ndi banja ndi iwo, mpaka ine ndinakhudza ganizo ili.

³⁷ Ine ndinali nditalowa mnyumba basi pang’ono izo zisanachitike. Ine ndinali nditayima panja, ndipo dona anati, “Ndikufuna kuti ndiyankhule ndi mtumiki ameneyo.” Ndipo ine ndinapita ku nyumba yawo yaying’ono. Ndipo kumeneko kunali. . . Iye anati, “Ndinu M’bale Branham?”

Ndipo ine ndinati, “Inde mayi.”

³⁸ Iye anati, “Ndikuchita manyazi ndi mawonekedwe a nyumba yanga,” ndipo iye anati, “kuti ndikufunsemi inu kuti mulowe.” Iye anayamba kulira. Iye anati, “Koma ine—ine ndiri ndi chosowa chotero ndipo ndiri ndi chidaliro chenicheni mwa inu.”

³⁹ Ndipo ine ndinapeza kuti kunali kumene Mlongo wathu wamng’ono Cox amene ife timakhala naye kumusi—kumusi uko, a—agogo aang’ono okhala ndi tepi rekoda akudutsa mmadera oyandikana nawo akusewera matepi. Ndi zimenezotu! Ndiro lingalirolo! Mukuona?

⁴⁰ Ine ndinayang’ana pozungulira mnyumba iyi, nyumba yaying’ono yophweka, pafupifupi ngati imene ine ndinaleredweramo, koma khoma lodzaza ndi zithunzi za Khristu. Apo panali Baibulo pa tebulo. Ine ndinati, “Sindinakhaleenso ndi ulemu mmoyo wanga, uwu ndi mtundu

wanyumba imene ndimakonda kulowamo.” Iye anapempha pempho la winawake. Ndipo maora asanu kuchokera pamene ife tinapemphera limodzi, agogo aakazi aang’ono awa ndi ine tinapemphera limodzi, Mulungu anali atayankha.

⁴¹ Chotero ife tinapemphera kachiwiri, ndipo Amayi Cox ndi ine ndi iwo titazungulira tebulo mmawa umenewo, tinali titaweramitsa ndi kumupempha Mulungu kuti atipatse mwayi wochita chinachake kudzera mu kuyesetsa kumene iwo anapanga. Ndipo, kupyolera mu kupempha zimenezo, Mulungu anatsegula njira. Inu mukuona? Iye ndi Mulungu!

⁴² Timayesetsa kupanga zofooka zathu kukhala zowiringula. Timafuna kunena momwe ife tiriri aakulu, momwe ife tiriri opambana. Ndikuganiza kuti ndi chimodzi mwazinthu zimene ine. . . Mulungu anandipatsira ine mutuwo, chinali choti tichotse zimenezo kuzichotsa mmalingaliro athu. Mukuona?

⁴³ Pali zinthu zazing’ono zimene ife timachita. Ndipo ndi chimene ife timabwerera ku tchalitchi, ndi kudzapeza pamene zolakwa zathu ziri, ndi zinthu zimene ife tikhoza kudzipangitsa tokha abwinoko. Ngati ife tibwera ku tchalitchi pa china—cholinga china kuposa ichi, ine ndikuwopa kuti sitingapeze zochulukwa za zobwerera ku tchalitchi. Ife tiyenera kuti tizibwera kuti tidzapeze zofooka zathu, kudzapeza malo athu oyipa ndi athu. . . momwe. . . kudzawona momwe tiriri ochepa, ndi kuika chidaliro chathu mwa Winawake amene ali wamphamvu. Koma pamene tikhala ndi zifooko. . .

⁴⁴ Tilipo ambiri a ife amene timakonda kuchitira umboni kapena timakonda kuganiza kuti ndife osakwanira ndipo, chotero, timapanga zimenezo kukhala chowiringula, “Ndiribe maphunziro, ndiribe kuthekera, sindingathe kuchita *ichi*.” Ndipo ngati muzisunga zimenezo ndi kumachita izo mwanjira imeneyo, kupitirira kumachita monga choncho, ndiye inu simungathe kuchita chirichonse. Koma chinthu chomwecho chimene ife timachitira kuwiringula, mwa zifooko zathu, Mulungu amagwiritsa ntchito chinthu chomwecho kuti agwire nacho ntchitoyo. Mukuona? Iye amatidikirira kuti ife tifiike pa chikhalidwe chimenecho kuti Iye akhoze kutigwiritsa ife ntchito. Ife—ife timatenga zowiringula ndi kuti, “Chabwino, ine—ine—ine—ndine. . . sindingathe kuchita izi, ndine wosakwanira. Ine—ine sindingathe kuchita izi.” Ndipo Mulungu amatenga chinthu chomwecho kuti agwire nacho ntchitoyo. Izo nzoona.

⁴⁵ Ndicho chifukwa chimene Iye—Iye amatisankhira ife, chifukwa ife tiri mu chikhalidwe chimenecho. Tsopano, izo zikumveka zachirendo, koma maminiti pang’ono chabe ife tifika ku chifukwa chake, ngati Mulungu alola.

⁴⁶ Ife—ife tikupeza, monga ife takhala tikuwerengera, kuti zifooko ndi kukanidwa. . . ndipo tikupeza kuti anthu amenewo amene ali ofooka kwambiri ndi okanidwa ndi dziko lakunja, ndi

amene amakhala ngwazi za Mulungu, amene amagonjetsa pa mzere wakutsogolo, amatenga iwo amene ali—ali . . . amadzimva okha kuti ndi osayenera.

⁴⁷ Uko kunali m'bale wa Methodisti, atatu a iwo amene amabwera ku mpingo uno ochokera uko ku Ohio, kapena kumpoto kwa Indiana. Iwo ananena kwa ine osati kale kwambiri, anati, “M'bale Branham,” anati, “ife tangolandira kumene Mzimu Woyera, kodi tsopano tingafunefune mphatso za utumiki wathu?”

Ine ndinati, “Musachite zimenezo! Zisiyeni izo zokha.”

⁴⁸ Ndipo anapotoloka ndipo anandiyang'ana ine, anati, “Ndangowerenga kumene bukhu la m'bale wina limene linatiuza ife kuti tikalandira Mzimu Woyera ife ‘tikuyenera tizifunafuna mphatso,’ kuti awa agwiritse ntchito Mzimu Woyera uwu.”

Ine ndinati, “Ndipo nkukhala munthu wodzikweza!” Mukuona?

⁴⁹ Ngati mungazindikire mu Baibulo, nthawizonse amakhala iwo amene amayesetsa kuti achoke kwa izo, amene Mulungu amawagwiritsa ntchito. Nthawizonse munthu . . . akafuna kuti achite chinachake ndipo akuganiza kuti ali nako kuthekera kokwanira kuti akhoza kuyigwira ntchitoyo, Mulungu sangakhoze konse kumugwiritsa ntchito munthu ameneyo. Tamuyang'anani Mose, akuthawa; tamuyang'anani Paulo, akuthawa; ndi ena onse a iwo, akuyesetsa kuti achoke kwa izo.

⁵⁰ Ine ndinati, “Musafunefune kalikonse. Mulungu ali ndi chirichonse cha inu, Iye adzapereka icho kwa inu.” Mukuona? “Ndipo mungomulola Iye—mungomulola Iye asamalire zimenezo.” Ine ndinati, “Ndiye mumapeza nthawi zina monga zimene tiri nazo, lero, kuti aliyense akufuna kuchita *ichi* ndi kuchita *icho* ndi kukhala munthu wamkulu winawake. Tayang'anani chimene ife tinalowa nacho icho, inu mwaona.”

⁵¹ Mmallo moyesera kuti tikhale opambana ife tikuyenera kuti tidziyesera—tidziyesera kuti tipeze momwe tingakhalire aang'ono. Mukuona? Tikatero Mulungu akhoza kutigwiritsa ife ntchito. Ine ndiri ndi Malemba angapo olembedwa apa amene ine ndikuyenera kulozerako, ine ndikuganiza, koma ine . . . ife . . . Ine mwinamwake sindikhala ndi nthawi yoti ndichite zimenezo. Koma ife tiri . . .

⁵² Zindikirani kuti zimatengera—wofooka ndi wokanidwa, ndipo kwenikweni ngwazi iliyonse imene Mulungu anayamba wakhalapo nayo pamzere wakutsogolo anali munthu wa mtundu umenewo. Munthu amene anakanidwa, munthu amene ankaganiza kuti anali wosakwanira, munthu amene analibe kuthekera konse, ndiye ndi munthu amene amakhala mu chikhalidwe chabwino kuti Mulungu ayambe kumugwiritsa ntchito. Uko nkulondola. Ndi pamene iwo amamverera ngati

kuti iwo sangathe, iwo alibe kalikonse, ndi pamene Mulungu akhoza kuwagwira iwo ndi kuchita nawo chinachake. Mukuona? Pamene... Koma pamene ife tikuganiza kuti tingathe kuchita zimenezo, ndiye Mulungu sangatigwiritse ife ntchito chifukwa ife tikufuna kuchita izo tokha.

⁵³ Ndipo, kenako, mbali inayo, timakhala ndi kumverera uku ndipo timaganiza ndiye kuti ndife osakwanira, ndipo sitikufuna kuchita zimenezo; komano ngati ife titangomvetsera kukuitana kwa Mulungu, icho ndi chinthu chomwecho chimene Mulungu amafuna kuti ife tilowemo, mawonekedwe a mtundu umenewo, kuti Iye athe.

⁵⁴ Pamene ife tikhala osakwanira, ifeeni, ndiye ife timakhala ogonjera ku Mzimu wa Mulungu. Nthawizonse pamene ife tiganiza kuti tikhoza kuchita izo, ndiye kuti ife sitingathe kuchita izo. Koma pamene ife tifika pa malo pamene ife tikudziwa kuti ife sitingathe kuchita izo, ndiye ife nkudzipereka tokha kwa Mulungu ndipo Iye amachita izo. Chotero ndiye ngati tiri ife tikuyesera kuti tichite izo ife tidzalephera, koma ngati ife tingadzipereke tokha kwa Mulungu ndiye Mulungu sangalephere. Pali chinthu chimodzi chokha chimene Mulungu sangachite, ndipo, ndicho kulephera. Iye akhoza kuchita china chirichonse kupatula kulephera. Koma Iye sangalephere.

⁵⁵ Chotero bola ngati ife tikuyesetsa mwa ifeeni ndi kudalira pa kuthekera kwathu komwe, ndi zina zotero, chabwino, ife sitidzachita kalikonse. Koma pamene ife tifika pa malo pamene ife tikudziwa kuti ndife opanda kanthu, ndiye Mulungu akhoza kutigwiritsa ife ntchito.

⁵⁶ Chinthu chofunikira, chimodzi mwa zinthu zofunikira zimene tikuyenera kuzidziwa bwino... Tsopano kumbukirani ichi, ndipo makamaka inu alaliki achichepere, ndi mamembala wamba chimodzimodzi. Pali chinthu chimodzi chimene tikuyenera kuchigonjetsa ngati tikuyembekezera kukwaniritsa khumbo la Mulungu mmoyo mwathu, ndiko kuti, tikuyenera kujaila ganizo la *kuthekera kwa munthu*. Ngati tingadzafike pamalo pamene tikuganiza kuti titha kuchita izo ndi nzeru zathu ndi kuthekera kwathu komwe, tikuyenera kudziwa bwino izo mwanjira yoti ife tikhoza kuchichotsa chinthucho ndi kuziyika izo pambali kuti Mulungu adzathe kutigwiritsa ife ntchito. Uko nkulondola.

⁵⁷ Ndi kupanga kudzipereka kwathunthu! Ife sitingagwiritse ntchito kuthekera kumodzi. Ife tikuyenera kupanga kudzipereka kwathunthu! Ndipo, kuti ubwere kwa Mulungu, iwe ukuyenera kudzipereka kwa Iye zonse solo, thupi, ndi mzimu. Chirichonse chimene iwe uli chikuyenera kuperekedwa kwa Mulungu, kuti Iye akhoze kuchita chifuniro Chake mwa iwe ndi mwa ine.

⁵⁸ Tsopano, izo ndi zovuta, ine ndikudziwa, chifukwa ife nthawizonse timafuna kuyikapo gawo lathu, chinachake

chimene ife *tikuchidziwa*, ife tikudziwa kuti tikufuna kuchita izo. Ife timati, “Chabwino, ine—ine ndikungodziwa kuti zikuyenera kuchitidwa chomwecho.” Koma bola ngati mukuchita izo mwanjira imeneyo zidzakhala zolakwika, ndipo Mulungu sadzagwiritsa konse khama limenelo. Mwinamwake, ndi chithandizo cha Ambuye, ife tilowa mu zimenezo mu maminiti pang’ono, ndipo kungokuwonetsani inu momwe Mulungu sangagwiritsire ntchito kuthekera kwanu.

⁵⁹ Ndipo ndiro limene liri vuto ndi dziko lero: pali zokuchitikirani zambiri za kuseminare, zoyikidwa kwambiri pa maphunziro, zochuluka zoyikidwa pa ubale kapena chiyanjano mu chipembedzo, timagomerana wina ndi mzake, timawagomera amuna amene ali ndi kuthekera.

⁶⁰ Baibulo linati, “Inu mungakhale bwanji ndi chikhulupiriro pamene inu—pamene inu muli. . .” Tiyeni tiwone, kodi Lemba limenelo liri bwanji? “Kodi inu mungakhale bwanji ndi chikhulupiriro pamene mukugomerana wina ndi mzake?”

⁶¹ Pamene tikuyembekezera, ndikuti, “Munthu uyu, iye ndi munthu wamkulu. Uyu ndi munthu wamkulu, ndingotsamira pa iye,” zimenezo sizimukondweretsa Mulungu pamene inu muchita zimenezo. Ife tiyenera tizitsamira pa Mulungu ndipo Mulungu yekha! Ife sitikuyenera kuti tizidalira kuthekera kwa ife ni kapena munthu aliyense. Ife tikuyenera kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu.

⁶² Palibe kuthekera, sindikusamala kuti ndi kwa ndani, sikudzagwiritsidwa ntchito pamaso pa Mulungu. Mulungu ayenera kuti atulutsemo kuthekera kwathu konse mwa ife Iye asanakwaniritse cholinga Chake. Ngati Iye ali ndi chinachake choti ife tichite, ndipo nthawizonse pamene timverera kuti tikuchita ntchito yabwino kwambiri kuchokera mu izo, ndiye ife sitidzatha konse kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu.

⁶³ Tsopano, inu mukuti, “Inu mukupanga neno lalikulu moyipa pamenepo, M’bale Branham.” Ndipo ilo—ilo ndi limodzi lotambalala, koma mungoyang’ana pozungulira ndipo mupeze ngati ziri zoon kapena ayi.

⁶⁴ Tayang’anani pozungulira lero pa kuchita bwino kwathu konse kwakukulu kumene ife tikuganiza kuti tachita, ndipo Chikhristu chiri kuti mu United States? Tayang’anani pa mipingo yathu yonse ndi zipembedzo, ndi avangeri athu ndi misonkhano yamachiritso, ndi china chirichonse chimene ife takhala nacho, ndipo icho ndi chiyani? Zoyipa kwambiri kuposa momwe zinaliri pachiyambi! Ndi zoipa kwambiri lero kuposa momwe zinayamba zakhalirapo, chifukwa ife tayera kuti tichite izo mu kuthekera kwa munthu.

⁶⁵ Iwo amasonkhana pamodzi ndi kupanga mapemphero aatali ndi kupita kunja kuno. Ndipo tinali ndi tsiku lina kumene iwo anali ndi ochuluka chotero, handiredi ndi fifitini sauzande,

kapena chinachake chonga icho, atasonkhana pamodzi, awiri onse Achiprotestanti ndi Akatolika; amanena mapemphero ena, ndi kupemphera mapemphero ena, ndi kupanga mapemphero ena, ndi zina zotero. Iwo mwina akanati asasonkhane, izo ziribe kanthu pamaso pa Mulungu.

⁶⁶ Tsopano, ngati ndikukhala wotsutsa, mundikhululukire ine. Mukuona? Koma ine—ine nda... Ukuyenera kuchikhomerera chinthucho pansi. Mukuona? Ukuyenera kuzipanga izo zikhomerere msomali.

⁶⁷ Ndipo icho chinachita ubwino wanji? Palibe. Ndipo sipadzakhala mpaka munthu aliyense amene amadzinenera kuti ndi Mkristu adzaiwale mphamvu zake ndi kudzipereka yekha kwa Mulungu.

⁶⁸ Zikadzatero Mulungu adzakhoza kukwaniritsa cholinga chake potumiza... osati chitsitsimutso, koma, m'bale, chimene Iye akuyenera kuchita poyamba ndi kutumiza kupha, uko nkulondola, kuti ife *tithe* kutsitsimuka. Inu mukuyenera kufa musanabadwe mwatsopano, ndipo mukuyenera kutero... Iye akufuna kudzipha kwa ifeeni. Kachisi uyu akusowekera kuphedwa, ndipo ine ndi iye. Tonsefe, tikufunikira a—kuphedwa kuti titsitsimutsidwe mu moyo watsopano, kugwira kwatsopano, chiyembekezo chatsopano, chotichitikira chatsopano! Tikusowekera poyamba tsiku la kulira.

⁶⁹ Tikusowa malo odzipereka kwa Mzimu mmalo modalira kwambiri maphunziro ndi mapurogramu athu, ndipo ife... misonkhano yathu ndi zonse zimene tiri nazo. Ife—ife—ife timadalira mgwirizano ndi atumiki osiyanasiyana kuti tigwirizane. Ife timalola ambiri... “Ngati ife sitingathe kupeza ochuluka chotero, bwanji, ife sitingachite izo. Sitingapite ku mizinda popanda izo.” Ndipo kenako, pamene ife tichita zimenezo, ife tikuzipanga izo mu makina aakulu kwambiri amene ali ndi kugogoda kwa utsi mmenemo, mwaona.

⁷⁰ Chotero ife—ife tikuyenera kuti tichoke kwa izo, kuthekera kwa umunthu kumeneko. Ife tikuyenera kufika pa malo amene tingathe kupereka ma solo athu ndi miyoyo, ngakhale kwa mkazi wapakhomo, kwa mlimi, kwa makaniko, kapena aliyense amene ife tiri, ife tikuyenera kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu ndi kudziwa kuti “ife sitiri kanthu.” Ndiye nkumulola Mulungu ayambire pamenepo. Kenako Iye ayamba kusuntha, kumagwira ntchito. Ndipo izo zikuphatikizapo tonsefe, aliyense. Ndicho—chinthu chimene ife tikuyenera kuchita.

⁷¹ Mbiriyakale imatsimikizira, ikutero tsopano, imatsimikizira (mbiriyakale imatero) kuti Mulungu nthawizonse amasankha osadziwika kuti akhale odziwika Ake. Mulungu amatenga munthu amene si kanthu.

⁷² Lero, pokhapokha ngati ukhala ndi maziko abwino a zaumulungu, kulibwino usayesere kukayandikira mzindawo,

usayesere nkomwe ngakhale kukayandikira msonkhanowo. Koma ngati uli ndi maziko abwino, ndi kuphunzitsidwa kwabwino ndi zinthu kumbuyo kwako, ukhoza kupita mu mzinda uliwonse ndi kukayanjana nawo, kukakhala ndi msonkhano waukulu. Chabwino, si msonkhano... Ndi msonkhano, chimodzimodzi monga wina uliwonse, koma iwo umachita ubwino wanji? Mwaona, inu—inu apobe... Inu mutenge atsikana aang'ono awa ndi anyamata akubwera, akutafuna chingamu ndi kumapita ku guwa, ndipo akazi ndi amuna akupita kumeneko kuti akangonena iwo “anapita ku guwa,” kulowa mchipindamo kukalangizidwa ndi kubwerera panja ndi kukakonkhedwa kapena kumizidwa, kapena chirichonse chimene iwo ali, ndi a—ndipo chaka kuchokera pamenepo...

⁷³ Mmodzi wa avangeri athu aakulu anati, ngati akanadziwa kuti akanatha kusunga teni peresenti ya owatembenuza ake kwa chaka chimodzi, iye akanasangalala. Pamene, ndiye, pamene ngati iye akanakhala ndi owatembenuza sauzande, chaka chotsatira akuyenera kukhala—kukhala teni sauzande a iwo. Mwaona, tikuphonya chandamale, tikuphonya cholinga.

⁷⁴ Ena aife timamanga izo pa kumvetsa kwaluntha, “Oh,” kuti, “mdziwazonse uyu, munthu uyu ndi sikolala wophunzitsidwa. Tiyenera tiziwaphunzitsa anthu athu ndi kuwaphunzitsa iwo.”

⁷⁵ Enawo amazikhazikitsa izo pa zogirigisha zina za—kuyenda, kugwedeza, kulira, kufuula, kuvina mu Mzimu, kapena chinachake, ntchito ina yotengeka ya kunjwa. Ndipo izi ndizoyipa basi monga maphunzirowo! Ngati mdierekezi sangakupezeni inu kumbali *iyi*, iye adzakukankhirani inu kumbali *iyi*.

⁷⁶ Koma nkhani yake ndi yakuti, kusakhala ndi chirichonse chimene ungachidalire mwa iwe wekha kapena chirichonse chimene ungachite, basi kwathunthu, kupereka kwathunthu kwa zifooko zako kwa Mulungu, ndikuti, “Ine ndiri pano.” Osakhala ndi kalikonse, opanda kuthekera kumene ungamakudalire!

⁷⁷ Fufuzani mmbuyo kudutsa mu Lemba ndi kupeza, monga ine ndalemba Malemba apa amene ine ndikulozerako. Ena mmbuyo kudutsa mu Malemba, ife tikupeza, kuti Mulungu nthawizonse ankagwiritsa ntchito osadziwika kuti akhale odziwika Ake. Iye nthawizonse ankawatenga iwo amene dziko lawakana, m'badwo wamakono unali utawakana, ndipo ndiwo mtundu umene Iye anawutenga kuti awugwiritse ntchito.

⁷⁸ Talingalirani za—atumwi. Taganizani za Petro, nsodzi, wopanda maphunziro okwanira kuti alembe dzina lake. Yohane, mbuli ndi wosaphunzira. Amuna amenewo! Iye anawalambalala olemekezeka ndi ansembe ophunzira ndi anthu otchuka a masiku amenewo, masikolala, mamembala a mpingo,

ndipo anakatenga-. . .anthu amenewo amene ankaganiza kuti iwo anali winawake, ndipo anakawatenga iwo amene anali osadziwika ndi kuwagwiritsa ntchito iwo.

⁷⁹ Tsopano, winawake akhoza kukhala mmodzi wa anthu Ake, Mulungu akhoza kuwagwiritsa iwo ntchito ngati ali okonzeka kuiwala kuti iwo ndi winawake. Ngati iwe wakonzeka kuyiwala kuti ndiwe *winawake* ndi kukhala *wosadziwika*, ndiye Mulungu akhoza kukugwiritsa iwe ntchito ndi kupanga winawake kuchokera mwa iwe. Mukuona? Koma iwe uyenera kuiwala kuti ndiwe wofunikira kwambiri.

⁸⁰ Tiripo ambiri a ife, ambiri a ife timachita zimenezo mu—mmiyoyo yathu. Mwamsanga pamene. . .Anthu ena, mwamsanga iwo akangokhala Akhristu, iwo amakhala amwano, osayanjanitsika, uko nkulondola, pamene iwo akungotenga mosemphanitsa njirayo. Iwo akupita chobwerera mmbuyo mmalo mopita kutsogolo. Pamene. . .Zochuluka zimene ungazipeze kuchokera mwa iwemwini, ndi malo ochulukirapo kuti Mzimu Woyera ulowemo.

⁸¹ Monga Elisha anamuuzza Yehosafati ndi iwo, anati, “Kumbani malo awa adzaze ndi maenje. Mukakumba mozama, mukhala ndi malo ochulukirapo a madzi.” Ndipo zochuluka za ife eni, za—zinyalala za kuthekera kwathu komwe kumene ife tingathe kuzitaya kuchokera mwa ife, ndi pamene tidzakhale ndi malo ochuluka kuti adzazidwe ndi Mzimu wa Mulungu; bola ngati titachita zimenezo.

⁸² Paulo, amene tangomuwerenga kumene apa mu—mu Akorinto, mu Akorinto Wachiwiri, ife tikupeza kuti munthu uyu anali munthu wamkulu. Iye anali sikolala, munthu wamkulu. Koma iye ankayenera kuti ayiwale zonse zimene iye ankazidziwa, kuti adzamudziwe Khristu.

⁸³ Ine ndilola. . .ndiwerenga limodzi la Malemba awa apa, kuti inu—inu mukufuna kuwerenga ndi ine. Tiyeni titembenuzire ku Akorinto Woyamba, mutu wa 2 ndi ndime ya 1, miniti yokha. Ndipo tiyeni tiwerenge apa miniti yokha zimene Paulo ananena, munthu wophunzira wamkulu uyu, zimene ananena za iyemwini, zimene ankayenera kuchita. Akorinto Woyamba, a—mutu wa 2 wa Akorinto Woyamba, ndipo kuyambira ndi ndime ya 1. Mvetserani kwa sikolala uyu.

⁸⁴ Mwamuna uyu anaphunzitsidwa. Iye ankakhoza kuyankhula pafupifupi chinenero chirichonse chimene chinalipo padziko lapansi. Iye ankayenera kudzitamandira za izo. Iye analeredwa pansu pa kagulu kokhwimitsa ka Afarisi, ndipo abambo ake anali Mfarisi. Kenako iye anadzakhala “Mfarisi wa Afarisi,” ndipo izo zikutanthauza kuti iye anali—iye anali mwamtheradi—wokhwimitsitsa wa Afarisi. Iye anali munthu wamkulu. Ndipo iye anali ndi ulamuliro, ndipo iye anali wanzeru.

85 Bambo ake anamupatsa iye maphunzira pansa pa mphunzitsi wapamwamba amene analipo mdziko lonse, Gamalieli, pa nthawi imeneyo anali mphunzitsi wodziwika kwambiri pa iliyonse ya masukulu. Paulo anadzakhala munthu wa mtundu umenewo. Iye anaphunzira chinenero chirichonse. Anaphunzira kuwerenga maganizo. Iye anaphunzira zinthu zonse zosiyanasiyana zimene ziripo mu—mu...kuti aphunzire mwanjira imeneyo. Ndipo anatsamira kwambiri ku—ku kachisi wa—wa ansembe ndi—munthu wamkulu. Ndipo iye anali akuyendayenda akuwusokoneza Mpingo.

86 Mvetserani kwa munthu yemweyu, ndi maphunzira onse awa, iye atamulandira Khristu. Mvetserani zimene iye ananena. Momwe iye analiri wamphamvu ndi wamkulu, iye ankayenera kuiwala izo. Iye ankayenera kuzindikira kuti iye sakanatha kudzidalira pa yekha. Iye ankayenera kuzindikira kuti maphunzira ake sanali kanthu. Iye ankayenera kuzindikira, kuti kuphunzira konse kumene iye anakhalapo nako, ankayenera kuiwala chirichonse chimene anaphunzitsidwa. Mvetserani kwa iye tsopano.

*... Ine, abale, pamene ine ndinabwera kwa inu, ...
osati ndi kupambana kwa kuyankhula...kwa nzeru,
mwaona, kufotokoza kwa inu umboni wa Mulungu.*

“Ine sindinabwere kwa inu kudzakuzani inu, ‘Tsopano, ndine Dokotala Saulo wochokera ku Sukulu ya *Chakuti-ndi-chakuti*, Ine ndine...wochokera ku kagulu kakakulu ka chipembedzo ichi.’ Ine sindinabwere kwa inu monga chomwecho.”

*Pakuti ine ndatsimikizika kuti ndisadziwe
chirichonse pakati panu, kupatula Yesu Khristu,
ndi iye wopachikidwayo.*

87 Pamenepo, mvetserani pa umboni wa munthu wonga ameneyo.

“Ine ndatsimikizika kuti ndisadziwe kalikonse ka kuthekera kwanu. Ine ndikudziwa kuti mulibe kanthu mwa inu ndipo ndangotsimikizika kudziwa chinthu chimodzi chimene ndikuchiwona mwa inu, ameneyo ndi Yesu Khristu ndipo Iye wopachikidwayo. Mpulumutsi wopachikidwa pakati panu, ndizo zonse zimene ine nditi ndizizindikire.”

88 Mvetserani kwa iye.

*Ndipo ine ndinali ndi inu mu... (ukulu? Mu
chiyani?)...kufooka, ndi mmantha, ndi...
kunthunthumira kochuluka.*

89 Kodi inu mungamulingalire munthuyo, Mfarisi wa Afarisi, mphunzitsi wa aphunzitsi, munthu amene anaphunzitsidwa kuyambira ali mwana (chifukwa cha utumiki) kuti adzakhale munthu woyankhula bwino amene anali wanzeru ndi waluntha,

kubwera pamaso pa gulu la anthu monga Akorinto ndi kudzati, “Ndinali ndi inu mu kufooka, ndi mmantha, ndi kunthunthumira kochuluka”? Munthu amene analitembenuzira dziko chadodolido, mmishonare wamkulu amene anayamba wadziwikapo, anavomereza kuti iye “anabwera mu kufooka,” osati monga sikolala wophunzitsidwa, koma “mu kufooka, mmantha,” kuwopa kuti angachoke pa Njira kwina kwake. “Mu kunthunthumira kochuluka,” chifukwa sankadalira mu kuthekera kwake komwe.

⁹⁰ Chifukwa chimene iye “ankawopa,” osati chifukwa choti amawopa kalikonse, koma iye ankawopa kuti akhoza kumukhumudwitsa Mulungu mwa njira ina, kuti iye akanasokoneza kuthekera kwake komwe mu Zimenezo; chinachake chimene iye anali atachiphunzira, chimene iye anali nacho. . . Iye ankawauza iwo kuti, “Sindinabwere kwa inu ndi ulemu wa kuyankhula uwu (ine ndikubwera kwa inu *mmantha* kuti ndibwere mwanjira imeneyo), koma ine ndikubwera kwa inu wosadziwa kalikonse koma Khristu, ndi iye wopachikidwayo.”

Ndipo ine ndinabwera kwa inu mu mantha, ndi kufooka, ndi mu kunthunthumira kochuluka.

Ndipo kuyankhula kwanga ndi kulalikira kwanga sikunali ndi mawu okopa anzeru za munthu, koma mu chiwonetsero cha Mzimu ndi. . . mphamvu:

⁹¹ Tamvetserani kwa munthu uyu amene anali wankhondo anali atadzivula yekha. Amen! Ngati pali chirichonse chimene masukulu athu akusowa lero, ngati ndi chirichonse chimene mipingo yathu ikusowa lero, ndi kudzivula okha, maganizo anu omwe ndi kuthekera kwanu. Dzivuleni nokha pamaso pa Mulungu pokhapokha mutayesera kupanga kanthu mwa inueni.

⁹² Ine ndikuyembekeza inu. . . izo zikufika pansi mozama kwa ife, ziwiri zonse pano ndi dziko la tepi, nalonso, kuti muzindikire kuti simukuyenera kukhala kanthu. Osati wodziwa-zonse, osati winawake wamkulu, koma *wosadziwika*. Inu mukhale. . . mukuyenera kusanduka fumbi. Mukuyenera kufika pamalo amene mukudziwa kuti inu si kanthu. Ndipo osakwera konse pamwamba pa izo, pakuti nthawi yomweyo inu mukangokwera pamwamba pake inu mudzakwera pamwamba pa Mulungu. Mukuyenera kudzisunga nokha mu fumbi ndi panjira yopita ku Damasiko. Mukuyenera kudzipatula nokha pa akavalo anu apamwamba. Ndipo izo ndi za kulikonse, kuno ndi mdziko la tepi.

⁹³ “Kuyankhula kwanga,” iye anati, “sikuli. . . mu mawu okopa a munthu ndi nzeru za munthu, koma mu chiwonetsero cha Mzimu wa mphamvu.”

⁹⁴ Tsopano penyani! “Za chiyani, Paulo? Nchifukwa chiyani iwe ukuchita izi?”

Mphamvu! *Kuti chikhulupiriro chanu chisakhale mu nzeru za anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu.*

⁹⁵ Oh, mlaliki wotani! Munthu wamkulu uyu amene... Iye anamufunafuna Mulungu, ndipo anati, “Mulungu, ndine wofooka ndipo ine—ine sindikudziwa choti ndichite. Ine ndikungokupemphani Inu, Mulungu, kuti mundilimbikitse ine ndipo muchotse zofooka zanga kwa ine, ndi zinthu izi, kuti ine ndikhale wamphamvu.”

⁹⁶ Mulungu anayankhulanso momuyankha iye, anati, “Paulo, mphamvu Yanga imakhala yangwiro mu kufooka kwako.”

⁹⁷ Kenako Paulo anati, “Pamene ine ndiri wofooka ndiye ine ndimakhala wamphamvu. Inde!” Iye anati, “Ndiye ndidzatero... Ndidzazitamandira mu zolephera zanga za zifooko zanga ndi zina zotero. Ndikumuthokoza Mulungu kuti ndachotsa zonse mwa ine. Ndipo pamene ine nditulutsa chirichonse mwa ine, ndiye Mulungu akhoza kulowamo. Koma pokhapokha ngati ine ndiri ndi zina za inemwini mmenemo, ndiye Mulungu sangalowemo.”

⁹⁸ Pamenepo, ndi zimenezo, ife—ife timamubanikitsa Iye. Timamuthamangitsira kutali ndi zathu... Kuchokera kwa osauka a ife kufikira kwa olemera a ife, kuyambira wamng’ono kufikira kwa wamkulu, timamuthamangitsa Mulungu kuchoka mmoyo mwathu chifukwa cha ife eni.

⁹⁹ Nthawi zambiri ndimanena kuti, “Mdani wamkulu amene ine ndiri naye ndi William Branham.” Iyeyo ndi amene amakhala panjira ya Mulungu. Iyeyo ndi amene amakhala waulesi. Ndi iyeyo amene amafika pamalo amene nthawizina amaganiza kuti akhoza kuchitapo kanthu, ndipo, pamene iye atero, izo zimamukankhira Mulungu kunja kwa chithunzicho. Koma pamene ine ndimuchotsa munthu ameneyo, pamene ndifika pamalo amene iye wachoka pa njirapo, ndiye Mulungu akhoza kubwera ndi kudzachita zinthu zimene William Branham sakuzidziwa.

¹⁰⁰ Ndi pamene Mulungu akhoza kukugwiritsani inu ntchito. Ndi pamene Iye akhoza kumugwiritsa ntchito aliyense wa inu. Iye akhoza kumugwiritsa ntchito aliyense pamene tichoka panjirayo. Koma ngati tadziyika tokha panjirayo, ndiye ife sitingathe. Chabwino.

¹⁰¹ Tsopano ife tikupeza, munthu wamkulu uyu, Paulo, iye anali—iye anali kalonga pakati pa alaliki. Iye ankalemekezedwa ndi chipembedzo chirichonse. Munthu ameneyo akanatha kupita ku mzinda ndi kukakhala ndi msonkhano kulikonse. Chifukwa chiyani? Iye anali ndi zomuyenereza. Bwanji, iye anali wamkulu kwambiri, ndipo wotsimikizika kwambiri kuti aphwanye anthu onse amene anali ofooka, mpaka iye ankalandira mphamvu kuchokera kwa wansembe wamkulu, ulamuliro wapamwamba kwambiri, kuti amange mmodzi

aliyense wa Akhristu amenewo. Mphamvu zandale zochokera ku mpingo wake, kuti akawamange onse a iwo! Oh, iye anali wamphamvu! Iye amatha kumanga Akhristu ndi kuwaponya iwo mu ndende chifukwa iwo sankagwirizana ndi iye pa ziphunzitso zake za fioloje, pa ziphunzitso za Afarisi ndi Asaduki. Iye anali akuwamanga Akhristu.

¹⁰² Koma, zindikirani, iye ankayenera kuti akhale womangidwa, iyemwini, chotero kuti iye athe kutaya izo, iye akanakhoza kutaya mphamvu zake ndi ulamuliro. Iye anadzakhala womangidwa, iyemwini, kuti ataye chimene iye anali nacho mphamvu yomangira. Iye ankayenera kutaya chimene iye anali, kuti akhale womangidwa.

¹⁰³ Mulungu amawapitirira olemkezeka! Iye anawapitirira ansembe. Iye anawapitirira iwo amene anali odzitukumula. Ndipo Iye anasankha Paulo, munthu wankulu uyu, ndipo anamugwetsera iye mu fumbi la dziko lapansi ndi kumachita zinthu zimene iye . . . monga enawo ankachitira. Iye anawapanga iwo kuchita mwa . . . anamupangitsa kuti achite mofanana ndi amene ankawamangira. Iye anamumanga Paulo ndi Mzimu wa Mulungu, kuti akamumasule iye ku mphamvu imene iye anali nayo yomangira Akhristu. Ndiuzeni ine Mulungu samadziwa chimene Iye akuchita? Iye anachotsa mphamvu zake kuti ataye zake—kugwira kwake.

¹⁰⁴ Ndi atumiki angati amene Mulungu angawagwiritse ntchito mmawa uno ngati iwo atangomulola Mulungu awamange iwo ndi Mawu Ake ndi mphamvu yake, ndi kuwamasula iwo ku mphamvu ya zipembedzo zimenezo ndi mabungwe! Ndi anthu angati odzipereka mu mzinda uno, mmawa uno, amene amapita ku mipingo yayikulu ya bungwe iyi, ndi angati Iye angakhoze kuwadzaza ndi Mzimu Woyera, ndi kuyatsa dziko lino ndi Uthenga ndi mphamvu, ngati iwo atangotenga ndi kudzimasula okha ku mphamvu imene ali nayo ndi kumangidwa ndi Mzimu Wake, kukhala monga Paulo anali, kapolo wachikondi wa Mulungu!

¹⁰⁵ Mulungu anamutenga Paulo ndipo anamupanga iye kapolo, anamumanga iye kwa Iyemwini ndipo anamutumiza kwa Amitundu amene iye ankawada. Koma, inu mwaona, iye ankayenera kuti amasulidwe ku mphamvu yake yachipembedzo, kuti akamangidwe ku mphamvu ya Mulungu. Iye ankayenera kutaya mphamvu yake ndi kukhala wofooka wopanda kanthu, kuti alandire mphamvu ya Mulungu, kuti akakhale womangidwira kwa Mulungu, kuti azikachita chimene Mulungu angamuuze kuti achite.

¹⁰⁶ Ichi ndi chimene tikuyenera kuchita lero. Ndi chimene ine ndikuchifuna. Ichi ndi chimene munthu aliyense akuchisowa, ndi kudzitaya yekha, kutaya kuthekera kwake, kutaya chimene iye ali, kuti akhale ndi kudzipereka kwathunthu kwa Mzimu

Woyera. Mkazi wapanyumba akuchisowa chimenecho. Mwana wasukulu akuchisowa chimenecho. Ife timatenga . . . ngakhale ana athu aang'ono.

107 Mnyamata wina wamng'ono amene ine ndikumuganizira, dzulo masana kapena dzana, kapena tsiku lina, iye anadzalowa ndipo anamutenga mlongo wake wamkulu kuti alembe phunziro lake mwachangu, ndipo anatuluka ndipo anakawauza anyamata aang'onowo, anati, "Psyii! Mafunso amenewo anali ophweka." Mwaona, iwo amaphunzitsidwa, pafupifupi, kuti azinama.

108 Zikanakhala zabwino bwanji. . . Ndipo anthu amenewo ndi mizati mu mpingo. Zikanakhala zabwino bwanji kwa Adadi, mmawa pa nthawi ya kadzutsa, kunena, "John akulemba mayeso ake lero. O Mulungu, mukakhale ndi John! Mukamuthandize John! Iye anandifunsa ine mchipinda mmawa uno, anati, 'Adadi, mundipempherere ine lero, ine ndikuyenera kukumana ndi mayeso anga. Mundipempherere ine.'"

109 Ndingakonde mwana wanga atapeza—yabwino, yokongola "F" pa khadi lake, kuti walephera, kuposa momwe ndingakhali nditadziwa kuti wapeza "A" ndi kubera pa izo. Inde, bwana! Chimene tikusowa ndi kudzitaya tokha, kudalira kwathunthu mphamvu ya Mulungu.

110 Tsopano, "womangidwa." Mulungu amadutsa olemekeseka ndipo amatenga ofooka. Mulungu amawadutsa iwo amene amadziwona kuti ali chinachake, kukamutenga winawake amene sakudziwa kalikonse ku dongosolo kuti agwire ntchito Yake mmoyo wawo. Ndi chimene ife timapeza.

111 Mulungu ananena kwa Paulo, "Mphamvu yanga ndi yangwiro mu chifooko chako. Yanga—mphamvu yanga imakhala yangwiro mochuluka pamene iwe ukukhala wofooka kwambiri. Mukadzipereka kwa Ine mochuluka nditha kukugwiritsani ntchito bwino. Mukamaiwala mochuluka za maphunziro anu, ndi pamene mungaiwale mochuluka za chipembedzo chanu, mochuluka momwe mungaiwale za zinthu zanu ndi kudzipereka nokha kwa Ine, ndikhoza kukugwiritsani ntchito mochuluka. Chifukwa mumakhala ofooka, ine ndi—ndipanga cholinga Changa Changa kukhala champhamvu."

112 Mulungu akhoza kupanga mphamvu kuchokera mu kufooka! Ndi chifukwa chake Iye nthawizonse amachita zimenezo. Pamene Iye anasankha ophunzira ake, ndani akanaganiza. . .

113 Kudzichepetsa kwa Mwana Wake Yemwe pamene Iye anabadwa mu khola, mu khola la manyowa, mu khola la ng'ombe, ndipo anakulungidwa mu chovala chapagoli! Mwaona, Iye akanakhoza kubwera kudzera mu nyumba yachifumu. Iye akanakhoza kutsikira pansu mmakonde a Kumwamba, ndi zonse . . . ulemu wathunthu wa Mngelo. Koma Iye anasankha

kumupanga Khristu kukhala Chitsanzo cha ife, kwa ife, ndipo Iye anamubweretsa Iye mu kudzichepetsa.

¹¹⁴ Iye sanamuphunzitse konse Iye mu masukulu a mdziko lino, koma Iye anamuphunzitsa Iye ndi mphamvu Yake Yomwe, ku...kuti Iye athe kudzipereka Iyeyekha kwathunthu, osati ku malingaliro a munthu kapena mphamvu ya mdziko, koma kudzipereka Yekha ku mphamvu ya Mulungu.

¹¹⁵ Ndipo ndicho chimene ife tiri lero, ife timadzipereka tokha lero mu zipembedzo zathu zazikulu ndi madera. Ife timadzipereka tokha kwa chipembedzo, chimene icho chikuyenera kuti chinene, chimene *iwo* amanena pa izo. Koma zimenezo ndi zotsemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Ife tikuyenera kudzipereka tokha kwa Mzimu wa Mulungu ndi kupita kumene Mzimu wanena kuti tipite. Uko nkulondola.

¹¹⁶ Ahebri a Mulungu amene ife, kapena, asilikari a Mulungu, kani, “ngwazi.” Ife tangowerenga kumene mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 11 ndi ndime ya 34.

...*kuchokera mu zofooka analimbikitsidwa,...*

¹¹⁷ Iwo ankayenera kufooka asanakhale amphamvu. Kuchokera mu kufooka kwawoko iwo analimbikitsidwa. Inu amene mukulemba Malemba, kunja uko, Ahebri 11:34. Chabwino.

¹¹⁸ Apa pali chinachake chotitonthoza ife. Apa pali chinachake chimene chimalimbikitsa. Kuchokera mu kufooka ndi kudzichepetsa Mulungu amasankha anthu kuti amangepo Ufumu Wake. Ngati ife tidzakafike konse Kumwamba, ngati ife tidzakayime konse mu Kukhalapo kwa Mulungu ndi Mpingo Wake, ife tidzakaima mu gulu la anthu amene anakhala ali ofooka ndi okanidwa ndi otayidwira kunja ndi dziko, ndipo osadziwa kanthu.

¹¹⁹ Kodi sizodabwitsa kuti Mulungu anatifanizitsa ife ndi nkhusa? Nkhusa ndi chinthu chosatha kudzithandiza chimene chiripo. Palibe chimene chiribe chitetezo chokwanira kuposa nkhusa. Kalulu amatha kuthamanga; gologolo akhoza kukwera mu mtengo; galu akhoza kuluma; mkango ukhoza kung’amba; kavalo akhoza kumenya; mbalame ikhoza kuwuluka; koma nkhusa imaima yosatha kudzithandiza.

¹²⁰ Ndipo umo ndi momwe Mulungu amatifunira ife. Kuzindikirani kuti ndife osakwanira kwathunthu, ndiye Mulungu amamutenga munthu ameneyo ndi kuyamba kudziwumba Yekha mwa munthu ameneyo; kupanga manja ake kuchita chimene Mulungu akanakhala ndi manja akanachita, kupanga milomo yake kuyankhula chimene milomo ya Mulungu ikanadzayankhula; chifukwa si ake, iwo ndi a Mulungu. Iye amayamba kumanga khalidwe, amayamba kutenga kufooka uku ndi kudzipereka Iyeyo Mwiniyekha.

121 Iye amatibweretsa ife kuno pa dziko lapansi, kwa pamenepo...Ndife ophunzitsidwa, ndife anzeru. Kodi inu munayamba mwazindikirapo mizere, timibadwo? Pamene ife titenga, mwachitsanzo, monga mwa Abele, kuchokera kwa Abele kunabwera Seti; Kam'badwo ka Seti kanadzabwera mmusi momwe, mpaka ku nthawi ya Nowa, onse a iwo anali alimi odzichepetsa chabe. Koma ana a Kaini anali anzeru, ochenjera, ophunzira, amuna aakulu, omanga, akatswiri achimuna.

122 Koma mbali ya Mulungu anali ofooka ndi odzichepetsa. Umo ndi momwe Mulungu ankawagwiritsira ntchito iwo. Umenewo ndi mwayi wa Mulungu. Ndiyo njira ya Mulungu yofikira kwa ife, ndi pamene ife tafooka. Ife timapeza chinachake ndiye. Izi zimalimbikitsa, ndithudi, chifukwa Ufumu wonse wa Mulungu unamangidwa kuchokera mwa anthu otere. Ndiye pamene inu mufika ku njira ya mtundu umenewo ndiye inu—inu mukhoza. . .inu muli mu Ufumu Wake.

123 Nkhaniyo ndi yakuti, ndi ife, kuti. . .osati kuti ndife ofooka kwambiri, nkhani ndi yakuti ife ndi amphamvu kwambiri. Ndife—ndife—ndife amphamvu kwambiri basi. Ndizo zonse. Chinthu chake ndi chakuti ndife ammutu kwambiri. Ndiko kulondola, ndife amphamvu kwambiri mmutu mwathu. Ife timadziwa zochuluka. Mulungu amafuna kuti achotse izo mwa ife. Uko nkulondola. Ndife amphamvu kwambiri, ndife amphamvu kwambiri kuti tidzipereke kwa Iye. Ife tiri. . .Ife—if timadzipereka kwa ifeeni. Ife tikuyenera kuganiza, “Chabwino, tsopano, apa, ine—ndiri ndi nzeru zokwanira kuti ndidziwe!”

124 Ine ndinadabwitsidwa mausiku angapo apitawo pamene amayi ankadwala, uko ku chipatala. Ndinapita ku. . .Panali dona wamng'ono pafupi ndi chitseko. . .Ngati dona wamng'ono ameneyo ali pano, inu mundikhululukire ine, mlongo. Iye ndi mtsikana wamng'ono waku Kentucky wochokera kumusi uko, ndipo ife tinali. . .ndipo amenewo anali apongozi ake aakazi. Ndipo ndinali kuyankhula ndi iye usiku umenewo, mkazanga ndi ine, kumeneko pafupifupi wani koloko mmawa. Ndipo mwamuna wake anali atagona pansu ndipo anapita kukagona; iye anati, “Choka muno! Iwe siwabwino kwa amayi ako, mulimonse.” Ndipo anamuthamangitsa iye, mwamuna wake, kutuluka mchipindamo, chifukwa iye anali atagona molunjika pa chitseko kumene anamwino, palibe amene akanakhoza kulowamo; akungoliza nkonono, pansu. Chotero iye anamudzutsa iye ndi kumuthamangitsira iye panja.

125 Ndipo iye anayamba kuyankhula pamenepo. Ine ndinayamba kuyankhula ndi iye za Ambuye, ndi zina zotero. Ndipo anati, “Chabwino,” iye anati, “zonse zimene ine ndimadziwa zinali khasu mu chigamba cha fodya, mmawa molawirira, kudula udzu ndi kuchisa fodya, ndi zina zotero monga choncho.” Anati, “Koma, ndikukuzani inu,” anati,

“abambo anatitumiza ife, aliyense, ku sukulu.” Ndipo anati, “Ife tiribe kukhudza.”

Ine ndinaganiza, “Chabwino, mwinamwake ndi chifukwa chake.”

¹²⁶ Mwaona, inu—inu mukuyenera kuti mutalikirane ndi zinthu za mdziko. Tsopano, sindikuthandizira umbuli, ayi—si choncho, koma ine ndikuyesera kuganiza ukafika pamalo amene ukuganiza kuti umango—umangodziwa zambiri mpaka palibe wina akudziwa kalikonse za izo. Kudziwa kwako nkwabwino bola ngati si—ngati sikusokonezana ndi malonjezano a Mulungu.

¹²⁷ Ife timalamuliridwa ndi zokhudzira zisanu, ndipo zokhudzira zisanu zimenezo (kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva) ndi zabwino kwambiri mpaka izo zitasokoneza chokhudzira cha Chikhulupiriro. Ndiye pamene izo zibwera motsutsana ndi Chikhulupiriro... Ndipo mumadziwa bwanji amene ali wolondola? Chifukwa Chikhulupiriro nthawizonse chimagwirizana ndi Mawu. Ndiyeno ngati—ngati chikhulupiriro chako chikutsutsana ndi Mawu, kapena iwe ukuganiza kuti icho chiri, ndiye kuti iwe ulibe Chikhulupiriro. Iwe uli ndi chikhulupiriro chodzipangitsa. Uli ndi kudzitamandira mu zokhudzira zakozo, pa maphunziro ena amene iwe unaphunzirapo, kapena chinachake. Koma pamene iwe uchoka kwa izo ndi kudalira kwathunthu pa Chikhulupiriro, ndipo Chikhulupiriro chitha kokha kumangidwa pa Mawu a Mulungu (Chikhulupiriro cholondola).

¹²⁸ Dokotala nthawiina anandiuza ine, anati, “Ine ndikukhulupirira, Billy, ngati anthu amenewo...ngati ungawawuze iwo kuti apite kunjira kumeneko ndi kukagwira mtsanamira imeneyo, mtengo umenewo, ndipo iwo nkukhulupirira kuti iwo achira, iwo akhoza kukachira chimodzimodzi basi.”

¹²⁹ Ine ndinati, “Ayi, bwana. Izo sizingatero, adokotala, chifukwa cha chinthu chimodzi ichi, mwaona, anthu amenewo akudziwa kuti iyo ndi nsanamira chabe. Iwo amadziwa kuti palibe ukoma kapena mphamvu mu nsanamira imeneyo.”

¹³⁰ Koma munthu aliyense amene ndi wokhazikika mmalingaliro angadziwe kuti amenewo ndi Mawu a Mulungu wamoyo, kuti ine ndikhoza kukhazikitsa chikhulupiriro changa pa izo ndi kudziwa kuti Iwo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! Ndipo ngati chirichonse chiri chotsutsana ndi Iwo, ndiye ine sindimakhulupirira zokhudzira zanga. Ayi, bwana, ndimangozisiya izo zokha. Muziyenda ndi chokhudzira chanu china, chokhudzira cha Chikhulupiriro.

¹³¹ Chabwino, Mulungu amawatenga anthu amenewo kuti achite...Pamene iwo ali osadziwika, iwo amadzipereka kwa Iye.

¹³² D. L. Moody waku Chicago, iye anali waku Boston, iye anali wosoka nsapato; munthu wamng'ono, wochepa, wosakwanira, sankadzidalira yekha. Tsopano, inu mutenge masukulu opambana awa amene iwo ali nawo, Sukulu ya Moody kumtunda uko, ngati Dwight Moody akanadzuka kachiwiri ndi kuwona sukulu imeneyo, chinthu choyambirira chimene Dwight Moody angachite ndi kuchotsa sukulu imeneyo.

¹³³ Ngati Martin Luther akanawuka, chinthu choyambirira chimene iye akanachita ndi kuchotsa bungwe la Chilutera. John Wesley angadzachite chimodzimidzi. Amuna amenewo sanayambitse konse mabungwe amenewo, anali amuna amene ankawatsatira iwo, amene ankachita zimenezo.

¹³⁴ Paulo sanawupange mpingo bungwe nkome, chifukwa iye anati, iyemwini, “Ndikadzachoka ine, anthu a mu khamu lanu lomwe adzawuka pakati panu, akuyankhula zinthu zopotoka.” Zinali pambuyo pa imfa ya Paulo, ndipo zaka handirede (kapena ziwiri) zitatha izi, kuti iwo anapanga mpingo wa Katolika, bungwe loyamba.

¹³⁵ Amuna anadzuka! Zinali pambuyo pa imfa ya Moody kuti iwo anali ndi Sukulu ya Moody; pambuyo pa imfa ya Wesley kuti iwo anadzapanga mpingo wa Wesley; pambuyo pa imfa ya Luther kuti iwo anadzapanga mpingo wa Luther. Mulungu amatumiza ngwazi; ndipo iwo amamanga . . .

¹³⁶ Nzosadabwitsa Yesu anati, “Inu—inu makoma oyeretsedwa!” Iye anati, “Inu—inu mumakongoletsa manda a aneneri, ndipo inu ndi amene munawayika iwo mmenemo!” Uko nkulondola.

¹³⁷ Amuna aakulu awa amawuka; kenako iwo amawamangira iwo chikumbutso. Ine ndikuganiza, chimodzimidzi monga David, “Anatumikira Mulungu bwino mu kam'badwo kake.” Chotero ndiyo njira yake yochitira izo. Mulole mabungwe ndi zinthu kumeneko, zimene, zikhale kutali ndi inu.

¹³⁸ Moody, wokonza nsapato wamng'ono wakale, iye anali wofooka. Iye anali chitsanzo cha kufooka. Chinthu choyambirira chimene chimanenedwa chimene Moody anachita . . . Iye analibe maphunziro nkome, ndipo galamala yake inali yoipa kwambiri inali yowopsya. Munthu anabwera kwa iye nthawi ina ndipo anati, “Bambo Moody,” anati, “galamala yanu ndi yoyipa kwambiri imene ndinayamba ndaimvapo mmoyo wanga.”

¹³⁹ Iye anati, “Ndikupindula miyoyo ndi umbuli wanga, iwe umachita nawo chiyani maphunziro akowo?” Ine ndikuganiza kuti limenelo linali yankho labwino. Ndithudi linali!

¹⁴⁰ Ndipo tsopano, iwe ukakhala membala wa Sukulu imeneyo, iwe ndithudi ukuyenera kukhala wophunzira wopukutidwa. Uko nkulondola. [M'bale akuti, “Angochisintha icho!”—Mkonzi]. Tsopano, eya, iwo “anasintha icho” ndi kulondola, kubwerera njira inayo.

¹⁴¹ Ndi zomwe anthu amachita. Pamene ndinanena kumayambiriro kwa uthenga wanga...Mmalo mwa Akhristu kudzichepetsa okha ndi kudzipatula okha kuti apeze malo ochulukirapo a Mulungu, iwo amayesetsa kudzimangira okha mu chidziwitso chopangidwa kunyumba, kapena chidziwitso cha sukulu yaukadaulo, kapena chinachake, chimene chimawathamangitsira iwo kutali ndi Mulungu kuposa momwe iwo analiri pamene iwo ankayamba.

¹⁴² Ndicho chimene ine ndikuganiza za maitanidwe aguwa ochita kupanga awa. Inu mukamubweretsa iye, ndipo nthawi yotsatira zidzakhala zovuta kateni kuti mumubwezeretse iye. Musiyeni iye akhale ndi kumamvetsera mpaka Mulungu atamuchitira chinachake! Ndipo kenako muloleni iye abwere ndi kudzachivomereza icho, ndi kuwuka, akuyitanira pa Dzina la Ambuye. Izo nzoona.

¹⁴³ Zindikirani Moody, wofooka mu maphunziro, wofooka mu kuyankhula, iye ankallira miluzi m'mphuno mwake. Ine ndimangowerenga mbiri yake tsiku lina, "Kulira miluzi m'mphuno mwake, matenda a mphuno." Wowoneka wamng'ono, mwamuna wadazi, ndevu zikulendewera pansi...?. . .; munthu wamng'ono, wochepa, wamfupi. Mwachupi, iye anali wosweka mwathupi. Chotero iye analibe kalikonse koma kufooka kopitirira. Koma Mulungu anamugwiritsa iye ntchito kuti aligwedezze dziko mu tsiku lake!

¹⁴⁴ Nthawi ina panali mtolankhani anapita ku msonkhano wake (ine ndinkawerenga), ndi atolankhani, kuti apange lipoti pa mtundu wanji wa munthu umene uyu anali (munthu wamkulu, mwamuna wamkulu).

¹⁴⁵ Kodi switchi yaing'ono ija ili pati imene mumazimitsira matepi? Ndi iyi? Ine ndikuyenera kungoiyimitsa iyo pamene.

¹⁴⁶ A—mwamuna wamkulu, Moody anali. Iye anali mwamuna wabwino. Ndipo chotero iye anakakopa chidwi cha anthu, ankawasiya iwo ali kakasi. Chotero apo panali mtolankhani anapita kwa Bambo Moody ndipo anati...anapita ku msonkhano kukapanga lipoti pa mtundu wa kumanga kwakukulu... .

¹⁴⁷ Monga mtolankhani anangopita ndi kukanena za mvangeri wina wamkulu, posachedwapa, anati, "Munthu ameneyo ndi woyankhula bwino. Iye ndi Dokotala wa Zauzimu. Amagwiritsa ntchito galamala yabwino kwambiri imene ine ndinainmvapo. Iye amawagwira anthu mu kuwerenga maganizo kwake. Iye akhoza kuwapangitsa anthu kakasi."

¹⁴⁸ "Dwight Moody," pamene mtolankhani anapita, anati, "Ine sindikuwona chimene chiri mwa iye chimene chiri chokopa kwa aliyense." Anati, "Chinthu choyamba, iye ndi wonyansa monga iye angakhalire. Chinthu chotsatira, iye ndi wotheratu mwathupi. Chinthu chotsatira" iye anati "iye ali,

iyе alibe maphunziro. Galamala yake ndi yoipa kwambiri imene ndinaimvapo!” Ndipo anati, “Amakhala a kuliza miluzi komanso kupuma befu pamene akulalikira.” Ndipo anati, “Ine sindimawona chirichonse mwa Dwight Moody chimene chingakope chidwi cha aliyense.”

¹⁴⁹ Bambo Moody anabweretseredwa nkhaniyo. Iye anaiwerenga iyo, anachita ngati yamuseketsa, anati, “Ndithudi ayi; ndi Mulungu. Ndithudi! Anthu samabwera kudzamuwona Dwight Moody, amabwera kudzamuwona Mulungu.”

¹⁵⁰ Anthu sasamala kuti mumachitira umboni mochuluka bwanji, iwo amafuna chenicheni china mmoyo mwanu chimene chimatsimikizira kuti Mulungu wakugwirani inu. Inu mukhale wa Methodisti, Baptisti, Pentekoste, chirichonse chimene inu mungakhale, iwo akufuna kumuwona Mulungu. Uko nkulondola, anthu a . . . anthu otchuka, anthu amene ali ofooka ndi ozindikira kufooka kwawo.

¹⁵¹ Tayang’anani pa Mose, mwamuna wamng’ono waluntha. Oh, iye anali sikolala. Iye anali wophunzitsidwa kwambiri mu nzeru zonse za Aigupto mpaka iye ankakhoza kuwaphunzitsa Ahebri. Iye ankakhoza kuwaphunzitsa Aigupto. Iye ankakhoza kumuphunzitsa aliyense, chifukwa Mose anali munthu wamkulu, munthu wanzeru. Oh, iye anali munthu wamphamvu.

¹⁵² Mu lingaliro la Cecil DeMille la izo, pamene—pamene anapanga *Malamulo Khumi* kuti iseweredwe, ndipo iye anamubweretsa munthu uyu amene analipo. . . Ine ndaiwala dzina la munthu amene anachita gawo la Mose mmenemo, wosewera wina, koma munthu wamkulu wokhala ndi manja aakulu ndi mphamvu. Ndipo Mose mwina anali munthu wotero.

¹⁵³ Iye tikudziwa kuti iye anali wamphamvu komanso wophunzitsidwa bwino, chotero anadzitengera yekha, powona chosowa cha tsikulo. (Oh, Mulungu alole kuti izi zimire mpaka mkati!) Powona chosowa cha tsikulo, Mose ndi mphamvu zake za luntha ndi kuthekera kwake kumene ankayenera kuchita nako. . . Iye anali munthu wanzeru. Iye anali Farao wakudza. Iye anali ndi kuwerenga maganizo. Iye anali—iye anali ndi mphamvu. Anali ndi mphamvu zakuthupi. Iye anali—iye anali ndi chirichonse. Chotero iye anati, “Ndiri ndi zida. Ine ndikudziwa zonse za izo. Ndipo ngati pali mwamuna mdziko amene angathe kuchita izo, ndi ineyo. Chotero, ndine munthu wa orali chotero nditulukira.” Ndipo iye anapita kukakwaniritsa ntchito imene inali yolondola ndiponso mu chifuniro cha Mulungu, ndipo iye anapereka luso lake lachibadwa. Ndipo Mulungu anazikana izo! Iye sakanakhoza kugwiritsa ntchito chinthu chimodzi chimene Mose anali nacho.

¹⁵⁴ Iye sakanakhoza kugwiritsa ntchito icho apo, kapena Iye. . . ngakhalenso Iye sangakhoze kugwiritsa ntchito icho tsopano. Mulungu sangagwiritse ntchito kuthekera kwathu

kwachibadwa. Ife tikuyenera kudzichotsa tokha ndi kuthekera kwathu panjira, ndi kudzipereka ku chifuniro ndi mphamvu ya Mulungu.

¹⁵⁵ Kuti, “Chabwino, m’bale, ine ndikhoza kulalikirira.” Iye sangagwiritse ntchito izo bola ngati *inu* mungathe kulalikirira. “Izo ziri bwino, ine ndikhoza kuchita *ichi*, ine ndikhoza kuchita *icho*.” Simungathe kuchita chirichonse. Chabwino, ndiye Mulungu sangathe kugwiritsa ntchito icho. Koma ngati mungadzipereke nokha kwa Mulungu ndi kumulola Iye kuti achite izo!

¹⁵⁶ Inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, ine ndikudziwa. Ndine mphunzitsi.” Chabwino, bola ngati *inu muli* mphunzitsi, bwanji, Iye safika patali kwambiri. Koma Mzimu Woyera ndiye Mphunzitsi wathu. Ndithudi, Iwo uli! Mulungu anatomiza Mzimu Woyera kuti udzakhale Mphunzitsi pa Mpingo.

¹⁵⁷ Anthu ena amapita ku sukulu kwa zaka ndi zaka ndi zaka. Kodi iwo amachita chiyani? Amakawerenga zolemba kuchokera mu Chipinda Chapamwamba, ndipo chotero (oh, izo nzabwino) mumatenga phunziro la Sande sukulu ya Fuko. Ine ndiribe kanthu kotsutsa izo. Amenewo ndi Mawu a Mulungu, ndi zinthu, koma izo zimayikidwa pamodzi ndi aluntha! Izo zikuyenera kubwera mwa mphamvu ndi chiwukitsiro cha Khristu, ndipo inu simungadalire pa luso lanu lachibadwa.

¹⁵⁸ Chotero, Mose, chimphona chaching’ono ichi, chabwino champhamvu, munthu waluntha, iye anyanyamuka kukachita ntchito yabwino; koma Mulungu mophweka, mwamtheradi sakanatha kugwiritsa ntchito izo. Iye sakanagwiritsa ntchito kuthekera kwake kwachibadwa.

¹⁵⁹ Ndipo ife sitingathe...Si lero, kuti ife sitingathe... Mulungu sangagwiritse ntchito kuthekera kwathu kwachibadwa.

¹⁶⁰ Koma pali chinthu chimodzi chimene Mose anali nacho chimene ndimachisilira, anali ndi nzeru zokwanira kudziwa kuti anagonjetsedwa. Ife tiribe. Ndizo zonse. “Ife timapanga chipembedzo *chatsopano*. Ife timapeza winawake wokhala ndi mphatso ya machiritso, kapena chinachake,” Achipentekoste, inu mwaona. Mukuona? Ife—ife sitimadziwa mokwanira basi kuti tizindikire kuti tagonjetsedwa. Mpingo wa Chipentekoste, Assemblies of God, United, ina yonseyo, zikuwoneka ngati alibe kuthekera kodziwa kuti agonjetsedwa. Aleluya! Oh, ine ndikanakonda ndikanazipanga izi kumamatira. Iwo agonjetsedwa. Bungwe la mpingo lagonjetsedwa! Chimodzimodzi basi monga United States uyu wagonjetsedwa, akunjenjemera ndi mantha, ndipo mabomba akulendewera uko kwa iwo, iwo akudziwa kuti anachoka ndipo akulowetsa moyo wawo ku gehena. Ndipo iwo agonjetsedwa, Mzimu unatuluka mwa iwo. Umayenera kusaladza mitengo kuti utengere

anyamata kunkhondo; iwo anawona zimene zinachitika mu inayo. Ife tagonjetsedwa! Mpingo wagonjetsedwa. Iwo akudziwa zimenezo.

¹⁶¹ Mose anazindikira zimenezo, ndiye iye anadziwa mokwanira ndiye... Mulungu anamutengera iye mmbuyo kuseri, mu chipululu, kuti akamuphunzitse iye zofooka zina zaumunthu. Iye anamutengera iye kuti akamuphunzitse chimene icho chinali. Anaphunzira bwino kwambiri! Oh, mai, kodi iye anayamba wapezapo phunziro! Mulungu akuyenera kuti anali ndi nthawi ndi iye kumbuyo uko! Inu mukudziwa, Mose anali ndi kupsya mtima; ndipo Mulungu anamupatsa iye mkazi dzina lake Zipporah, iye anali nako, nayenso. Chotero ine ndikuganiza kuti chirichonse sichinali chosangalatsa kumbuyo kwa chipululu kwa kanthawi, pamene kupsya mtima kwawo konse kunasiya kuwugwira mtima nthawi imodzi.

¹⁶² Ine ndikuganiza kuti lingaliro lake laluntha la momwe kuwerenga malingaliro kukuyenera kumulamula munthu silinachite zabwino zochulukana, chifukwa, pamene iye anali pa ulendo wake waku Igupto, ine ndikumuwona Zipporah akadali ndi kupsya mtima. Iye anadula khungu la mwana wake wamwamuna ndipo analiponyera ilo pamaso pa Mose, anati, “Ndiwe mwamuna wamagazi kwa ine.”

¹⁶³ Ndipo Mulungu anamukwiwira iye kwambiri Iye... anakamusaka iye mnyumba ya alendo, ngati Iye akanamupeza Iye akanamupha. Ine ndikuganiza panali zinthu zazing’ono zimene Mulungu ankayenera kuti amuphunzitse iye kumbuyo uko, mwaona, kuti iye anali munthu. Nzeru zake zonse za ku Igupto ndi mphamvu zake zonse za luntha, Mulungu sakanakhoza kugwiritsa ntchito imodzi ya izo.

¹⁶⁴ Inu mubwere, ndikuti, “Tsopano, Ambuye, ine ndaphunzitsidwa kwa zaka forte tsopano, ndine a—ndine wophunzira waluntha. Ine ndikhoza kuwerenga mobwereza Baibulo limenelo ndi maso anga otseka.” Mulungu sangagwiritse ntchito pang’ono za izo. Mukuona? Ayi.

¹⁶⁵ “Oh, ine ndi wa mpingo wawukulu kwambiri umene ulipo mdziko. Ine—ine ndine... Ndine *ichi*, Ambuye. Oh, ndine wa Pentekoste. Ine... Ulemelero kwa Mulungu! Ine ndangolandira kumene Mzimu Woyera usiku wina. Aleluya! Inu mundipangitsa ine kuchita *chakuti-ndi-chakuti*.” Mulungu sangagwiritse ntchito kalikonse ka izo. Ayi!

¹⁶⁶ Nthawizonse mukagonjetsedwa ndi kuzindikira kuti mwagonjetsedwa, ndipo kenako bwererani ndipo mudzadzichepetse nokha. Khalani ofooka, mudziwe kuti ndinu munthu. Ndipo palibe waluntha wanu amene angachite kwa... Zofooka zaumunthu sizidzagwiritsidwa ntchito konse ndi Mulungu; Mulungu mwa zofooka zaumunthu amadzitsanulira Yekha mwa inu, kenako Iye amadzigwiritsa ntchito Yekha. Inu

mumangokhala chida. Ndithudi! Inu mukuyenera kudzichotsa nokha panjirapo.

¹⁶⁷ Mose, oh, iye anaphunzira, iye anaphunzira zofooka za umunthu mwabwino kwenikweni. Iye anaphunzira izo mwabwino kwambiri, mpaka, pamene Mulungu anamuitana iye, iye anali ndi zofooka zisanu ndi ziwiri zimene iye akanakhoza kutsutsana ndi kuyitana kwa Mulungu. Kodi inu munayamba mwaphunzirapo mu gawo loyamba la Eksodo, zofooka zisanu ndi ziwiri? Ine—ine ndazilemba izo apa. Ndikufuna kuti mumvetsere kwa izo. Chofooka choyamba chimene anali nacho chinali kusowa kwa uthenga. Chofooka chachiwiri chimene anali nacho chinali kusowa ulamuliro. Chofooka chachitatu chimene anali nacho chinali kusayankhula bwino. Chachinayi chinali kusintha. Chachisanu chinali kupambana. Ndipo chachisanu ndi chimodzi chinali kuvomereza.

¹⁶⁸ Tsopano, inu mufanizitse zanu ndi zake ndipo muwone ngati inu mungabwere ndi izo, muwone ngati inu mungakhoze kukhala wofooka monga iye anali. “Ambuye, ine—ine si wabwino. Sindingathe kuyankhula. Ine—ine—ine ndinapha munthu wa ku Igupto. Sindingathe kubwererako. Oh, chirichonse! Sakandilandirako ine. Ndiribe uthenga. Ine ndiri . . . sindimatha kuyankhula. Ndipo ndine—ndine wochedwa poyankhula.” Ndipo mukuona momwe iye analiri? Iye sanali kanthu! M’bale, iye anali atachiritsidwa. Eya, Mulungu akanakhoza kumugwiritsa ntchito iye atachiritsidwa. Mukuona? Eya.

¹⁶⁹ Ndizo . . . Iye akhoza kutigwiritsa ife ntchito titatha kuchira, kupeza kuti “Ph.D yanga. ndi LL.D. ndi awiri ma L.D.,” kapena chirichonse chimene chingakhale, “madigiri anga onse si kanthu.” Mulungu sangakhoze kuwagwiritsa iwo ntchito!

¹⁷⁰ “Chabwino, ndine wa Assembly of God. Ndine wa Oneness. Ndine wa Baptisti. Ndine wa Presbateria.” Mulungu sangagwiritse ntchito mpang’ono pomwe za izo! Mukachokako mwachangu kwa izo, chabwino, kwabwinoko inu—inu—mungadzipereke nokha kwa Mulungu.

¹⁷¹ Monga mneneri anali, anati, “Ndine munthu wa milomo yodetsedwa, ndipo pakati pa anthu odetsedwa.” Ndipo Mngelo anapita ndipo anakatenga—zopanira, ndipo anakwera kupita ku guwa la nsembe ndipo anakatenga khala la moto ndipo anakakhudza milomo yake. Kenako anafuula kuti, “Ambuye, ndiri pano; nditumeni ine.” Eya, atazindikira kuti iye . . . Komabe pokhala mneneri, iye anali ndi milomo yodetsedwa.

¹⁷² Mwamsanga pamene ife tingazindikire kuti ife tiri—sitiri kanthu, kuti ndinu chabe, ndinu fumbi la dziko lapansi . . . Mulungu sangakhoze kukugwiritsani ntchito . . . Inde, chanu chokuchiti- . . . Zofooka zanu zonse sizingafanane ndi Mose.

Iye anali ndi zofooka sikisi zosiyanasiyana apa, ndipo anali ataphunzira kufooka kwaumunthu.

¹⁷³ Tsopano tayang'anani pa kusiyana pakati pa Mose *ameneyo* akukumana ndi Mulungu, ndipo Mose akuyang'ana pa...?... monga lero. Anati, "Titi, ife tikusowa *chakuti-ndi-chakuti!* Ife tikusowa chitsitsimutso mdziko. Ine ndikuuzani chimene nditi ndichite, ndikubwerera ndi kukaphunzira mpaka nditapeza Bachelor of Art yanga. Uh-huh! Ndikubwereranso ndipo ndikaphunzira mpaka nditadzedwa kukhala ndi LL.D. Ndikupita kukaphunzira zowerenga. Ine ndikachita zonsezi, ndikatero ndituluka ndipo ndikakhala 'mwamuna wa orali.' Ine ndikawapatsa befu anyamata onse awa amene anyamba kunjja kuno." (Oh, m'bale!) "Ndikadzipezera nyumba ya madola firii milioni. Ndidzipezera ma cadillac thwelofu. Ndipo..." Oh, m'bale! Inu mukhoza—inu mwina mukhoza osayamba, chifukwa inu munagonjetsedwa kuyamba ndi kuyamba, inu mwaona. Koma vuto lake ndi lakuti iwo sakudziwa izo!

¹⁷⁴ Iwo amaganiza kuti ukuyenera kukhala ndi tsitsi lopiringizika ndi kuvala suti za tuxedo ndikuti "ah-munthu" ukukongola kwambiri, ndi zonse monga chonchi, ndi kukhala kalonga. Ameneyo ndi chidole cha mkazi!

Mulungu akufuna amuna, amuna aumulungu, amuna amene angagweze!

¹⁷⁵ Koma lero tikufuna Hollywood. Ife tikufuna chinachake chimene—chimene chiri chosiririka mmaso. Ife tikufuna chinachake chimene chingayankhule mwanzero moti iye akhoza kutilola ife kugona kwa mphindi zisanu pamene iye... Lamlungu mmawa.

¹⁷⁶ Mulungu akufuna olekanitsa amene angamutumize iye ngati mphezi, kutsutsa tchimo mpaka ku mizu, (ndiko kulondola) kulikumba ilo.

¹⁷⁷ Koma ife tiri... Ife timafuna azibusa athu aluntha. Anthu ambiri amafuna m'busa wonong'ona, winawake wakuti, "Inde, wokonedwa."

Mulungu amafuna mabingu! Inde, bwana.

¹⁷⁸ Kuwasisita iwo pa nsana, ndi tsitsi lalifupi ilo ndi zozipenta, ndi china chirichonse, ndi kumavala zovala zimene iwo anatsanuliridwamo, ndi zonse monga choncho, ndipo osanena liwu pa izo.

¹⁷⁹ Munthu wamkulu anandiyitanira mu ofesi yake kuno, (osati ofesi yake) ofesi yake ya kumunda, kuno osati kale litali, anati, "Ndikufuna ndiyike manja pa inu kuti musiyeye zimenezo!"

Ine ndinati, "Usachite zimenezo. Usachite zimenezo. Ayi, bwana."

¹⁸⁰ Pamene inu muyimitsa izo, inu mumayimitsa Uthenga. Inu mumamuimitsa Mulungu pamene muchita zimenezo. Inde, bwana. Ife sitikufuna kalikonse ka izo.

¹⁸¹ Kodi Mulungu anamumvera chisoni Mose ndi zofooka zake zonse, anati, “Mose wamng’ono wosauka, chinachake—chinachake ndithudi chachitika kwa iwe, iwe unagwa kuchokera ku digirii yako. Oh, mai! Apa, eya, iwe unali munthu wamkulu, waluntha, ndipo panalibe chirichonse choti chikulepheretse iwe. M’bale, inu munali ndi ma Ph.D. anu onse ndi ma LL.D., ndi china chirichonse, ndipo tsopano apa iwe wabwera ukuvomereza kuti si iwe kanthu, sungathe kuchita kanthu. Ndiwe—ndiwe wofooka basi”? Ayi! Mulungu sanamumvere iye chisoni. Mulungu sanamuchitire chifundo iye. Mulungu anamuchiritsa iye ku zinthu zonsezo. Iye analibe chisoni kwa iye.

¹⁸² Koma ife tikupeza, ngati inu mukulemba izo, Eksodo 4:14, “Mkwiyo wa Mulungu unayakira pa iye.” Mulungu sanamuchitire chisoni iye chifukwa iye anali wofooka.

¹⁸³ Inu mukuti, “O Ambuye, ndikungomverera moyipa kwambiri, sindikukhulupirira kuti ndingathe kuchita zimenezo.” Mulungu samakumverani chisoni; amamverera ngati akumenyeni mozungulira pang’ono. Mukuona? Mukuona? Ndithudi. Mulungu samakumverani chisoni; Iye—Iye amakugwiwirani inu. Inu mukungofika powumbidwa ndiye pamene Iye angathe kukugwiritsani inu ntchito. Eya.

¹⁸⁴ Mose anali akufika pamenepo, Mulungu akanakhoza kumugwiritsa iye ntchito. Iye anali atacha, iye anali kutali ndi kuthekera kwa umunthu pamenepo. Iye analibe chirichonse chimene akanadalira pamenepo, chifukwa iye—iye anali wokonzeka ndiye ku utumiki.

¹⁸⁵ Mulungu anati, “Zaka forte kunja kuno ine ndakhala ndi iwe ndi Zipporah kumakangana ndi kumangoyendayenda kunja kuno mu chipululu muno, kaya iwe ukanapeza kuti pali kufooka kwaumunthu kapena ayi, pamene waima pamenepo ngati kalonga wamkulu, ‘Moni, Dokotala Moses. Mmawa wabwino, M’busa, Bwana. Inde, bwana. Mose, ndiwe kalonga wakudza. Zonse...Tonse timakuganizira iwe.’ Tsopano iwe uli kunja kuno mu chipululu ndi gulu la nkhoa ndi mkazi wopsya mtima.” Mukuona? Izo zinamukonza iye. Inde, bwana. Mose ali mmawonekedwe oyipa, koma Iye anati, “Tsopano ndikhoza kukugwiritsa iwe ntchito, pamene uzindikira kuti sindiwe kanthu. Tsopano bwera kuno pa chitsamba choyaka ichi, Ine ndikufuna ndikutume iwe kumusi uko.” Oh, mai!

¹⁸⁶ Mulungu, tipatseni ife zochuluka zina za mtundu umenewo, tipatseni ife zofooka zinanso. Ndi zimene ife tikuzisowa, zofooka zina. Ndithudi!

¹⁸⁷ Anali Yakobo, inu mukudziwa. Yakobo ankaganiza kuti anali munthu wamkulu nthawi ina, inu mukudziwa,

amatha kunama ndi kumapitirira ndi chirichonse. Anapita ndipo anakayika timitengo ta msondodzi mmene nkhosa ndi ng'ombe za apongozi ake pamene izo zinali ndi pakati, ndipo anazisandutsa izo kukhala nkhosa zamadonthomadontho, ndi kuziponya monga choncho pamene izo zinkapita ku madzi kuti zikamwe. Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, Yakobo anadzakhala munthu wamkulu. Ndithudi. Iye anali a . . . “Iye kwenikweni ankatchedwa *Yakobo*, osalakwitsa,” Esau anati, “Iye anali ‘wolanda’ chabwino.” Chotero iye anali wachinyengo. Iye ankachita bwino, amapeza, anali ndi ziweto zochulukana ndi akazi ndi nkhosa ndi ng'ombe, ndi ng'ombe za ngolo, ndi—ndi chirichonse, iye anali ndi chirichonse.

¹⁸⁸ Koma usiku wina (oh, mai!) pamene iye anafika ku kamtsinje kakang'ono nthawi ina, anali woti awoloke, iye anafika pa malo amene Mngelo anamugwira iye. M'bale, Yakobo wakale anakhala usiku wonse. Iye ndithudi anapirira kwa nthawi yaitali. Koma pamene iye anadzipereka yekha, pamene iye anafooka ndipo sanathe kupiriranso . . .

¹⁸⁹ O Mulungu, mulole mpingo ukhale monga choncho, ufike pa . . .mpingo ufike pa malo amene iwo sungathe kupirira motalika ndi kuthekera kwake kwachibadwa, koma ukuyenera kudzipereka kwa Mulungu. Mulole a Methodisti azidzichitira okha manyazi kuti iwo ndi a Methodisti. Mulole a Baptisti ndipo mulole a Pentekoste azidzichitira okha manyazi, ndi kusiya kumagwiritsitsabe, ndi kumadzipereka kwa Mzimu.

¹⁹⁰ Panali pamenepo pamene Yakobo anadzakhala “kalonga wa Mulungu.” Baibulo linati iye anadzakhala “kalonga,” ndipo dzina lake linasinthidwa. Mukuona? Ndipo—ndipo, kumbukirani, iye anali munthu wamphamvu kwambiri kumbali *iyi*, wamphamvu mwaluntha; koma kumbali *inayo* iye anali kalonga wotsimphina, wofooka ndi wotopa, koma anali ndi mphamvu pamaso pa Mulungu.

¹⁹¹ Eya, inu mukhoza . . .Bungwe lanu likhoza kusweka mpaka mzidutswa. Kutchuka kwawu mwa oyandikana nawo mwanu, mukhoza kukhala “khwangwala wachikale” kuyambira pamenepo, mwa oyandikana nawo mwanu. Izo zikhoza kukhala zolondola. Koma ndikuuzani inu, mudzakhala ndi mphamvu ndi Mulungu. Ndingakonde nditakhala monga choncho. Nditenga njira imeneyo nthawi iliyonse.

¹⁹² Ophunzira anabwerera ndipo anasangalala chifukwa iwo anali okondwa kuti anayesedwa oyenera kuzenza chitonzo cha Ntchitoyo ndi cha Yesu. Ndithudi! Iwo adzakutchani inu “oyera odzigudubuza.”

¹⁹³ Mudzachoke pa malo amenewo nthawi ina, mulole izo zidasweke. Muchokeko ku zanu, “Chabwino, kuti, ndine wa Methodisti,” kapena “wa Presbateria” kapena “Ndine wa Assemblies,” “Ndine wa Oneness, ndine wabwino basi monga

inu muliri.” Chabwino. Mudzangochokako kumeneko nthawi ina, mudzapereke njira. Mudzapeze zonse . . .

¹⁹⁴ Mudzalole mngelo adzakugwireni inu nthawi ina, mngelo wa Ambuye amene ati adzakubweretsereni inu Choonadi cha Uthenga. Mudzalole iye adzakugwireni inu nthawi ina, inu mudzadzichepetsera mpaka ku ubatizo mu Dzina la Yesu, inu mudzadzichepetsera mpaka ku zina zonse za Izo. Inde, mudzatero, ndithudi mudzachita zimenezo. Eya, inu mu—mudzaiwala basi zaluntha zonse izi.

¹⁹⁵ Masiku angapo apitawo, mmodzi mwa abwenzi okoma kwambiri amene ndiri nawo, munthu wabwino, anati kwa ine, ndikutuluka mchipindamo nditakhala pa zokambirana, anatuluka mchipindamo, anati, “M’bale Branham . . .” Ndipo munthu uyu wakhala mmodzi wa wondithandizira wanga wa zachuma mu msonkhano kunja uko. Ndinafika pamalo amene sindimadziwa momwe ndingapangire chinthucho kuti chiziyenda, ndi kungodalira Mulungu; munthu uyu amangodzafufuta izo. Inde, munthu wabwino basi! Ndipo munthu uyu anali ndi ulendo ndipo anachokera ku mzinda wawukulu, kuno mausiku angapo apitawo, ndipo anadzaima mchipindamo ndipo anati kwa ine, madzulo wina, anati, “M’bale Branham,” anati, “Ine ndikungofuna kunena chinthu chimodzi.” Anati, “Palibe munthu koma amene amakukondani inu amene ndikumudziwa.”

Ine ndinati, “Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha zimenezo.”

¹⁹⁶ Anati, “M’bale Branham, pali chinthu chimodzi chokha, chinthu chimodzi cholakwika.”

Ine ndinati, “Ndi chiyani chimenecho, mlongo?”

¹⁹⁷ Anati, “Chabwino, chinthu chimodzicho ndi ichi, M’bale Branham, kuti ngati mungalekelere chabe pang’ono pa Chiphunzitso chaching’ono chimene muli nacho,” anati, “bungwe lirilonse likhoza kukulandirani inu.”

¹⁹⁸ Ine ndinawona pomwepo, ine ndinaganiza . . . Ine ndinati, “Chiphunzitso chiti, mlongo?”

Ndipo anati, “Oh, ubatizo umenewo mu Dzina la Yesu.”

¹⁹⁹ “Oh!” Ine ndinati, “Koma, mlongo, iwe sungayembekezere kuti ine ndilekerere pa Mawu a Mulungu ndipo nkukhalabe wantchito wa Mulungu.”

²⁰⁰ Ndipo anati, “Chabwino, apa, pali gulu la atumiki amene ine ndiri pano kuti ndidzawaimirire kuchokera mu mzinda wawukulu uwu.” Anati, “Ngati inu muti muwauze iwo kuti Mngelo wa Ambuye amene amakupatsani inu masomphenya awa anakuuzani inu kuti muzibatiza mu Dzina la Yesu, ndiye iwo akhala ololera kuti alandire Iwo.”

201 “Chabwino,” ine ndinati, “chowachitikira chawo ndi chofooka kuposa madzi otsukira mbale!” Ine ndinati, “Ine sindikusamala chimene mngelo aliyense anganene, ngati izo siziri mogwirizana ndi Mawu ine sindikhulupirira izo!” Ine ndinati, “Ngati mngelo ameneyo atandiuza ine chinachake chosiyana ndi Icho, sindingamukhulupirire mngeloyo.” Kulondola! Mawu a Mulungu amakhala oyambirira, pamwamba pa angelo onse ndi china chirichonse! Mngelo woona... Ine ndinati, “Ngati iye sanandiuze ine Izo, sindingamumvere iye.” Inde.

202 Donayo sanadziwe choti achite. Iye anati, “Ine sindinamvepo za zoterozo. Ine sindimadziwa konse za Izo.” Mwaona, ndi zimenezotu. Chotero ine ndinamupatsa dona wamng’onyo Malemba ena. Ndipo iye anati, “Ndikubwerera kwathu ndipo ndikawerenga Chipangano Chatsopano. Ine sindinayambe ndawerengapo Icho.” Mwaona, ndi zimenezotu. Oh, mai! Oh, mai! Ndi kumene mukufikako. Oh, mai!

203 Musiye kumayesetsa kugwiritsitsabe. Masukani! Ndicho chimene inu mukufuna kuti muzichita: masukani. Yakobo, pamene iye anamasuka iye zinamuyendera, iye anadzakhala kalonga ndipo anali ndi mphamvu ndi Mulungu.

204 Anali Davide *wamng’ono* atavala jekete lake lachipembedzo cha Sauli, amene anapita ku—ku—kukamenyana ndi Goliati. Ndipo pamene Davide anapita kunja uko kukamenyana ndi Goliati atavala zida zonse zazikulu izi, iye anayang’ana pozungulira, iye anayang’ana mmbuyo, iye ankawoneka ngati ena onsewo, chotero iye anati, “Pali chinachake chalakwika apa.”

205 Bola ngati iwe uli ngati dziko lapansi ndi kumalekerera nalo dziko lapansi, ndipo kumachita chinthu chomwecho chimene dziko liri, pali chinachake cholakwika.

206 Davide anati, “Izi zikuwoneka zolimba kwambiri. Ndiri ndi Digiri ya Udokotala, ndiri ndi Ph.D. Mwaona, ndine wa bungwe lalikulu, ine ndingathe bwanji kupita kukamenyana ndi zinthu zonsezi? Sindikudziwa kanthu za izo. Ine sindikudziwa kanthu za izo!” Davide anati, “Chotsani zinthuzo mwa ine.” Uko nkulondola. “Ngati nditi ndimenyere nkhondo Mulungu ine sindikufuna kuti ndiziwoneka ngati gulu la amantha limene layima apa, onse ananyamula zida ndipo anakalasa. Sindingakhale ndi msonkhano...”

207 Misonkhano yambiri, amuna ambiri, atumiki ambiri amene amabwera kwa ine ndi kudzavomereza kuti iwo amakhulupirira kuti Dzina la Yesu Khristu ndi lolondola kuti abatizidwemo, koma anati, “Gulu lathu likhoza kutitulutsa ife kunjja.” Iwe wowiringula wosauka iwe! Chotsa zida za Sauli!

208 N dipatseni mphamvu ndi mphamvu ya Mzimu Woyera! Mulungu, nditumizeni ine ndi legeni, ziribe kanthu chimene

icho chiri (chochepa bwanji), mugwetsereni mdaniyo pansi. Izo nzoona. Nditumizeni ine, koma musandirole ine ndivale monga ena onsewo a L.L., Ph.D., Madokotala, mtundu wonse wa zinthu.

²⁰⁹ Davide anati, “Chinthucho sichikuwoneka bwino.” Iye anati, “Ine sindikudziwa kanthu za izo.” Iye anati, “Chinthu chokhako chimene ine ndikuchidziwa, chimene ine ndiri nacho. . . Kuseri kwa chipululu ndinkaweta nkhusa za atate anga.” Ndipo anati, “Mkango unabwera ndipo unadzagwira nkhusa yaing’onyo ndi kudzathawa nayo iyo, ndipo ine ndinadziwa kuti iyo inali nkhusa ya abambo anga, ndi, oh, ine—ine—ine ndi. . . Ndinalibe zida, koma ndinangotenga legeni yanga ndi kuwutsatira iwo.” Anati, “Ndinawupha iwo ndipo ndinabweretsanso nkhusayo.” Oh, mai! Iwo atayima pamenepo, nkondo mdzanja lawo, sakanatha kuchita izo.

²¹⁰ Ndiro limene liri vuto lero. Mulungu ali ndi nkhusa zambiri zimene zasochera, mabungwe ndi zinthu zawaba iwo, kuwabweretsa iwo mu kuwerenga maganizo. Mulungu tipatseni ife a Davide ndi Mawu a Mulungu ndi mphamvu ya Mulungu, kuti azitsogolere izo pamene tipita kukakumana ndi zimphona zalunthazi (Kulondola!) ndi ma Ph., L.L.D., Q.U.S.T. onse, kapena chirichonse chimene chingakhale. Ndipatseni ine Mawu a Mulungu ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ndipo, ine ndikuuzani inu, ife tikhoza kukapha chimphona chirichonse ku tchireko. Kulondola! Tikufuna amuna amene angathe. . .

²¹¹ Bwanji, Davide anali wowiringula wosaukitsitsa kwambiri amene analipo kutchireko, kuti apite kukamenyana ndi chimphonacho. Iye, bwanji, iye—iye sanali kanthu koma mnyamata. Ndipo Baibulo linati iye anali “wofiira,” munthu wamng’ono wosawoneka bwino, mwinamwake wamapewa akugwa, chikopa cha nkhusa chitakulungidwa pa iye. Iye analibe ma digiri a luntha aakulu awa ndi wophunzitsidwa bwino. Iye sankadziwa kanthu za lupanga. Iye sankadziwa kanthu za kuphunzitsidwa konse uku kumene Sauli. . .

²¹² Sauli anali wabwino koposa amene iwo akanakhala naye, Bishopu Sauli. Ndithudi, iye anali mutu ndi mapewa pamwamba pa gulu lonse la nkondolo. Bwanji, iye anali—iye anali amene ankayenera kupita kukamenyana naye, koma iye ankachita mantha.

²¹³ Ndipo lero ife tikudziwa ife tikusowa chitsitsimutso. Ife tikudziwa kuti tikusowa kukondoweza pakati pa anthu. Izo sizidzatengera Dokotala wa Zaumulungu. Izo zidzatengera wofooka (Aleluya) izo zidzatengera Mawu a Mulungu mu mphamvu ya chiwukitsiro cha Khristu ndi kupha chinthu ichi. Izo zidzamubweretsa Khristu ku dziko mu. . .kuwalola iwo awone kuti Iye akhozabe kutsegula maso a akhungu, kuchiza odwala, kuwukitsa akufa, ndipo Iye ndi Mulungu, Mgonjetsi! Ameni. Ife tikusowa Davide, wosaphunzitsidwa mu masukulu

a zafioloje, ife tikusowa mwamuna amene sakudziwa kanthu za izo, mnyamata wina wamng'ono wolima kapena chinachake, mnyamata wina wamng'ono wa mapewa ake akugwa, wosati ungamuyang'ane mochuluka, adzabwera akuyenda munjira ndi mphamvu ya Mulungu.

214 Amayi akumwalira, anati, “Billy, ine ndakudalira ndipo ndakukhulupirira iwe. Iwe wakhala mphamvu yanga yauzimu, wanditsogolera ine kwa Mulungu.”

215 Ine ndinati, “Amayi, pamene ine ndinali mnyamata... Chiyambi chathu, ndithudi, Irish, ife timakhala ngati timatsamira pang'ono Chikatolika.” Ndipo ine ndinati, “Mpingo unanena kuti—kuti iwo—iwo anali gulu la anthu, anali ndi zonsezo, chirichonse chimene iwo ankachita chinali chabwino. Ine sindikanakhulupirira izo, chifukwa Achilutera anati, ‘Ndife gulu la anthu, tiri nazo zonsezo.’ A Baptisti anati, ‘Ndife thupi, tiri nazo zonse.’ Pali ochuluka kwambiri, alipo pafupifupi mabungwe osiyanasiyana naini handiredede.” Ine ndinati, “Amayi, ine sindingayike chidaliro mu zimenezo, ndi uti wa iwo ali wolondola?”

216 Ndinadzapeza kuti, ndikunena izi modzichepetsa ndi mokoma, koma ndikukhulupirira kuti palibe mmodzi wa iwo akulondola. Uko nkulondola. Ine ndinabwerera ku Mawu a Mulungu, ine ndinawona chimene Iwo anachita kumbuyo uko. (Ndipo kenako, Mulungu, tiloleni ife tonse tibwerere mmbuyo uko.) Ndipo ndi kufooka, ndi kupanda thandizo la bungwe, kupanda thandizo la zipembedzo, kupanda thandizo la kakhazikitsidwe ka zachipembedzo, koma mu kuphweka ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene inagwa pa Pentekoste, ndi uthenga womwewo umene Petro anali nawo pa Tsiku la Pentekoste, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.”

217 Simudzakhala pa goli monga gulu la afioloje awa, ndi kolala yanu yotembenezidwa ndi madigiri a Bachelor of Arts. Koma, m'bale, iwe udzakhala ndi chinachake mdzanja lako, ndipo bola ngati Mzimu wa Mulungu udzalowe mu Mawu amenewo Iwo udzagonjetsa ndi kuzibweretsanso nkhoa zotayikazo zimene zinasochera. Amen! Kuvomereza zofooka zathu! Tayani Chiphunzitso chanu cha Zaumulungu! Tayani kudziwa—zonse kwanu, umembala wanu! Dzivuleni nokha pamaso pa Mulungu, kuyankhula mwauzimu, ndipo mudzitche nokha “wosayenera!” Ndiye Mulungu akhoza kukugwiritsani inu ntchito. Musangonena izo kuchokera mkamwa mwanu, muzibweretse izo kuchokera mu mtima mwanu.

218 Yakobo, Davide, iwo ankayenera kudzivula okha. Iye anali wofooketsetsa pakati pa gulu lonselo.

219 Taganizani za, mwinamwake, asilikari teni sauzande kapena handirede sauzande pa phiri. Onse a iwo ophunzitsidwa, aliyense wa iwo ali ndi Ph.D., aliyense wa iwo ali ndi mikondo, iwo anali asilikari. Aliyense wa iwo anali Corporal *Wakuti-ndi-wakuti*, Private *Wakuti-ndi-wakuti* (ngakhale kwa ma Private), General *Wakuti-ndi-wakuti*, Lieutenant *Wakuti-ndi-wakuti*. “General wamkulu wa nyenyezi zinai Sauli, Bishopu, inde, Ulemu wanu, Bwana!” Aliyense wa iwo atayima pamenepo, amuna ophunzitsidwa.

220 Ndipo mdani atayima pa phiri, anati, “Inu gulu la amantha.” Oh!

221 Ndipo pamwamba mu msasa munabwera wamng’ono, wamapewa-akugwa, (O Mulungu!), munthu wamng’ono wowoneka-mofiira, legeni yaing’ono pa nsana wake, ali ndi chitumbuwa champesa mu dzanja lake cha m’bale wake. Ndipo chimphona chija chinatulukira ndipo chimafuula mowirikiza. Chinati, “Inu mukutanthauza kundiuza ine kuti inu gulu la masikolala ophunzitsidwa pano mungayime pamenepo ndi kumulola Mfilisiti wosadulidwa uyo kuti anyoze Mawu a Mulungu wamoyo?” Ameni! Anati, “Kodi inu mukumuwopa iye?”

222 Sauli anati, “Ngati iwe ukufuna kupita, bwera kuno. Ine ndi—ine ndi—ine ndikutumiza iwe ku sukulu kwa zaka twente tsopano, ndipo ndikakupatsa iwe a—Ph.D. Ndikuuza iwe chimene nditi ndikachite, ine ndidzangokupatsa iwe digiri yanga.”

223 Iye anati, “Chichotsenipo chinthucho.” Oh, mai! “Ine sindikufuna kanthu kochita nacho.” Iye ankafuna kudalira Mulungu. Iye anati, “Ndikudziwa chimene Mulungu anachita nane ndi *ichi*, ndipo ndine wokonzeka kudalira Mulungu pamaso pa chirichonse ndi *icho*.” Ameni! Ndicho chomuchitikira cha Mkristu.

224 Ngakhale Saulo, pamene ankayenera kuti avule zida zake, iye anavula zida za mpingo, iye anachita monga Davide anachitira. Koma pamene Saulo anafika kumapeto kwa njirayo, iye anati, “Ndamenya nkondo yabwino.” Ameneyo anali mdani womaliza kumugonjetsa. “Ndamenya nkondo yabwino, ndatsiriza njira yanga, ndasunga Chikhulupiriro. Kuyambira pamenepo payikidwa kwa ine korona, amene Ambuye, Woweruza wolungama, adzandipatsa ine tsiku limenelo.” Anati, “Osati ine ndekha, komanso onse amene amakonda kuwonekera Kwake.”

225 Imfa inati, “Koma ndikupeza iwe mu mphindi pang’ono.” Ndipo manda anati, “Ine ndikakuwumba iwe uko.”

226 Iye anati, “O imfa, mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Ndikudziwa kuti ndagona muno mu dzenje la Chiroma, womangidwa ndi maunyolo, mikono yanga ndi

manja anga, ndipo ine—ine ndiri ndi mikwingwirima sarte naini pa nsana panga. Ndiri pano ndi misozi ikupweteka maso mwanga mpaka sindikuwonanso. Ine ndikulephera kuwona ndi diso langa lachibadwa, koma ine ndikutha kuwona korona wa chirungamo atayikidwa uko. Akakolo anga atopa. Ndagwa kambiri kuchokera ku mkate wakale wowumbidwa umene iwo anaponya muno, ndipo makoswe andikwerakwera ine, ndi akangaude ndi zinthu, mpaka ine ndafooka.” Koma amakhoza kuyima pamaso pa imfa ndi kunena, “Mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti?” ndi unyolo ukugwederera mmanja ake. Aleluya! (Ndi chimene ife tikusowa.) “Manda, chigonjetso chako chiri kuti?”

Manda anati, “Ine ndikuvunditsa iwe, Paulo.”

227 Iye anati, “Koma ayamikike Mulungu, ndalandira kale chigonjetso kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.”

228 Pamene iye anali wofooka, wake—wachipembedzo, wake. . . miyambo yake yonse inali itathetsedwa kwa iye. Mapepala onse a kudzozedwa kwake anali atachotsedwa kwa iye. Iye sanalinso wa Assemblies konse, kapena wa . . . aliyense wa iwo. Mwaona, iye sanali wa aliyense wa iwo konse. Iye anali atayankhula mochulukwa kwambiri motsutsa iwo mpaka mabishopu amenewo anali. . . anati, “Inu mukutanthauza kundiuza ine mwamuna amene ali ndi zaka twente wa ndende ya Chiroma kumtunda uko ndipo angatiuze ife kuti tisamawalole akazi athu kulalikira? Huh! Musatiuze ife zimenezo,” anati, “ife tikudziwa bwino. Ndi ndani munthu ameneyo kumtunda uko, mulimonse, akutiuzza ife kuti tichite *ichi*, *icho* kapena *china*?” Anati, “Ife tikudziwa chimene tikuchita.”

229 “Eya,” Paulo anati, “pali amuna amene akuwuka pakati panu, ayambitsa bungwe posachedwapa, adzawuka ndipo adzachoka ku Chikhulupiriro monga choncho, osakhala ndi Mzimu wa Mulungu.” Anati, “Iwo atuluka kale pakati pathu chifukwa iwo sanali a ife.”

230 Ndipo, chiyani, izo zinachitika? Zinabwera momwemo mu mpingo wa Katolika; kuchokera ku Katolika kupita kwa Lutheran; ndipo kumapitirira mpaka kwa wotsiriza, Assemblies of God, chinthu chomwecho, akuchita chinthu chomwecho.

Nthawi zonse, chinthu chomwecho!

231 Koma, oh, kwa mwamuna kapena mkazi amene ali wofooka mokwanira, amene amazindikira kufooka kwanu, amene angamulole Mulungu akugwiritseni inu ntchito! Ndimangopitiriza kuyankhula, ndikuganiza ndimayankhula motalika kwambiri.

232 Tsopano, icho chinali chiyani? Tsopano, iye anali. . . Davide anali wosaphunzira kwambiri pa gululo. Iye sanaphunzire sukulu ya nkondo, iye sankadziwa kanthu za izo. Chotero iye analibe maphunziro pakuti palibe imodzi ya nkondo iyi imene

inayikidwa patsogolo pake, koma iye anazindikira kuti kunali Mulungu. Ndipo iye anatenga chinthu chofooketsetsa; iwo anali ndi mikondo, zida, mauta, ndi china chirichonse, ndipo Davide anali ndi legeni yang'ono yokhala ndi mwala mmenemo. Koma, mwaona, iye ankadziwa chimene iye akanakhoza kudaliramo. Iye anavomereza kufooka kwake, koma chikhulupiriro chake mwa Mulungu.

²³³ Iye anati, “Sindikufuna chishango chirichonse pa ine kuti ndisagwetse kalikonse. Sindikufuna kubwera pamenepo, kudzati, ‘Tsopano, kodi inu abale mugwirizana ndi ine? Ndine wa Assemblies, ndine wa Presbyterian, ndine wa Methodist, ndine wa Baptist, kodi inu abale mugwirizana nane?’ Sindikufuna kudziwa chirichonse cha zinthu zimenezo. ‘Apa, ndikuwonetsani mthumba mwanga, ndiri ndi digiri yanga. Ine ndangopezeka kumene Bachelor ya Art yanga. Ndimachokera ku yunivesite ya *Chakuti-ndi-chikuti*, ine—ine ndinaphunzitsidwa kumeneko. Ine ndiri nazo. Oh, ndikhoza kuyankhula! Ndine *ichi, icho*, kapena *china*.” Iye sankafuna chirichonse cha zinthu zimenezo!

²³⁴ Zonse zimene iye ankafuna, anati, “Ine ndiri ndi chidaliro changa mwa Mulungu ndipo apa ndikupita.” Ndi zimenezotu. Ndipo chimphonacho chinapita kumusi. Ndi zimenezotu.

²³⁵ Ndicho chimene ife tikusowa lero, m'bale. Ife tikusowa, lero, amuna ngati Davide, osati zochitika zaku yunivesite.

²³⁶ Anali Mikaya wamng'ono, Mikaya wamng'ono, mwana wa Imla, wosauka, wokanidwa, wotayidwa kunja kwa zipembedzo zonse chifukwa cha kuyima kwake koono kwa Mulungu. Koma kunabwera munthu wa Mulungu nthawi ina, kumusiko, dzina lake Yehosafati, ndipo ananena kumeneko, “Ine ndikufuna kudziwa Mawu owona a Mulungu.”

²³⁷ Sauli anati, “Ine ndiri ndi foro handirede a opambana amene inu munayamba mwawadziwapo.” Anati, “Iwo onse ali ndi madigiri awo, iwo onse anaphunzitsidwa kuno ku sukulu.” Anati, “Bwanji, iwo ndi alaliki opambana amene inu munayamba mwawamvapo.” Anati, “Ndiwatulutsa iwo ndipo tidzafunsira kwa Yehova mmalo mwako.”

²³⁸ Koma kenako iye anatulukira kunja uko ndipo iye anayang'ana mozungulira, Yehosafati anati, “Eya, ndimamumva uyu akunena *izo*, ndipo ndimamumva uyo akunena *icho*, koma,” anati, “kodi muli naye wina? Kodi mulibe wina?”

²³⁹ Mulungu anali woti apititsa uthenga ku mtima woona uwu. Kunali mmodzi yekha wa iwo atayima pamenepo, koma Mulungu amakhala ndi munthu wa ameneyo. Ameneyo. Ngati pali mtima umodzi wokha woona, penapake Mulungu amakhala naye munthu wa iye. Yehosafati anali mwamuna weniweni, mfumu yopa Mulungu, ndipo anali ndi nzeru zokwanira kudziwa kuti mauthenga awo anali olakwika. Iye ankadziwa kuti izo zinali

zosiyana ndi Mawu, ameni (Oh, M'bale Neville!), Yehosafati ankadziwa zimenezo.

240 Iye anati, “Chabwino, ine—ine ndinadutsa mu mbiri yonseyo, chipepala kuno mu seminare iyi, ine ndinamupeza aliyense wa iwo kunja kuno.” Anati, “Chabwino, penyani apa, uyu ali ndi . . . chabwino, tawonani madigirii amene iye ali nawo. Tamuwonani uyu apa,” akuti, “taonani—taonani madigirii amene iye ali nawo. Tayang’anani pa Zedekiya apa, iye ndi mkulu wa onsewo. Bwanji, iye ndi bishopu, iye ali pamwamba pa ife tonse. Ndithudi inu mutenga mawu ake!”

Yehosafati anati, “Eya,” anati, “Ine—ine—ine . . .”

241 “Chabwino, taonani, taonani, ena onse akugwirizana naye iye. Iwo onse ndi gulu limodzi lalikulu! Ndipo simunganene kuti iwo si Ahebri. Inu simunganene kuti iwo si aneneri, digirii ndi iyi ikutsimikizira kuti iwo ali.”

242 Yehosafati anati, “Eya, ine—ine—ine ndikudziwa, Ahabu.” Anati, “Izo—izo zonse nzabwino, koma . . .”

243 Anati, “Iwe ndi ndani . . . Iwe undifunsa bwanji ena owonjezera? Apo pali sukulu yanga yonse! Pamenepo pali bungwe lonse pamodzi.”

244 “Koma kodi inu mulibe mmodzi amene si wagulu limenelo? Kodi palibe mmodzi, penapake?”

245 “Chabwino, kodi iye angakhale ndani? Angakhale mbuli yosaphunzira! Chabwino, mungafune chiyani ndi munthu woteroyo?”

246 “Koma—koma ndikungokufunsani inu, kodi inu mulibe mmodzi, penapake?”

247 “Oh,” iye anati, “eya, alipo mmodzi woteroyo.” (Uko, oh, zikomo Mulungu chifukwa cha zimenezo!) “Alipo mmodzi woteroyo, koma,” anati, “Ndimadana naye iye. Ndipo ena onse a iwo amadana naye iye, nawonso.” Anati, “Ife tinamukankha, ndipo iwo anamuthamangitsa iye mu bungwe limenelo, aliyense wa iwo.” Anati, “Iye anabwera kuno kudzakhala ndi msonkhano, ife tinamuthamangitsira iye kunja kwa mzinda. Inde, bwana. Tiribe chochita naye iye. Chabwino,” anati, “iye ndi wofooka, ndipo amachokera ku banja losauka kwambiri. Galamala yake ndi yoyipa.” (Uh-huh, monga Moody, inu mukudziwa.) “Eya, galamala yake ndi yoyipa.” Ndipo anati, “Zoonadi, kwa wa fioloje, iye ndi wosauka kwambiri amene ndinayamba ndamumvapo. Sindinamvepo chirichonse chonga iye. Oh, iye amangowononga mwambo wawo. Bwanji, Chikhulupiriro chawo cha Atumwi chang’ambidwa mzidutswa ndi iye. Ine sindinamvepo za chinthu choterocho! Oh, iye amangoching’amba icho, ndipo iwo amamuda iye ndipo ine ndimamuda iye, aliyense amamuda iye.”

248 “Oh,” Yehosafati anati, “musalole kuti mfumu inene chomwecho, koma ndikufuna ndimumve iye.” Iye ankadziwa chimene Elisha akanati adzanene! Iye ankadziwa chiyani.

249 Mulungu anawalambalala alaliki onse aakulu, amphamvu, aluntha, ndipo anadzaika Uthenga Wake mwa munthu wamng’ono amene ankadzinenera kuti samadziwa kalikonse. Koma kodi iye anachita chiyani?

250 Iwo anamupatsa iye yesero, ndipo anati, “Tsopano, iwe ukanene chinthu chomwecho chimene iwo ananena.”

Iye anati, “Ine ndikanena chimene Mulungu ati ayike mkamwa mwanga, ndizo zonse.”

251 Iye anati, “Ngati ukufuna kukhala wamphamvu tsopano, kumbukira kuti ndiwe basi. . . ndiwe—iwe uli ngati kunja kwa dongosolo apa, mnyamata. Kumbukira, iwe unathamangitsidwa mu bungwe limenelo. Iwo akhoza kukuganiziranso chiyanjano chako ngati ungagwirizane nawo mu nthawi yamavuto ngati iyi. Ife tonse tikukonzekera kukhala ndi kampeni yabwino,” anati, “ngati iwe ungagwirizane ndi ine.”

252 Anati, “Sindinena chirichonse koma chimene Mulungu wanena!” Kunyengerera, kodi mungayembekezere munthu wa Mulungu kunyengerera pa Mawu a Mulungu? Ayi, bwana, mulibemo mwa iye.

253 Anati, “Koma ndiwe wofooka. Ndiwe wochokera ku banja losauka. Bwanji, iwe ukudziwa chiyani, iwo akhoza. . .”

“Ine sindikusamala chimene iwo akuchita.”

254 “Chabwino, iwo adzakuyendetsa iwe kuchoka mdziko kupita ku dziko mu ndege. Iwo adzachita chirichonse, waona, ngati iwe—ngati iwe basi. . .”

255 “Ayi, ayi. Ndidzangonena chimene Mulungu angayike mkamwa mwanga.” Mulungu analambalala gulu lonse, (inde, bwana, kuyima kwake kowona kunachita izo) analambalala foro handirede ndipo anamupatsa iye PAKUTI ATERO AMBUYE!

256 Ndiye kodi iwo anakhulupirira Izo? Ayi, bwana! Iwo anati, “Izo si PAKUTI ATERO AMBUYE, seminare yathu siimaphunzitsa zinthu zotero monga zimenezo. Chabwino, apa pali bishopu wathu, wanena kale mawu, iye analemba mwambowo. Ife tonse tinasonkhana pamodzi, tinapanga masakulu athu. Mulungu ali nafe! Ndi njira iti imene Mulungu anapita kuchoka kwa iye pamene Iwo anapita kwa iwe?”

Iye anati, “Mudzawona, nthawiyina.” Uh-huh, ndiko kulondola.

257 Kodi iye anali chiyani? Iye anali wofooka, koma anali wamphamvu kwambiri pakati pa iwo. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anali ndi Mawu a Ambuye. Oh, m’bale, kodi

izo zimapanga kusiyana kotani pa za . . . china chirichonse bola ngati inu muli ndi PAKUTI ATERO AMBUYE?

²⁵⁸ “Kuti, M’bale Branham, ngati inu munganyengerere pa Dzina la Yesu pa ubatizo, chabwino, tidzakhala ndi msonkhano waukulu ku Chicago kapena malo awa monga awa.” Huh! Kodi inu mukuganiza kuti muchita zimenezo? Ine sindikusamala kumene inu mumasonkhana pamodzi, chimene inu mumachita, m’bale, khalani ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

²⁵⁹ Ine ndikufuna ena a iwo abwere adzandiuze ine pamene Izo ziri zolakwika. Adzandiwonetse ine mu Mawu a Mulungu pamene Izo ziri zolakwika. Eya. Iwo sangachite izo. Ayi, bwana. Koma Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE! Khalani ndi Iwo, ngati aliyense wa iwo akukankhani inu. Sindikusamala kuti mukhala wofooka bwanji, “Kenako ine ndidzakhala wamphamvu.” Pamene iwo andithamangitsira ine kunja, Mulungu adzanditengera ine mkati. Uh-huh, eya. Mulungu . . . Iwo akakutulutsani inu, Mulungu adzakutengerani inu mkati.

²⁶⁰ Kumbukirani, ndi oyipa amene Mulungu amawatola nthawizonse, osadziwika. Kenako Iye amawapanga iwo *ofunikira* kwa Iye. Mwina akhoza kusadziwa izo mmoyo uno, koma chidzakhala mu umene ukudzawo; mwaona, ndi umenewo.

²⁶¹ Ndipo anamupatsa iye PAKUTI ATERO AMBUYE, chifukwa chiyani? Iye anakhala ndi Mawu. Iye anali ndi Uthenga wolondola. Mulungu anamupatsa iye masomphenya. Ena onse a iwo analibe masomphenya. Mukuona? Iye anali ndi masomphenya. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anakhala ndi Mawu. Pamenepo ndi pamene tinawona zizindikiro ndi zodabwitsa. Chifukwa . . . Enawo akupanga ngati Iwo, koma iye anakhala ndi Mawu. Tsopano tiyeni tifulumire.

²⁶² Eliya, ndi pamene mpingo wake unamutulutsa iye ndi kumusiya iye kamba ka dziko lamakono. Ine ndikuganizira kuti Eliya anali atawakonza iwo pa malasha. Kodi simukuganiza choncho? Inu mukudziwa chimene Eliya anali. Ine ndikulingalira, mu utumiki wake woyambirira, iye anayima pamene ndipo anati, “Bwanji, inu akazi mukuyesera kukhala ngati Dona Woyamba,” zipewa zimenezo, inu mukudziwa, “Abiti Yezebeli! Inu akazi amakono, pokhala ngati Dona Woyamba wa dziko, kumavala monga iye, kumachita monga iye. Alaliki inu!” Oh, mai, momwe iye anawapesera iwo! Ndipo onse ankangopitirira kugwa mpaka panalibe aliyense.

²⁶³ Iye ankayenera kuti afike kumapeto kwa njira yake. Panalibe amene akanagwirizana naye konse. Panalibe mpingo uliwonse umene ukanagwirizana naye iye. Mpingo wake wonse unamusiya iye, unabwerera ku dziko (mofanana monga momwe ziliri tsopano), uko nkulondola, unabwerera ku dziko. Ochepa chabe anali kukangamira, mmodzi apa ndi mmodzi

apo, akubwera kuchokera kutali kudutsa dziko kumene inu munkayenera kuti mupite kukamuwona iye, ndi zina zotero. Iye anali mu mawonekedwe oyipa kwambiri, iye anali atafika pamapeto a chidziwitso chake.

²⁶⁴ Iye anati, “Ambuye, ine ndinayima pa Mawu Anu, ine ndinanena Choonadi. Ndipo onse a iwo anapita, palibe amene watsala pano. Ine ndiribe, ndiribe ngakhale aliyense woti ndizimulalikira.” Amen. “Inde, ine ndinaima pa Mawu Anu, Ambuye, ndipo tsopano tayang’anani pamene ine ndiri tsopano, palibe mmodzi wa iwo ati andilandire ine. Ine ndikapita ku tauni, iwo amati, ‘Apa pakubwera waphokoso wakale uja. Eya, eya, uyu ndi waphokoso wakale uja akubwera mtawuni, tsopano ayamba kupitiriza—kupitiriza za moyo uwo wamakono ndi chirichonse.’”

²⁶⁵ “Musamulandire iye! Abusa, musagwirizane ndi munthu ameneyo! Ayi, bwana!”

²⁶⁶ Abusa, “Tsopano wotentheka wakale uja ali mtawuni kenanso. Mwaona, Eliya uja kunja uko, munthu wokalamba wamutu wadazi. Musakhale naye chidwi munthu wokalamba ameneyo. Tamuoneni iye, iye samavala nkomwe ngati mtsogoleri wachipembedzo atavala miinjira yake yaunsembe ngati yanga (chipewa chake, inu mukudziwa; ndipo waimirira kutsogolo, ndi kolala yotembenezidwa, inu mukudziwa).” Anati, “Iye satero. . .” Anati, “Iye—iye. . . iwo. . . iye ndi wosiyana. . . Iye—iye ndi munthu wosamvetsetseka.”

²⁶⁷ Ndipo ine ndikuganiza ena a anyamata otchukawo anati, “Inu mukudziwa chiyani? Iye—iye ndi wamisala. Uh-huh, inde, iye—iye ndi wamisala, amakhala kunja uko mchipululu, amakhala kuthengo nthawi yake yambiri, akubwera atazikulunga ndi chikopa chankhosa. Oh, mai! Ndipo akatero aziwatsutsa akazi amenewo! Ine sindinawonepo chinthu choterocho. Musatero inu. . . musatero—musatero—musakhale ndi chochita ndi iye, nkomwe! Musagwirizane naye!”

²⁶⁸ Chabwino, bungwe la atumiki linali litasonkhana pamodzi, inu mukudziwa, anati, “Musakhale—musakhale ndi chirichonse choti mu. . . Mumasuleni iye, iye potsiriza. . . adzafika kumapeto kwa nzeru zake. Musiyeni iye—musiyeni iye atulutse ubongo wake womwe. Ndizo zonse, musiyeni iye yekha.”

²⁶⁹ Koma Eliya wokalamba, akuyenda moona pomwepo ndi Mulungu, (Mai, mai.) anakhala pomwepo ndi Mawu. Iwo amakhala ndi msonkhano wawung’ono kumusi uko, ndipo iye amayang’ana pa omvetsera, ndikuti, “Ayezebeli nonse inu!”

²⁷⁰ “Oh, kulimba mtima kumene! Sindidzapitanso kukamumva munthu ameneyo! Ayi, bwana, sindidzakhala ndi kalikonse!”

²⁷¹ Izo sizinamuletse iye, iye anakhala pomwepo chimodzimodzi basi. Pamene iye anataya mpingo wake, pamene iye anataya

zake...zipembedzo zonse zinamutembenukira iye, panali pamene (pamene iye anafooka) iye anati, “Ndine ndekha amene ndatsala, ndipo iwo akufunafuna kuti andiphe ine.” Anati, “Iwo andiwombera ine ngati angakwanitse izo.” Uh-huh. Mukuona? “Koma ine...Iwo akufunafuna moyo wanga. Ndipo ndine ndekha amene ndatsalira, Ambuye, kodi ndichite chiyani?”

²⁷² Panali pamene, pamene iye anafooka (komabe kuyima moona, kuvomereza kufooka kwake ndi chirichonse), mpamene Mulungu anati, “Bwera pamwamba pa phiri, ndikupatsa iwe uthenga watsopano. Ndikutumizira iwe uthenga watsopano tsopano. Ndakuza kale iwe, ‘Pita ukatsutse zinthu izi,’ tsopano ndikutumizanso iwe ubwerere ndi chinachake kuti ukatsimikizire kuti Iwo anali olondola.” Anati, “Wachita ntchito yabwino, Eliya. Iwe unawauza iwo za Dona Woyamba, ndi zonse izo, ndi momwe iwo achitira. Iwe unamutsutsa Ahabu ndi zinthu zake zonse zamakono ndi mipingo yonse yamakono, ndipo tinawauza alalikiwo kumene iwo anali. Iwe unali chitsanzo. Iwe unayima pamene popanda chithandizo chirichonse, bungwe lililonse, chirichonse kumbuyo kwako, koma iwe unakhala ndi Mawu Anga. Tsopano ndikupatsa chinachake. Pita kumusi uko ndipo ukamuuze wachinyengo uja, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE! Sipakhala ngakhale mame akugwa kuchokera Kumwamba mpaka ine nditawaitana iwo.’” Mai! Mai! Anamutengera iye pamwamba pa phiri kuti akamuwonetse iye chinachake!

²⁷³ Oh, ine ndikukhoza kumuwona iye mmawa umenewo, akubwera, akuyenda mu msewu waku Samaria uwo. Iye analibe zochuluka zoti ungamamuyang’ane, ndithudi, mutu wadazi uwo ukuwala ku dzuwa, imvi ndi ndevu zikulendewera pa nkhope yake, chidutsa cha chikopa cha nkhoa. Baibulo linati iye anali “waubweya,” ubweya paliponse pa iye, ine ndikulingalira iye anali wonyansa kumuyang’ana; ndodo yaing’ono yakale iyo mdzanja lake, ndi maso aang’ono akale awo akuyang’ana mlengalenga, akuyenda chotsika mkanjira. Ndipo inu... iye...Ine ndikuganiza iye ankachita ngati wausinkhu wa zaka sikisitini pamene iye anali wa pafupifupi eyite. Apa iye akubwera, akuyenda kumatsika msewu, molunjika waku Samariya. M’bale, anali atalimbikitsidwa mu kufooka kwake, “Mphamvu zanga ndi zokwanira. Usadandaule za mabungwe, Eliya. Usadandaule za iwo, mphamvu Yanga ndi zonse zimene ukuzisowa.”

²⁷⁴ Ine ndikukumbukira nditayima pafupi ndi kachisi wamkulu nthawi ina, ndipo ine ndinati, “Ambuye, ine ndidana nazo kuti iwo abwere ku yanga—ofesi yanga.”

Iye anati, “Ine ndi Gawo lako.” Mukuona? “Ine ndi Gawo lako.”

²⁷⁵ “Mu—mu kufooka ndiye ine—ndine... Mphamvu yanga ndi

yolimba. Chifuniro Changa changwiwo chikhoza kuchitidwa (Paulo, kapena Eliya, kaya ndiwe ndani) ukachokapo panjira.” Mukuona? “Mu kufooka kwako, pamene Ine ndimalimbikitsidwa. Ndine Mmodziyo! Ndine Iye Wamphamvuyo amene ndimabwera ndikudzazadza.”

²⁷⁶ Ine ndikukhoza kumuwona iye akuyenda kumusi kwa msewu waku Samariya umenewo, maso aang’ono akale awo akuwoneka monga *chomwecho*, mnyamata, akukhala ngati akumwetulira mwatheka pa nkhope yake. M’bale, iye anayenda mpaka pamaso kumene pa Ahabu. Sanachite chibwibwi, sanajejeme. Ayi, ayi! Ukugunda pansu pa chifuwa chakale chowonda icho unali mtima wokhala ndi Mzimu Woyera ukukhala mmenemo. Inde, ndithudi! Anabwera akuyenda mu msewu umenewo, anayenda mpaka patsogolo pa Ahabu, ndipo anati, “Ngakhale mame sadzagwa kufikira ine nditawaitana iwo.”

²⁷⁷ Anaponda mapazi ake ndipo, anatembenuka mozungulira, kubwerera mu chipululu iye anapita. Anati, “Imeneyo inali ntchito yabwino, Eliya. Bwera kuno, Ine ndalamulira akhwangwala onse kuti akudyetse iwe tsopano, ndi. . . ndipo khala pansu apa kanthawi.” Oh, mai!

²⁷⁸ Pamene iye anali wofooka, ndiye anadzakhala wamphamvu. Inde, bwana. Iye anatseka mmiyamba kuti mvula isavumbe. Ndi pamene anadzakhala wamphamvu, pamene anataya mpingo wake, anataya chirichonse chimene iye anali nacho, china chirichonse. Koma anakhala ndi Mawu a Mulungu, zitatero iye anadzakhala ndi mphamvu yotseka miyamba.

²⁷⁹ Pamene Yakobo anataya mphamvu zake zonse, ndiye Mulungu anadzamupatsa iye mphamvu yokhala kalonga. Mukuona?

²⁸⁰ Pamene Paulo anataya maphunziro ake ndi fioloje yake yonse, Mulungu anamupanga iye kukhala mmishonare kwa Amitundu.

²⁸¹ Pamene Mose anataya kuthekera kwake konse ndi kukhala wofooka, Mulungu anamupanga iye wamphamvu, ndipo anamutumiza ku Igupto mu mphamvu ya Mzimu, ali wa usinkhu wa zaka eyite; ndevu zikulendewera pansu, mkazi wake pa bulu ndi mwana atakhala mchiuno mwake, ndi ndodo mdzanja lake, anapita kumeneko ndipo anakagonjetsa Igupto. Eya. Mukuona? Osati ndi ankhondo kumbuyo kwake, monga iye ankafunira kuti apite, koma mu mphamvu ya Mzimu. Amen!

Pamene iwe wafooka ndiye umakhala wamphamvu.

²⁸² Akungoyenda kumatsika mumsewu uja, iye sanachite chibwibwi, sanapunthwe, sanachite kalikonse, anayenda mpaka pamaso pa Ahabu, ndipo anati, “Ine ndiri ndi Mawu a Ambuye.”

Iye anati, “Iwe ndi amene ukuvutitsa Israeli.”

283 Iye anati, “Iweyo ndi amene ukuvutitsa Israeli.” Inde, bwana. Oh, m’bale! Inde, bwana. “Abweretse ansembe aluntha awo amene uli nawo kumtunda kuno, ndipo tiyeni tiwone amene ali Mulungu.” Ndi zimenezotu. “Tikwere pamwamba pa Phiri la Karimeli, tikamulole Mulungu amene anayankha pa Pentekoste adzayankhe kachiwiri. Tiyeni tikawone ngati Mulungu akadali Mulungu yemweyo, ngati Yesu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Iye anaatsika kuchokera pa phiri, iye anali ndi Uthenga. Inde. Iye anafooka kwenikweni poyamba, ngakhale, iye anataya chirichonse iye asanachite icho. Iye ankayenera kufooka kuti akhale wamphamvu.

284 Ndi kuphweka kwa Uthenga kumene kumawadodometsa anthu. Iwo amayesetsa kuwupanga Iwo kukhala chaluntha chachikulu chinachake chimzake, pamene ndi kuphwekako. Koma Mulungu amatenga chida chomwecho cha kudzichepetsa ndi kufooka ndi kuphweka, kuti akagwire nacho ntchito Zake. Ndicho chida chokhacho mdzanja la Mulungu.

285 Yohane M’batizi, Uthenga wake, wotsogolera Khristu, wophweka kwambiri Iwo unadutsa pamwamba pa mitu wa anthu. Tamvetserani miniti yokha. (Ine ndikuyembekeza ine sindikukusungani inu motalika kwambiri, inu mwaima mozungulira makoma, mwaona.) Taonani! Yohane, pamene... Aneneri onse anachitira umboni za kubwera kwa Mesiya. Mmodzi wa iwo ananena kuti “Mapiri akanadzadumphira ngati ana ankhosa.” Ena anati, “Masamba akanadzawomba mmanja mwawo.” Mmodzi anati, “Malo onse otsika adzakwezedwa, ndipo malo okwera adzatsitsidwa.” Oh, mai! Ndi tsiku lotani!

286 Kodi munaganizira Sukulu ya Aneneri ndi lingaliro laluntha la zimenezo? Oh, mai, iwo anali ndi chirichonse mwapamwamba kwambiri! Koma pamene izo zinachitika, kuchokera ku chipululu kunadzabwera mlaliki wokalamba amene analibe tsiku limodzi la maphunziro mmoyo wake, mwinamwake galamala yake inali yoipa kwambiri. Abambo ake anali wansembe, koma Mulungu anamuchotsa iye kwa izo. (Ife tinali nazo mu phunziro la Lamlungu lapitali.) Sakanamulola iye kusakanizikana ndi zipembedzo zimenezo, ndipo anamutengera iye ku chipululu kuti akamuphunzitse iye Mwiniwake. Ndiwo mtundu wake—ndiwo mtundu umene umakhala ndi Mawu a Mulungu.

287 Anabwera kuchokera ku chipululu, pafupifupi usinkhu wa zaka sarte; ndikuganizira ndevu zakuda zikulendewera pa nkhope yake, yosawoneka bwino; chikopa chachikulu cha nkhusa chokulungidwa momuzungulira iye; anayima mmatope, mpaka mmaondo ake; anati, “Ndine amene ananenedwa ndi mneneri Yesaya.” Ndipo zina za zipembedzo zinatulukira; iye anati, “Musaganize kunena mwa inu nokha, ‘Tiri ndi *ichi* ndi *icho*,’ Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu!” Oh, mai! Bwanji? Iye anali ndi PAKUTI ATERO

AMBUYE! Iye anali ndi Uthenga. Mulungu ananeneratu kuti akubwera. Ndipo chifukwa... Izo zinabwera mu kuphweka chomwecho, Izo zinadutsa pamwamba pa mitu yawo.

²⁸⁸ Pamene Yesu anabwera, Iye anati, “Kodi inu munapita kukawona chiyani, woyankhula waluntha amene angathe kusinthidwa kuchokera ku Methodistu kupita ku Baptistu, ndi kuchoka ku Baptistu kupita ku Presbateria, kuchokera kwa wa Presbateria kupita ku Chipentekoste, ndi Chipentekoste kupita ku chinachakenso? Kodi munapita kunja kukawona bango likugwedezeke ndi mphepo iliyonse? Osati Yohane!” Anati, “Kodi munapita kunja kukawona munthu wovala zovala zofewa?” Iye anati, “Iwo amakhala mnyumba zachifumu, mtumiki wa mtundu umenewo.” Iye anati, “Kodi inu munapita kukawona chiyani, mneneri?” Iye anati, “Woposa mneneri!”

²⁸⁹ Yohane anali woposa mneneri. Ndipo, taonani, iye anabwera wodzichepetsa wa onsewo. Koma iye anali woposa mneneri. Inu mukudziwa chimene Yohane anali? Iye anali mtumiki wa pangano. Ndithudi, iye anali. Iye anapita kupyola mneneri. *Mneneri* ndi mpenyi amene amawona zinthu. Yohane anatero, nayenso, koma iye anadutsa zimenezo. Iye anali mthenga wa pangano. Iye anati, “Eya, uyu ndi amene ananenedwa, ‘Ndidzatumiza wa mthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yako.’” Ndi yemwe iye anali, iye anali wa mthenga wa pangano. Ndithudi. Mwa njira yake yophweka yobwerera, izo zinangowachititsa khungu aluntha.

²⁹⁰ Tsopano ife tikuyenera kutseka posachedwapa, pafupifupi maminiti owonjezera angapo, ndiri ndi zinthu zingapo pano zimene ndikufuna ndinene, Malemba ena ndi zolembe zina.

²⁹¹ Nanga bwanji mkazi wamasiye ali ndi ufa wochepa? Iye anali atafika ku kufooka kwake, iye mwinamwake akanadziphya yekha ndi njala. Analibe ufa. Sakanatha kupita kwina kulikonse ndi kukabwereka ufa, kunalibe aliyense anali nawo uliwonse. Koma iye anafika pa malo, wokhulupirira wamkulu, mwamuna wake anali munthu wopambana wa Mulungu. Ndipo iye anali wamasiye, ali ndi mwana. Ndipo iye anali ndi ufa wodzaza mdzanja, koma iwo unali wokwanira, ndizo zonse zimene ankazifuna; wopatulika mmanja mwa Mulungu, anakhala moyo ndi umenewo kwa zaka zitatu ndi miyezi sikisi, ndi ufa wodzaza mdzanja. Iye anafooka.

²⁹² Iye anatuluka mmawa umenewo kuti akatole nkhu ni ziwiri, ndi kudzazithyola izo ndi kudzaziyika izo pamodzi. Mwaona, ndodo ziwirizo ndi Mtanda. Mukuona? Kuzazithyola... Iye anati, “Ndikatenga nkhu ni ziwiri.” Sananene kuti, “Ndikatenga wodzaza mdzanja,” tsopano, nkhu ni ziwiri zokha. Ndi zimenezotu. Mukuona chiphiphiritsocho?

²⁹³ Ndipo, eya, njira yakale yamakedzana... Njira yoyatsira moto tsopano, ndiyo kutenga zipika ndi kuzisemphanitsa,

nkudzaziyatsa izo pakati. Ndikapita kukapanga kampu, ine . . . mmapiri usiku, kuti ndisazizidwe, ndimayika chipika mbali *iyi* ndi chipika mbali *iyi*, ndipo usiku ndimangokankha kumapeto kwa izo, ndipo zikuwotcha izo monga choncho pamene iwe ukusendeza, mwaona, pomwepo pa mtandawo.

²⁹⁴ “Ndiri ndi nkhuhi ziwiri. Ndikupita kukapanga mkate, kukakonzwa ufa uwu, ufa wodzaza mdzanja, ndi kupanga mkate wa ine ndi mwana wanga. Tidye iwo ndi kufa.” Iye anali kwenikweni mu kufooka, sichoncho iye? Iye anati. . . Ndipo iye anatembenuka ndipo anayamba kuyenda kumabwerera. Oh, mmawa wotentha umenewo! Oh, unali utakhala wautali kwambiri ndiye wopanda chirichonse. Chirichonse. . . Popanda madzi, ndipo anthu akukuwa, anthu akufa, konsekonse; kopanda kobwereka, palibe chochita. Iye anali kumapeto kwa msewu. Iye anali mu kufooka kwake. Iye anati, “Ndikonza iwo wa ine ndi mwana wanga, ndipo kenako tidya ndikufa.” Chotero iye anatembenuka ndipo anati. . .

²⁹⁵ “Miniti yokha!” Iye anayang’ana mmbuyo. Ndipo nkhope yachikale yosawoneka bwino ija ikusuzumira pa chipata kumusi uko, anati, “Pita ukandikonzere ine mkate pang’ono poyamba, ndipo undibweretsere ine.” Oh! “Nditengere ine madzi pang’ono mdzanja lako, ndi chidutswa cha mkate, chifukwa, PAKUTI ATERO AMBUYE!” Oh, mai, umodzi umenewo unachita izo. Oh, mai! Kachidutswa kakang’ono kameneko iye anali nako, mwaona, iye anakapatulira iko kwa Mulungu. Umenewo unali wokwanira kumudyetsa iye nthawi yonseyo. Eya. Mwaona, pamene iye anali wofooka ndiye iye anali wamphamvu.

²⁹⁶ Wina anali ndi mbiya yokhala ndi mafuta pang’ono. Ndipo iye analibe kalikonse, ana ake aamuna awiri akanati agulitsidwe kukakhala akapolo. Iye analibe china chirichonse chimene akanachita ndi mbiya yaying’ono iyi ya mafuta. Sikuti analipo ochuluka, iye anali pamapeto.

Eliya anati kwa iye, anati, “Uli ndi chiyani mnyumba mwako?”

Anati, “Mafuta pang’ono okha mu mbiya.”

Anati, “Pita kwa oyandikana nawo, ukabwereke ochuluka.”

²⁹⁷ Pamene, penyani, akukonzekera izo zisanachitike nkomwe. Hmm? Konzekerani! Davide anamva phokoso limenelo mu tchire la mabulosi. Eliya anawona mtambo waukulu ngati dzanja, anati, “Ndikumva phokoso la mvula yambiri.” Ngati Mulungu atangopeza mbiya zopanda kanthu! Uko nkulondola.

Iye anati, “Dzadzani nyumba ndi izo.” Amen!

²⁹⁸ Mukuona zimene Mulungu amafuna? Mulungu akuyenera kukhala ndi mbiya zopanda kanthu. Mvetserani! Ife takhalapo nacho chiphunzitso chochuluka, zachipembedzo zamkhuu zochuluka, mpaka ife tafika kumapeto kwa dengo. Pali

chinthu chimodzi chokha chimene chatsalira, kutembenukira kwa Mulungu ndi Mawu Ake. Ndipo ngati mungachite zimenezo, mukapeze mbiya zina zopanda kanthu. Mukachotse Chimethodisti chonse mwa iwo, Chipentekoste chonse mwa iwo, ndi Chibaptisti chonse mwa iwo, ndipo mungowalola iwo akhale mbiya, ndi kuwayika iwo mnyumba. Ndipo kenako muchotse kuchokera mu Mbiya iyi ndi kuyamba kutsanulira, ameni, mungoyamba kutsanulira.

²⁹⁹ Iye anali ndi zokwanira kumusamalira iye ndi ana ake, ndi china chirichonse, ndi kulipira ngongole zonse. Bwanji? Bwanji? Basi zochepa zimene iye anali nazo, zopatulidwira kwa Mulungu, ndi kumatsatira mawu a mneneri uyu, iye anatulukira wabwino.

³⁰⁰ Mulungu, titumizireni ife mneneri amene adzatenge Mawu a Mulungu, amene sadzatenga *chinachakenso*, koma kungotenga mbiya zopanda kanthu. Ngati Mulungu atangotenga mbiya zopanda kanthu, ndipo kenako nkutenga Mawu a Mulungu ndi kuwatsanulira Iwo mwa munthuyo.

³⁰¹ Osati ena kudzati, “Oh, ine ndinagwedezeka pamene ndinaulandira Iwo. Ine ndinayankhula mmalirime pamene ndinaulandira Iwo. Ine ndinavina mu Mzimu.” Iwalani zimenezo, mwaona, iwalani zimenezo!

³⁰² Mungokhala pamenepo mpaka Iwo utabwera, ndizo zonse, mpaka mbiyayo idzaze. Ndi zimenezotu. Umo ndi momwe mumachitira izo. Inde, bwana, kuphweka kwa Iwo! “Mbiyazo zinadzaza,” momwe tingakhalire pa zimenezo!

³⁰³ Anali ophunzira, onse atakhumudwa tsiku lina, Yesu anati kwa iwo, anati, “Pali anthu faivi sauzande pano,” ndipo anati, “iwo akulefuka, ali ndi njala.” Oh, ine ndikhoza kukhala pa zimenezo ora lina. “Faivi sauzande, ali ndi njala,” pali handirede billioni ali ndi njala!

Anati, “Atumizeni iwo azipita.”

Anati, “Palibe chifukwa chochitira zimenezo.” Anati, “Inu muwadyetse iwo.”

³⁰⁴ Oh, mai! Ndikulungalira akusonkhanitsa zonse zimene akanapeza, ndipo inu mukudziwa pamene anasonkhanitsa (chirichonse) anaziwunjika izo. . .Ndikhulukireni kufotokozaku, “anaziwunjika.” Koma iwo anapeza chirichonse, iwo anati, “Tsopano, apa, tadutsa msasa wonse. Ife tiribe ndalama, chotero sitingakhale ndi msonkhano.” Inu mukuona? “Chotero ife tiri ndi chirichonse pano, koma chinthu chokha chimene ife tingachipeze ndi mabisiketi asanu aang’ono ndi nsomba ziwiri zazing’ono za kamwana” monga Davide, anabwera kuchokera ku chipululu uko. “Ndizo zonse zimene tiri nazo. Ndizo zonse zimene tingazipeze. Ife tiri kumapeto kwa nzeru zathu. Sitingachite china chirichonse, Yohane.” Petro anati, “Ndizo zonse zimene tingachite. Ndizo zonse zimene

tingachite. Ife tiri kumapeto kwa nzeru zathu. Ndicho chinthu chokhacho mu mzere wa chakudya chimene ife tiri nacho.”

³⁰⁵ Chabwino, ine ndikhoza kungotenga Lemba limodzi laling’ono, Machitidwe 2:38, ndipo ndizo zonse zimene ife tikuzisowa, kungomvera Ilo. Inu simukusowa kuti muphunzire maseminare, zonse za *ichi*, *icho*, *chinacho*, mungotenga Ilo. Eya, basi—mungotenga Ilo, ndizo zonse zimene mukuzisowa, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu muzadzazidwa ndi Mafuta.” Mukuona? Mungodzikhuthula, mukonzekere Mmodziyo, ndizo zonse zimene muzikusowa. Mungoyika dontho mmenemo, muwone ilo likudzaza.

³⁰⁶ Inu mukudziwa, sizinali zokwanira mu mbiyayo kuti apange dontho mu chirichonse. Mwinamwake anatenga chala chake, monga *chonchi*, anangogwetsera iwo mu chimodzi monga choncho; atayang’ana m’mbuyo ndipo inali itadzaza. Anangogwetseramo iwo, mwaona, ndizo zonse zimene iye amasowa, chifukwa iwo anali mafuta odalitsika.

³⁰⁷ Musatengere zochitika zina zaku seminare. Mutenge Mawu a Mulungu ndipo muwagwetsere Iwo mmenemo, muwone momwe iwo ati adzadzire.

³⁰⁸ Iye anati, “Chabwino, kodi ife tikuyenera kupanga dontho la mtundu wanji? Mwinamwake ife tikhoza kutenga chinachake kuchokera mu Masalmo.”

³⁰⁹ Mutenge chimene ndakuuzani inu, “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo mudzadzazidwa ndi Dontho limenelo.” Mungogwetsera izo mmenemo, ndipo inu mudzadzazidwa ndi Dontho limenero. Ndiro Dontho limene Petro anagwiritsa ntchito pa Tsiku la Pentekoste. Ndiro Dontho limene Paulo anagwiritsa ntchito. Ndiro Dontho limene ophunzira onse anagwiritsa ntchito. Zina zonsezo zidzawonjezedwa, inu mungotenga Dontho limenelo ndi kutsatira izo, ndipo zina zonsezo zidzakhala bwino.

³¹⁰ Khalani ofooka! Khalani opanda kanthu! Khuthulani zonse, ndipo kuyambira pamenepo izo zidzapitirira kumagwa, ndipo Mulungu adzapanga kugwa konseko. Inu musingochita zimenezo. Inu mugwade pa maondo anu ndi kulandira izo ndi mtima wanu wonse. Mugwade mu mtima mwanu pompano ndikuti, “Mulungu, ine ndikukhulupirira Izo, ndi mtima wanga wonse!” Mulungu adzasamalira madontho ena onse, mudzadzazidwa, “Inu mudza- . . . dzazidwa ndi Mzimu Woyera.”

³¹¹ Tsopano iwo anali ndi mabisiketi asanu aang’ono ndi nsomba ziwiri. Chotero iwo akanati achite chiyani? Chotero iwo anabwera ndipo anati, “Izi ndizo zonse zomwe tingathe kuzisonkhanitsa. Ife tiri kumapeto kwa nzeru zathu. Ife sitingapeze chidutswa china cha mkate kulikonse, palibe

aliyense. Ndipo mnyamata wamng'ono uyu, mwinamwake akuwonetsera . . . atathawa kusukulu, anapita kusukulu mmawa uno, ndipo anaphonya sukulu ndipo anapita kukawedza kumusi kuno. Ndipo ife tinakamunyamula iye kumusi kuno pa mtsinje, iye anabwera kuti adzamvetsere. Ndipo, apo, ali ndi zisanu." Zikomo Mulungu chifukwa cha kamnyamata kameneko! Inde, bwana. Anati, "Ife . . . chinthu chokha chimene ife tiri nacho mu mzere wa moyo ndi dontho laling'ono ili apa." Anati . . .

³¹² Yesu anati, "Izo ndizokwanira. Bweretsani izo kuno." Mukuona? "Bweretsa iwo kuno, undilore Ine ndikhale nawo iwo. Undilore Ine ndikhale nalo dontho pang'ono limenelo, ine ndisamalira zina zonsezo. Tsopano, udingopitirira kumapereka pamene Ine ndizikupatsa iwe kuchokera mu dontho ili."

³¹³ Ndipo aliyense wa inu atenge dontho la Machitidwe 2:38 mmawa uno, mu mtima mwanu, ndipo mungotenga kuchokera pamenepo ndi kumamuyang'ana Iye akuyamba kunyemera Mkate wa Moyo kwa inu. Lapani, batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo kenako muwone ngati Mzimu Woyera sugwera mkati, kupitirira kumagwera pa *ichi* ndi kugwera pa *icho*, kugwera *apa* ndi kugwera *apo*, ndi kugwera *apo*, ndipo padzakhala kudzazitsidwa kwa Mzimu Woyera! Kulondola!

³¹⁴ Inu simukusowa kuti mupite ku maseminare. Simukusowa kuti mukhale anzeru. Chinthu chokhacho chimene inu mukuyenera kuchita ndi kuzindikira kuti simukudziwa kalikonse. Mulole Mulungu akugwiredi inu, Iye adzasamalira zina zonsezo.

³¹⁵ Chabwino, kenako Liwu linati, "Bweretsa izo kuno." Ndicho chimene Mulungu akufuna mmawa uno, kuti timubweretsere Iye mulu wa mbiya zopanda kanthu. Iye adzasamalira zina zonsezo. Inde, bwana.

³¹⁶ Bartumeyo wakhungu atakhala pafupi ndi chipata, atatheratu, atazidwa, oh, mphindi yake yofooka kwambiri, pamene iye anamva Liwu, linati, "M'bweretseni iye kuno." Uko nkulondola, iyo, nthawizina, imakhala nthawi yako yofooka kwambiri.

³¹⁷ Panali Mariya ku mandako, atasweka mtima, Mwana wake, Mnyamata wake anali ataphedwa, chirichonse, ziyembekezo zonse zinali zitapita. Ndipo iye anapita kuti akamukonze Iye, ndipo ngakhale thupi Lake silinali mmenemo. Ndipo iye anamva Liwu likuti, "Iwe ukulira chifukwa chiyani, mkazi?"

³¹⁸ Iye anati, "Iwo amuchotsamo Ambuye wanga. Ndipo ine. . ." Kanthu kakang'ono kosauka, anali Mwana wake amene anali atachititsidwa manyazi; anamuvula Iye maliseche ndi kumupachika Iye pamwamba apo pa Mtanda, ndipo anamupachika Iye ndi kumukhomera Iye pamwamba apo, Iye atatha kudzinenera kuti anali Mesiya, mkaziyo atatha kudziwa

kuti Mzimu Woyera unamuphimba iye ndi kumubweretsa Mwana uyu. Anali Mwana wa Mulungu. Iye anali ataona ntchito Zake, ndi chirichonse, ndipo anawona pa mphindi yofooka kwambiri. . .

³¹⁹ Ndipo pamenepo Yesu anali ataimirira motsutsana ndi woyipayo, anaima motsutsana ndi mabungwe amenewo, anaima motsutsana ndi Afarisi amenewo; ndipo anadzakhala wofooka ndipo anadzipereka Yekha ku imfa, ndipo anafa monga wochimwa pa Mtanda, atasenza machimo athu. Masalmo omwewo, aneneri omwewo amene iwo ankawakhulupirira, anali atabwereza (mahandirede a zaka mmbuyomo) Mawu omwewo amene Iye ananena pa Kalvare, ndipo iwo analephera kuziwona izo. Mkulu wawo wamkulu-. . .

³²⁰ “Mulungu wanga,” anatero Davide, “Mulungu wanga, chifukwa chiyani Inu mwandisiya ine?” Masalmo 22, “Mafupa anga onse, akundiyang’ana ine, palibe ngakhale limodzi lomwe lathyoka. Iwo amagwedeza mitu yawo ndi kunena, ‘Iye anadalira ena. . .Iye—Iye anapulumsa ena, Iyemwini Iye sakutha kudzipulumutsa.’” Ndipo zinthu zonse zimene aneneri ananena, zinali pomwepo! Ndipo Yesu, akufa, atagwira Mawu amenewo, anadzipereka Yekha. Mulungu, Emanuele, anadzakhala wofooka kwambiri mwakuti Iye anadzipereka Yekha ku imfa, ndi ku manda, ndi moyo Wake ku gehena. Kufooka! Koma kuchokera mu kudzipereka kwathunthu uko. . . kunadzabwera mmawa wa Isitara uja, ukukhota njira Yake kuchokera kwa wotsikitsitsa.

³²¹ Iye anali Wapamwamba kwambiri, ndipo anadzakhala wotsikitsitsa. Iye anabwera kwa anthu otsikitsitsa, anapita ku mzinda wotsikitsitsa. Ndipo munthu wamng’ono kwambiri mu mzinda ankachita kumuyang’anira Iye pansi. Anapita kuchokera kumeneko kupita ku imfa, ndipo kuchokera ku imfa anapita ku manda, ndipo kuchokera kumanda anapita ku gehena; mpaka kwa wotsikitsitsa amene akanakhoza kufikiridwa, ku gehena yotsikitsitsa imene ikanakhoza kuganiziridwa, Iye anapita kwa iyo.

³²² Komano, kuchokera pamenepo, Mulungu anayamba kumukweza Iye mmwamba. Kudutsa Paradiso, kuchokera kumeneko kupita ku—kumanda, ndipo kuchokera kumanda kupita ku Ulemelero, ndi Mmwamba kwambiri mwakuti Iye amayenera kuyang’ana pansi kuti awone Kumwamba. Anakwezera mipando Yake yachifumu Kumwamba!

³²³ Mayi wamng’ono wosweka mtima uja, wosadziwa ichi, atayima pamenepo, “Iwo amuchotsa Ambuye wanga, ndipo ine sindikudziwa ndikuti.” Iye anali. . . ora lofooketsetsa limene iye anayamba wakhalapo nalo. Wake—Ambuye wake anali atapita. Iwo anali atamupachika Iye, komabe Iye analola izi. . . anamupachika Iye mwa manyazi a kumupachika Iye pamwamba

apo wamaliseche pamaso pa anthu amenewo; ndipo anamubaya Iye mnthiti, ndipo akuwukha magazi, ndi kumumva Iye akulira pa Mtanda, ndi kuwona dziko likugwedezeke, ndipo miyamba yonse inazindikira kuti Iye anafa. Anamutsitsira Iye pansi, atawuma ndi wozizira, ndipo anakamugoneka Iye mmanda. Iye anaganiza, “Ulemu wotsiriza umene ine ndingachite kwa Mwana wanga wokondedwa ndi kubwera ndi kudzamukonza Iye, ndipo tsopano iwo amuchotsapo Iye.” Ndipo iye anali atayima pamenepo akulira, mayi wamng’ono ameneyo atayima pamenepo akulira, akusisima. Oh, mphindi yofowoketsetsa kwambiri!

“Iwe ukulira chifukwa chiyani, mkazi?” linali Liwu kumbuyo kwake.

³²⁴ Iye ankaganiza kuti anali wosamalira kumanda, anati, “Oh, iwo amuchotsapo...” Sanathe ngakhale kutembenuka, anali atafooka kwambiri. Iye anati, “Ndakhala ndiri maso masiku atatu onsewa ndi usiku. Ine ndinaima ndi kumayang’ana kupachikidwa, ine ndinamuona Wokondedwa wanga yemwe amene ine ndikudziwa kuti anali Mwana wa Mulungu. Ine ndikudziwa Iye anali! Ndipo komabe iwo...” (Akuyang’ana mbali inayo, ndi Iye ali kumbuyo.) “Ndipo iwo amuchotsapo Iye ndipo anamupachika Iye. Ine ndinamuwona Iye akuwukitsa akufa kuchokera mmanda. Ine ndinamuwona Iye akuchita zozizwitsa pambuyo pa zozizwitsa. Ndipo ine ndikudziwa Mzimu Woyera... Mulungu akudziwa mtima wanga, ndinali wosalakwa pa chirichonse, ndipo Mzimu Woyera unandipatsa ine Mwana ameneyo popanda kumudziwa mwamuna. Momwe ine ndikudziwira kuti izo zinali zoono! Ndipo ine ndinamuwona Iye atachititsidwa manyazi ndipo... kumuvula zovala Zake pa Iye, ndi kumupachika Iye pamenepo ndi kumukwapula Iye. Iye anafa imfa yowopsya kwambiri. Ine ndimamukonda Iye, ine sindikusamala chimene chachitika kwa Iye. Ine ndikufunabe kumuyika Iye mmanda, ine ndikufuna—ine ndikufuna kuti ndimupatsa Iye mtundu woyenera wa kuikidwa mmanda, ndipo iwo amuchotsapo Iye. Ndakhala masiku ndi masiku, mtima wanga ndi wosweka. Ine ndangoyima mu chikhalidwe ichi. Ine sindikudziwa chimene iwo achita ndi Ambuye wanga.”

³²⁵ Iye anati, “Mariya.” Ndipo kenako iye anakhala wamphamvu. Amen! “Pita ukauze ophunzira Anga kuti ndikakumana nawo ku Galileya.” Oh, mai!

³²⁶ Mu kufooka ndiye timapangidwa kukhala amphamvu. Ukakhala wofooka, ndi pamene umakhala wamphamvu.

³²⁷ Petro, iye atatha kukhala kunja uko akuwedza, iye anali... ntchito yake inali kuwedza. Ndimachita ngati ndimaikonda ntchito yake. Ndipo chotero, iye anali kunja uko akuwedza, atakhumudwitsidwa, akudziwa kuti iye anali atamukana Khristu. Oh, mai! Anamva Mneneri uja atayima pamenepo

ndipo akumuza iye kuti, “Petro, kodi iwe umati umandikonda Ine?”

³²⁸ Iye anati, “O Ambuye, Inu mukudziwa ine ndimakukondani Inu.” Iye anati, “Ndimakukondani Inu. Ndine wokonzeka kukuferani Inu.”

³²⁹ Iye anati, “Petro, iwe ukuganiza kuti ukutanthauza zimenezo, koma iwe udzandikana Ine katatu..Iwe udzandikana Ine tambala asanalire kachitatu. Mwaona, udzandikana Ine katatu tambala asanalire.”

³³⁰ Ndipo powona kuti izo zinadzachitika, pamene iye anayima pamene ndipo anati “Ine sindikumudziwa Iye. Ayi, ine sindikudziwa kalikonse ka iwo kumeneko Achipentekoste.”

³³¹ Ino si nthawi yoti ndisiye kulalikirira, ndi wotchi yanga yomwe ili ndi vuto. [Alamu pa wotchi ya M'bale Branham inalira—Mkonzi.] Mukuona? Ananena kuti, “Ine—ine ndikudziwa..” Ine—ndikuyenera kuyima tsopano, koma ine—sindingayime pompano, mwaona, chotero ine ndikuyenera kuti ndimalize izi apa miniti yokha.

³³² Anati, “Ine—ine—ine—ine ndikudziwa ndinamukana Iye. Ine ndinamukana Iye pamaso pa Pilato. Ine ndinamukana Iye mu kukhalapo pamene mkazi wamng’ono uja anabwera mondizungulira ine, anati, ‘Kodi iwe si mmodzi wa iwo?’ ‘Ayi!’ Ndipo ngakhale kunyozala!” Oh, iye anali mu mawonekedwe oyipa. Anati, “Ine—ine—ine...” Iye anakana..Iye anali atamukana Iye. Ndipo anali atamuwona Yesu atayima ndipo anadzamuyang’ana, pamene ndi pamene tambala anadzalira, anadzayang’ana pa Petro. Iye anatuluka. Oh, iye anakhumudwitsidwa ndi iyemwini, anati, “Kodi ndikukhalanso ndi moyo chifukwa chiyani?”

³³³ Ndipo kenako, pambali pa zimenezo, iye anati, “Ndikuganiza kuti ndibwerera ndi kumakawedzanso. Sindingathenso kumalalikirira, chotero ndidzangobwerera ndi kumakayamba kuwedza.” Iye anali ataponyera maukonde ake ndipo ataponya usiku wonse, sanapeze nsomba. Ndipo iye anali pa malo ofooka, iye analibe kanthu, anakhumudwa ndi iyemwini, anafika kumapeto kwa kuthekerera kwake.

³³⁴ Chabwino, iye ankaganiza kuti iye anali munthu wopambana, anadula makutu a mwana wa wansembe wamkulu monga choncho. Chabwino, iye ankaganiza kuti iye anali munthu wopambana, inu mukudziwa, iye anali ataphunzira chinachake. Koma iye sankadziwa kanthu! Iye ankayenera kuiwala zonse za izo.

³³⁵ Ndipo apo iye anali kunja uko, anati, “Chabwino, ine ndikudziwa chinthu chimodzi, ndine nsodzi. Ndikhozabe kupeza zofunika pamoyo, ndi kuwedza.” Iye anaponya usiku wonse ndipo sanapeze kalikonse. Oh, zokhumudwitsa bwanji! Nthawi iliyonse akakoka iwo, ukonde wopanda kanthu. Ndipo iye anali

wokhumudwa kwambiri! Iye anali pamalo ofooka kwambiri, anati, “Ine ndikhoza kungomverera ngati ndilumphe kuchoka mu ngalawa iyi. Ine ndiribe kanthu, mulimonse.”

Iye anati, “Kodi muli ndi nsomba iliyonse, ana?”

³³⁶ Anayang’ana kunja ku gombe, ndipo apo panayima Mwamunayo. Iye anati, “Ayi, tagwira ntchito usiku wonse ndipo sitinapeze kanthu. Ine ndimaganiza kuti ndine nsodzi.”

“Kodi ndi iweyo, Simoni?”

³³⁷ “Eya. Chabwino, ndagwira ntchito usiku wonse osagwira kalikonse. Oh, ine—ine . . . Ife tiribe nsomba pano.”

Iye anati, “Chabwino, ponyerani khoka lanu mbali inayo.”

³³⁸ “Ife tachita . . . Chiyani?” Ndiye iye- . . . Anati, “Kumbali inayo? Ife takhala tikuchita zimenezo!”

“Ponyani ilo kumbali yinayo.”

³³⁹ Iye anaponyera makhoka ake kumeneko, ndipo iye anakoka. Iye anati . . . Kenako anadzakhala wamphamvu. Oh, mai! Iye anatenga chikhotho chake chakale cha nsomba ndipo anachivala icho modzikutira iye, anati, “Abale, Uyo ndi Iyeyo!” Ndipo anawaposa ena onsewo waku gombe, iwo asanakocheze ngalawazo mwamsanga momwe iwo akanathera, iye anasambira kuwaposa iwo, atavala chikhoto cha nsomba, anafika ku gombe. Chifukwa chiyani? Pamene iye anali wamphamvu. Pamene iye anali wamphamvu sakanatha kuchita kalikonse, koma pamene anafooka ndiye anadzakhala wamphamvu. Inde, bwana.

³⁴⁰ Oh, njira ya Mulungu ndi kutenga zotengera zopanda kanthu za anthu ndi kugwedeza nazo dziko lapansi. (Tsopano, pang’ono pokha ndipo ife tizipita.) Monga pa Pentekoste, pa Pentekoste, kodi Iye anachita chiyani? Zinawatengera iwo masiku teni kuti akhale opanda kanthu. Koma iwo onse anali atayima pamenepo ndi zotengera zawo zitatembenuzidwira mmwamba, ndipo Mulungu anadzitenga Iyemwini ndi kuzidzaza izo. Ndizo zonse! Iwo anagwedeza dziko; anadzitsanulira Yekha mwa iwo.

³⁴¹ Ndicho chimene chiri chosowa cha lero. Ndicho chimene ife tikuchisowa lero, ndi zotengera zopanda kanthu, inde, bwana, kuti Mulungu akhoze kuzidzaza izo. Ndipo simungathe kuwatenga iwo . . . Ndikuyenera ndilambalale zambiri apa. Mulungu sangathe kuwagwiritsa iwo ntchito ngati iwo adzazidwa kale. Ngati ndiwe wozadza ndi maphunziro a fioloje, Mulungu sangakhoze kukugwiritsa ntchito. Mulungu ayenera kukhala ndi zotengera zopanda kanthu kuti *Iye* athe kuzidzazitsa izo.

³⁴² Tsopano, Eliya sananene kuti, “Pita ukatenge mbiya zina ndipo ukabwereke mafuta ambiri, ndipo tiwona ngati sitingapeze mtengo wabwino wogulitsira, ndipo iwe ukapeze zochulukirapo pang’ono ndipo iwe ukhoza kumubwezera

woyandikana naye monga choncho.” Iye anati, “Ukangotenga zotengera *zopanda kanthu*. Ndizo zonse zimene ukusowekera.”

³⁴³ Ndi chimene chinali pa Pentekoste, iwo anali ndi mbiya zopanda kanthu kuti Mulungu akhoze kuzidzaza izo. M’bale, tsiku ili likufuna zimenezo. Lero; mukuyenera kukhala ndi chimenecho. Tidzakhala ndi chimenecho kapena tiwonongeka. Ndikutseka tsopano, mvetserani. Ife tikuyenera kukhala nacho icho kapena tiwonongeka. Inde, bwana.

³⁴⁴ Makina aakulu achipembedzo amene ife tiri nawo, makina aakulu a mpingo achita utsi, iwo agumuka mwauzimu mwa iwo. M’bale Collins ali penapake pano, ndi M’bale Hickerson. Ndikuganiza kuti krankishafiti yawonongeka. Chinachake chalakwika. Iwo akugwiritsa ntchito mafuta amtundu wolakwika, iyo yonse yachita utsi. Iwo akugwiritsa ntchito chowachitikira cha ku seminare mmalo mwa Mzimu Woyera.

³⁴⁵ Zitsitsimutso zathu zazikulu za mdziko, munthu wathu wamkulu, misonkhano yathu yamachiritso, zonse zalephera. Ife tikudziwa izo zatero. Tayang’anani pa mlaliki wathu wolemekezeka, Billy Graham, wadutsa fukoli mmbuyo ndi mtsogolo, mmbuyo ndi mtsogolo, mmbuyo ndi mtsogolo. Izo zachita ubwino wanji? Oral Roberts, misonkhano yamachiritso konsekonse, ndipo zikuipiraipira nthawi zonse.

³⁴⁶ Chifukwa zonsezo ndi Baptisti, Presbateria, Assemblies of God, mabungwe ena onse osiyanasiyana awa, kuwabweretsa iwo onse pamodzi, ndi chiyani icho? Makina aakulu achipembedzo, ndipo Mulungu wakudzazitsirani izo ndi utsi. Tsopano iwo ukungogwedera, “kugwedera,” kupopa, kupopa, kupopa, “kugwedera,” kupopa, kupopa, kupopa, pang’ono pokha apa ndi apo. Iwo watha! Iwo watheratu! Mafuta athamo, mwathiramo madzi mmenemo. Chirichonse chapita (inde, bwana), matayala aphwa mbali ziwiri zonse. Ife tiri mu chikhalidwe choyipa. Makina achipembedzo ayima.

³⁴⁷ Ndipo, m’bale, chivindikirocho chinachokapo pa gehena. Uko nkulondola. Ndipo mitsinje ya mphamvu ya ziwanda ikutsanulira kuchokera konsekonse. Izo zagonjetsa mafuko. Izo zagonjetsa ndale mpaka zavunda mpaka mkati. Izo zagonjetsa mipingo mpaka iwo sakudziwa kanthu koma chipembedzo.

Iwe ukati, “Kodi ndinu Mkhristu?”

“Ndine wa Methodist.”

“Kodi ndinu Mkhristu?”

“Ndine—ndine wa Pentekoste.”

³⁴⁸ Zimenezo sizikutanthauza mochulukanso, monga ndinanena tsiku lina, kuposa kukhala nkhumba, kapena nguluwe, kapena kavalo, kapena chinachake. Izo ziribe kanthu kochita ndi Iwo. Iwe umakhala Mkhristu pamene wabadwanso mwatsopano ndipo wadzazidwa ndi Mzimu Woyera, osati mpaka

chimenecho, ndipo wadzipereka kwathunthu kwa Mzimu. Ngati sunadzipereke kwa Mzimu, ndiye kuti sunabadwense mwatsopano ndipo ulibe Mzimu Woyera. Iwe ukhoza kuyankhula mmalirime ndi kunjenjemera, ndi kulumpha ndi kuthamanga, ndi kuchita mitundu yonse ya . . .

³⁴⁹ Paulo anati, “Ndikhoza kusuntha mapiri ndi chikhulupiriro, ndikhoza kuchiritsa odwala, ndikhoza kukhala ndi chidziwitso cha m’Baibulo, Ndikhoza kupita ku seminare ndi kukaphunzira zinthu zonsezi, chirichonse,” anati, “Sindine kanthu komabe!” Aleluya!

³⁵⁰ Oh, mai, kuyankhula za chivindikiro kuchoka pa ketulo! Ziwanda zikuyendayenda, mphamvu za mdierekezi, pansi pa dzina la Chikhristu, “kuphunzitsa Chiphunzitso malamulo a anthu,” ziphunzitso zaumulungu zakuseminare, kulisiya Baibulo lokha.

³⁵¹ Aleluya! Ndani angathe kutero, wamphamvu mokwanira nndani, nndani ali ndi nzeru? Ndani ali ndi mphamvu zokwanira kuti awete gulu ili limene likuvula zovala za akazi athu, mu dzina la alaliki, Amethodisti, Abaptisti, ndipo ngakhale Achipentekoste? Kumapenta nkhoze zawo monga Yezebeli, ndi kumadula tsitsi lawo, ndi kumavala mathalauza monga amuna. Alaliki athu, osakwanira kuti angawadzukire iwo kuti awawuze iwo za izo. Ogwidwa ndi mdierekezi! Linali gulu limene linang’amba zovala zake pa iye. Kodi mdierekezi wobangula uyu ndi ndani?

³⁵² Ndani ali wamphamvu mokwanira? Ndi mtundu wanji wa—wa chipembedzo umene uli wokhoza kumugonjetsa iye akuyendayenda kudutsa pa manda awa a zipembedzo, akufuula, “Masiku a zozizwitsa anapita, ndipo ife sitikuwufuna Mzimu Woyera”?

³⁵³ Ndipo ndani angamuwete mdierekezi ameneyo? Mulungu! Ife sitingachite izo ndi chipembedzo. Ife sitingachite izo ndi mphamvu zachipembedzo. Koma panali Liwu nthawi ina limene linachita izo, ameni, limene linawaweta adierekezi amenewo, kuwaika iwo mmalingaliro awo olondola ndi kuwaveka iwo zovala. Liwu lomwelo limatipatsa ife lonjezo, “Ntchito zimene Ine ndikuchita inunso mudzazichita.” Inu simudzachita konse izo pansi pa mafuta achipembedzo mu galimoto yodzaza utsi. Inu simudzachita konse izo mu bungwe. Inu mudzachita izo pamene mwadzikhuthula ndipo mwadzakhala ofooka, dzikhuthuleni yense nokha, ndipo mulole Mzimu Woyera ubwere mkati ndi kudzawulutsa gawo lililonse la inu, kudzasungunula chivindikiro chirichonse cha thupi lanu. Ndizo zokhazo . . . chitani izo. Ife sitikusowa bungwe latsopano.

³⁵⁴ Chimene ife tikusowa, O Mulungu, ine ndikumverera Iwo ukutsanulidwa mozungulira kudutsa pano tsopano. Chimene ife tikuchisowa ndi mneneri wa Mulungu kuti adzuke ndi bingu la

Mulungu, mphenzi zauzimu zimene zidzagwedezere dziko lino ku manyazi! Aleluya! Zotengera zopanda kanthu ndi chimene Iye akusowa, ndiko kulondola, Mpingo woitanidwa utuluke, gulu lapang'ono limene liti lidzalandire mphamvu ya Mulungu ndi madalitso ndi Uthenga Wake. Aleluya! Ndi zimene ife tikuzisowa.

³⁵⁵ Mukhale ofooka kuti mukhale amphamvu. Izo zidzagonjetsa mdierekezi aliyense. Zidzachititsa manyazi ophunzira. Izo zidzabweretsa amuna ndi akazi amene Mulungu wawaitana, ndipo izo zokha.

³⁵⁶ Kumbukirani, “Monga zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu, miyoyo eyiti inapulumutsidwa.” Mmasiku a Eliya panali seveni sauzande okha amene anali ndi Iwo. Oh, tangoganizani za kumene ife tikukhala tsopano. Pamene Yohane anabwera powonekera, mpingo wawung'onowo unali ndithudi mu kagulu kochepe, koma panali mbiya zopanda kanthu zoti zitsanuliridwe Mafuta. Aleluya!

Mulungu, tiloleni tidzikhuthule tokha.

³⁵⁷ Tikhale opanda kanthu, abwenzi. Tikhale ofooka! Mukane kuthekera kwanu komwe! Ndipo inu uko pa wailesi...osati wailesi, koma kunja mu...amene adzamvetsere matepi awa, kulikonse kumene iwo abwera, dzikhuthuleni nokha. Dzitsanulireni nokha pa guwa la nsembe la Mulungu ngati nsembe. Mulole Mngelo abwere ndi khala la Moto, adzaze mbiya imeneyo ndi mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse. Pezani...Ndiye Iye adzakupangani inu amphamvu, Iye adzakupatsani inu chisomo kuti muyime.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa miniti.

³⁵⁸ O Ambuye, mmawa wina wa Lamlungu wadutsa, ndipo ife takhala tikukhala mu msonkhano waulemu uwu, mmene amuna ndi akazi amene amakudziwani Inu, pamene Mzimu Wanu umakhala mkati mwa mitima yawo, ndipo iwo akukukhulupirirani Inu ndipo achita pa Mawu aliwonse amene Inu—amene Inu munatilamulira ife kuti tizichita. Ndipo tikukuthokozani Inu chifukwa cha anthu awa.

³⁵⁹ Ndipo pakhoza kudzakhala ena kunja ku dziko kumene matepi awa ati adzapite, kumene akazi aang'ono odzichepetsa ndi amuna adzawatengere iwo mnyumba ndi mmafuko ndi kunja mmaiko ena. Ndipo mulole iwo akamve, Ambuye, ndi kumvetsa, akadzikhuthule okha kuti Mzimu Woyera ukathe kuwadzazitsa iwo.

³⁶⁰ Pakhoza kukhala ena ngakhale pano mmawa uno, Ambuye, amene angati...adzikhuthula okha kuyambira pamene tinayamba kuyankhula, amene azindikira kuti adalira kwambiri mu maganizo awo omwe, awo eni ake, iwo...kuthekera kwawo, kudalira mu—kuchenjera kwa maganizo awo ophweka a

umunthu, omwe sali kanthu koma nyansi pamaso pa Mulungu. O Mulungu, mulole iwo angodzikhuthula okha tsopano, modzichepetsa adzipereke okha ndi kubwera ku kudzadzidwa ndi Mzimu. Perekani izi, Ambuye.

Zinanenedwa mu Baibulo, “Onse amene anakhulupirira anabatizidwa.”

³⁶¹ Pakhala mchipinda chino mmawa uno, Atate, mkazi wamng’ono, wakhala kuno kumbuyo, ndipo ine ndikukumbukira Akazi a Hicks akubwera akunditsatira ine usiku wina ndipo apo iwo anakhala pansi opanda kalikonse koma mafupa, mtsempha, khungu laling’ono la mtsempha litakokeka pa iye, khansa inali itamudya iye; mwamuna wake, sanali Mkhristu pamenepo. Ndipo ndikukumbukira pemphero limene ndinapemphera usiku umenewo: “Mulungu, Inu munatumiza Davide wamng’ono kuti atsatare mkango ndi legeni yophweka yaing’ono, ndipo iye anabweretsanso mwanawankhosa.” Ine ndinati, “Khansa iyi yamugwira mlongo wanga; iye ndi mdierekezi. Ine ndikudziwa Inu ndi Mulungu. Ine ndakuwonani Inu, Ambuye, ndipo ine ndikudziwa. Ine ndayankhula ndi Inu, ndipo Inu mwayankhula mondiyankha.” “Ine ndikutsatira nkhosa ya Mulungu; khansa, iwe umumasule iye!” Ndiye ndinamulamulira iye mu Dzina la Yesu Khristu kuti “Apite kunyumba.” Ndipo mwamuna wake, yemwe anali asanadzipereke, anakhulupirira Mawu amenewo ndipo anamutengera mkazi wake kunyumba. Ndi uyu apa mmawa uno, mkazi wopambana wamphamvu wathanzi, khansa inapita, iye akubwera mmawa uno kuti adzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. O Mulungu, zikomo Inu chifukwa cha chotengera chopanda kanthu icho chimene chakonzeka kuti chidzazidwe. Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mudalitse moyo umenewo.

³⁶² Ambuye, ichi ndi chitsanzo chabe cha ena ambiri. Ine ndikupemphera kuti madalitso Anu akhale pa omvetsera awa, mwaulemu, Mulungu, mwaulemu. Ngati . . .

³⁶³ Pali chinthu chimodzi chokha chatsalira, Atate, chimene ine ndikuchiwona, ndiko, mwina Inu mudzawuka kwinkwaka ndi zotengera zopanda kanthu ndi kulipangitsa dziko ili kudzichitira lokha manyazi, kapena mutumiza Yesu mwamsanga kumene. Kuti mapeto ali pano, Ambuye, kwatsala zinthu ziwiri zokha kuti zichitidwe (ndipo tikuyenera kuziwona nthawi yomweyo) pakuti tikudziwa kuti tiri kumapeto; mwina ife tidzawona chinachake champhamvu chikuwuka nthawi yomweyo, kapena ife tidzawona Kudza kwa Ambuye.

³⁶⁴ Mauneneri onse akwaniritsidwa. Chinthu chotsiriza Mpingo usanaukitsidwe, Iwo usanatengedwere mmwamba mu Chivumbulutso mutu wa 3, kunali kubwera kwa mthenga ku M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, amene akanati

“adzatembenuze mitima ya anthu kubwerera kwa makolo oyambirira,” kuwatengera iwo mmbuyo ku Pentekoste wamba, chimene iwo amadzinenera kuti ali nacho. Padzakhala masauzande kuchulukitsa masauzande, monga zinaliri mu tsiku la Nowa, Ambuye, amene adzatayike. Ambiri a iwo akanadzataika. Ife tikuwona izo zakwaniritsidwa kale, Atate.

³⁶⁵ Bwerani, Ambuye Yesu, dzatengeni Mpingo Wanu. Ndipo ngati icho chiti chikhale chifuniro Chanu, Ambuye, Mpingo umenewo usanakwatulidwe, mulole kuti pawuke Mphamvu. O Mulungu, zidzazeni mbiya izi. Adzutseni iwo, Ambuye! Ligwedezeni dziko lino kamodzinsola! Ife tikudziwa kuti idzakhala itadutsa nthawi, sipadzakhala kulapa pamenepo, izo zidzakhala kutali kwambiri kwa iwo pamenepo. Koma onetsani Mphamvu Yanu, Ambuye, dzazani mbiya zimenezo ndipo ligwedezeni dziko ili ngati silinagwedezekepo! Tengani Mpingo Wanu ndiye. Lisiyeni dziko mu chisokonezeke chake chimene ilo likukhalamo, O Mulungu, iwo akuvutika.

³⁶⁶ Ndiye ife tikudziwa kuti Mzimu Woyera wawukulu udzabwera kwa Ayuda pamenepo. Pamene ife tinawona handirede ndi forte foro sauzande atayima pa Phiri la Sinai, atayima ndi Mwanawankhosa, koma Mkwatibwi anali kale Kumwamba. Iye anali atatengedwera kale mmwamba, ndipo Mwanawankhosa anali atabwerera (Yosefe) kuti adzadzizindikiritse Yekha kwa anthu Ake. Ndipo Baibulo linanena kuti padzakhala kusweka pakati pawo pamene iwo ati adzayang’ane ndi kumuwona Iye atayima pamenepo. Pamene Iye adzadzizindikiritse Yekha, iwo adzati, “Munazipeza kuti zipsyera zimenezo?”

Iye anati, “Mnyumba ya abwenzi Anga.”

Kenako iwo adzati, “Anali Iye amene ife tinamupachika.”

³⁶⁷ Ndipo Iye adzanena monga Yosefe ananenera, “Musadandaule, chifukwa Mulungu anachita izi kuti apulumutse moyo wa Amitundu. Silinali vuto lanu.” Kenako iwo anati adzapatukana, banja lina kwa limzake, adzalira ngati mwana yekhayo watengedwa kuchokera pakhomopo.

³⁶⁸ O Atate, tsiku limenelo layandikira, ndiko kutha kwa Masabata Sevente amenewo. Kuti nthawi yayandikira, Ambuye.

³⁶⁹ O Mulungu, mulole liwu—liwu la aneneri owona a Mulungu lifuule motsutsa dona wamakono uyu wa tsikuli, mpingo wamakono uwu, fioloje ya mpingo wamakono iyi.

³⁷⁰ Agwedezeni alaliki awa amene akuwopa kunena Choonadi. O Mulungu, atengeni amuna awa ndipo muwagwedeze iwo kuposa kale, apangitseni iwo adzichitire okha manyazi.

³⁷¹ Koma tikudziwa chinthu chimodzi ichi, ndipo tikhoza kupuma ndi chidaliro chonse, kuti, “Palibe munthu angabwere pokhapokha Atate atamukoka iye. Ndipo onse amene Atate

wapereka adzabwera.” Iwo adzakafika mpaka pamene Inu mwalinga kuti afikepo. Koma Inu munati, “Musawope, nkhosa zapang’ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate wanu kukupatsani inu Ufumu.” Ife tikudziwa kuti Izo ndi zoono. Inu mwatichenjeza ife nthawi yonse kuti padzakhala ochepa kwambiri, kwambiri amene adzakhale okonzeka pamene nthawi imeneyo idzafika. Ndiye padzakhala chiwukitsiro chachikulu, ndipo owomboledwa onse amene anali atawomboledwa kudutsa mu mibadwo adzauka. Koma mu tsiku lotsiriza lino, basi pa mapeto a nthawi, kumeneko Mpingo ndithudi udzakhala mu kagulu kochepa.

³⁷² Chotero ife tikuziwona zimenezo, Atate, ife tikuwuwona Uthenga wa tsikuli. Ife tikuwona kukanidwa kwa Iwo, ife tikuwona kudzipatulako, ife tikuwona zinthu zonsezi.

³⁷³ Ife tikuwapeza anthu Anu akuvomereza kuti iwo siali. . . iwo “si kanthu.” Iwo akungofuna kuti adzazidwe ndi Inu, Ambuye. Tsopano, ine ndikupemphera kuti Inu muligwedeze dzikoli limodzi nawo, masiku pang’ono okha Kudza kwa Ambuye kusanachitike.

³⁷⁴ Tsopano pakati pathu pali matenda, pali anthu amene akufunika kuchiritsidwa mwathupi. Ife sitingawasiye iwo kunjwa, Ambuye, pakuti kunanenedwa, “Musaiwale zabwino Zake zonse: Amene amakhulukira mphulupulu zanu zonse; ndipo Iye amachiza matenda athu onse.” Ife tikupemphera kuti mphamvu Yake yaikulu yochiritsa ikhale pa aliyense amene ali pano. Ngati Inu mungathe kupulumutsa moyo kunjwa uko popanda kusuntha, mtima wake wokha utatembenukira kwa Inu, ndi mochuluka bwanji Inu mungathe kuchiza thupi!

³⁷⁵ Apa pali mipango ili apa. Ine ndikuyidalitsa iyo mu Dzina la Ambuye Yesu, monga Mtumwi wamkulu Paulo anachitira. Mulole aliyense amene wavala mipango iyi achire. Mulole nyumba zosweka zikonzedwense. Mulole ana aang’ono, opanda bambo, opanda amayi, ndi iwo olekanitsidwa, mulole nyumba imeneyo ilumikizane kenanso. Perekani izi, Ambuye. Chiritsani odwala onse tsopano, ndi osautsika, dzipezereni ulemelero kwa Inumwini.

³⁷⁶ Ndipo, Ambuye, ife amene tikuyesetsa kusunga mbiya zathu mmwamba, maso athu mmwamba, mitima yathu mmwamba kwa Inu, kukana kuti ife sikuyanjana mu dziko lino. Baibulo linanena kuti “Abrahamu anatuluka kuchokera kwawo, anatuluka kuchokera mu mzinda wake, kukakhala mlendo mdziko la lonjezo, kuvomereza kuti ‘sanali wa dziko lino’ koma iye anali ‘mwendamnjira ndi mlendo.’” Abrahamu ndi Isaki ndi Yakobo, onse amene ali ndi umboni uwu kuti iwo “si a dziko lino,” iwo mophweka amangonena kuti kuli Mzinda Umene Wowumanga ndi Wowupanga wake ndi Mulungu, ndipo iwo akupita njira imeneyo.

³⁷⁷ Mulole mitima isinthidwe pompano pamene ndikupemphera, Atate, ndipo makhalidwe atengedwe. Ndipo pamene mautumiki a ubatizo azibwera, mulole pakhale kukondoweza kotero pakati pa anthu, mulole pakhale anthu amene sanaganizepo za izo nkale lomwe, mulole izo ziwululidwe. Ndipo Inu munati onse amene Inu munawaitana, Inu—Inu mukana dzawatumiza.

³⁷⁸ Tsopano, ine ndikupereka izo zonse kwa Inu, Ambuye, ndi uthenga waung'ono wosweka uwu wochokera ku chotengera chosauka chopanda kalikonse mmenemo, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu mungotenga Mawu amenewo ndi kuwasungunulira iwo mmitima ya anthu, ndipo mulole iwo asadzathe konse kuchoka kwa Iwo. Perekani izi, Ambuye. Ndikuzipereka izo kwa Inu tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

[M'bale akupereka uthenga—Mkonzi].

³⁷⁹ Pamene mukupanga chigamulo chanu, inu musankhe. “Mukuimiranji pakati pa maganizo awiri?” Inu mwamva chimene Iye ananena. Ngati Mulungu ali Mulungu, mutumikireni Iye; ngati dziko liri mulungu, muzingopitirira. Mukuona? Ngati njira ya chipembedzo ili yolondola, zipitirirani nayo iyo; koma ngati Baibulo liri lolondola, ndiye bwerani kwa Ilo. Mukuona? Sankhani inu ora lino amene mudzimutumikira.

³⁸⁰ Tiyeni basi, mu Mzimu, tiyimbe nyimbo tsopano. Baibulo linati, “Iwo anayimba nyimbo ndipo anatulukuka.” Tiyeni tiyimbe nyimbo yakale yotchuka iyi, *Ndinkonda Iye*, ndi mitu yathu ndi mitima yoweramitsidwira kwa Iye.

Ndinkonda Iye,

Tsopano gamulani chimene inu muti muchite.

Ndinkonda Iye

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine

Nandigulira chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvare.

³⁸¹ [M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ndinkonda Iye*—Mkonzi]. Kodi mungapange chisankho chanu cha Khristu? Osati chisankho, ndendende, mungodzikhuthula nokha, “Ambuye, sindine wabwino. Palibe chabwino mwa ine. Ndiroleni ine ndiyiwale zonse zimene ine ndinazidziwapo. Tsopano bwerani, Ambuye Yesu, musalole kuti izi zidutse pamwamba pa mutu wanga. Mundilore ine ndilandire Iwo ndi kudzazidwa ndi Mzimu Wanu, Ambuye. Kuyambira lero mpakana, ndiroleni ine ndikhale Wanu kwathunthu.” Mungopemphera tsopano, pemphero laling'ono chabe kwa Mulungu; mophweka, pemphero ili, ana, onse.

Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi Waumulungu;

Mungolapa mu mtima mwanu.

. . . ndimveni ine pamene ine ndikupemphera,
Chotsani machimo anga onse,
O ndiloreni ine kuyambira lero
Ndikhale Wanu kwathunthu!

Pamene njira ya moyo ya mdima ndiyenda,
Ndipo zodandaulitsa zindizinga,
Inu Mukhale Namulondola wanga;
Thamangitsani mdima ukhale usana,
Pukutani chisoni, mantha zichoke,
Musandilore ndisochere
Kuchoka ku mbali Yanu.

³⁸² [M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Chikhulupiriro Changa Chiyang'ana Kwa Inu—Mkonzi*]. Awa amene akhulupirira, adzikhuthula okha pamaso pa Mulungu, ndipo atsimikiza kuti palibe chimene chidzakulepheretseni inu nkomwe, simudzavomereza konse za kuthekerakulikonse, ndipo mumafuna kuzipanga izo momveka, zomveka moona bwino ndi Mulungu, dziwe liri ndi madzi mmenemo, kukonzekera ubatizo. Akazi apite kudzanja langa lamanja, ndipo amuna ku lamanzere langa. Utumiki wa ubatizo ukhala mkamphindi chabe. Iwo amene adzikhuthula, ndinu okonzeka kuti musakhulupirire zimene atumiki amanena, zimene azipembedzo amanena, zimene zipembedzo zikunena, koma mutenga njira ya Ambuye, mukhulupirira PAKUTI ATERO AMBUYE, bwerani tsopano.

Pamene njira ya moyo ya mdima ndiyenda,

Izo zikhala akazi *kuno*, amuna cha *kuno*. Ndiko kuyitanira kuguwa kwanu, “Onse amene anakhulupirira, anabwera ndipo anabatizidwa.”

. . . Namulondola wanga;
Thamangitsani mdima ukhale usana,
Pukutani chisoni mantha achoke,
Musandilore ndisochere
Kuchoka kumbali Yanu.

³⁸³ Ndi akazi angati muno mmawa uno. . . Ine ndikunena izi mu Dzina la Ambuye Yesu! Ndi angati a inu akuchita manyazi ndi tsitsi lalifupilo limene muli nalo, mukufuna Mulungu, mwa chisomo Chake, alole ilo likukulireni inu? Mulungu akudalitseni inu.

³⁸⁴ Ndi amuna angati amene akuchita manyazi kuti amalola mkazi wawo kusuta ndudu, ndi kuvala mathalauza amene kwenikweni ndi anu?

³⁸⁵ Ndipo Baibulo linati, “Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu.” Kodi inu mukudziwa kuti Mulungu sangasinthe? Iye sangasinthe. Iye ali ndi chikhalidwe chimodzi, ndicho chiyero. Iye sangasinthe. Ngati simukhala monga Iye, simudzamuwona

Iye, “Popanda chiyero palibe munthu adzamuwone Ambuye.” Ndipo ngati kuvala zazifupi ndi . . . zimamupangitsa Mulungu kudwala mmimba Mwake ndi kusanza, Iye akudwala, ndi *chonyansa*, “nyansi,” inu mudzakwanitsa bwanji nkomwe . . . muli ndi mzimu wonga umenewo mwa inu ndipo mudzakafikako konse Kumwamba? Inu mudzakafikako bwanji Kumwamba ndi tsitsi lalifupi, pamene Mulungu anati, “Ndi chamanyazi kuti mkazi azimeta tsitsi lake”? Iye amakana mfundo kumene za kukhala a—mkazi. Mulungu samasintha. Amenewo ndi Mawu Ake, mzanga, inu kulibwino mumvetsere.

³⁸⁶ Ndipo inu amuna amene mumawalola akazi anu kuchita zimenezo, kodi inu simukuchita manyazi ndi inueni? Kodi simukuchita manyazi?

³⁸⁷ Musakhale ngati Dona Woyamba wa dzikoli. Khalani monga Mulungu! Mukuona? Dzikhuthuleni inu kuchoka ku kachitidwe kamakono ka mdziko, kuti Khristu adzikhuthulire Yekha mwa inu ndipo inu mukhoza kudzazidwa kwenikweni ndi Mzimu Woyera.

³⁸⁸ Iye sangachite zimenezo, Iye sangachite zimenezo, izo ndi—ndi zotsutsana ndi mfundo Zake; Iye adzakhala akutsutsana ndi Mawu Ake, ndipo zimenezo Iye sangachite; Iye sangachite izo pokhapokha ngati—ngati simukugwirizana ndi Mawu Ake. Inu mukuyenera kubwera . . . Iye tikuyenera kubwera ku Ichi china chirichonse chisanachitike. Inu mukudziwa zimenezo, aliyense wa inu mukuzidziwa zimenezo. Ndi angati akukhulupirira zimenezo, kwezani dzanja lanu. Ndithudi, inu mukukhulupirira izo, tsopano tiyeni tichite chinachake pa izo.

³⁸⁹ Mulungu, tichitireni ife chifundo! Momwe ife tikumufunira Iye! Ndi ife pano, tonsefe pamodzi tsopano. Kumbukirani tsopano, pa Chiweruzo, ngati ine . . . Ine ndidzayenera kuyimirira (ndipo limenelo likhoza kukhala mwina usiku usanafike) ndi kuyang’anizana ndi Mawu aliwone amene ine ndawanena. Mwaona, ine ndiyenera ndidzakumane nawo Iwo. Tsopano, kumbukirani kuti kusaweruzika kwachoka mmanja mwanga, kwachoka mu chikumbumtima changa, kwachoka mu solo yanga, kwachoka kwa Mulungu.

³⁹⁰ Ngati inu simutero . . . Ngati mukuima mu makhalidwe amenewo ndipo simukumvabe kutsutsika (psyii!), chiyani—chiyani—inu muchita chiyani? Ndiye inu mukudziwa kuti Mulungu sachita ndi inu, inu mukudziwa kuti inu mwadutsa Iwo. Mukuona? Inu mwadutsa Iwo. Inu mukhoza kukhala nthawizonse wachipembedzo, inu mukhoza kukhala wa mipingo ndi zina zotero, koma inu mwadutsa Iwo. Mawu a Mulungu amapita pansu mkati ndi kukamutulutsamo munthuyo. Ndicho chinthu chimene chimawabweretsanso iwo. Mukuona? Chotero amenewo ndiwo Mawu. Ine ndikumufunsa mtumiki aliyense,

munthu aliyense, kulikonseko, kuti akane Izo motsutsa Mawu a Mulungu. Uko nkulondola. Izo siziri chomwecho, mwaona.

³⁹¹ Chotero tiyeni tikhale Akhristu enieni. Ngakhale ife amene timayesetsa, amene timayesetsa, tikuyenera tidulidwe ndi kuwiritsidwa. Inde, bwana, ife tonse tikuzifuna zimenezo.

³⁹² Mulungu, mundichitire ine chifundo. Mulungu, nditengeni ine ndipo mundiwumbe ine. Ndi cholinga changa, ikatha sabata ino, kuti ndipite pamaso pa Mulungu, kuti ndikafufuze choti ndichite motsatira. Mulungu, nditengeni ine. Chiyani. . . Zonse—zonse zokhudza ine, ndipo ziripo zambiri, zomwe sizabwino, Mulungu, ziduleni izo, ndiro pemphero langa mmawa uno. Dulani mtima wanga, makutu, umunthu wanga. N dipangeni ine, Ambuye, ndipangeni ine chinachake chimene. . . chirichonse chimene Iye akufuna kuti ine ndikhale. Ndiro pemphero langa.

³⁹³ Chirichonse chimene ine ndikuchisowa kuti ndikhale, chiduleni, ndiduleni ine, Ambuye. Ndiwonetseni ine mu Mawu, ndiuzeni ine, ine ndipita ndikachite icho. Molele Ambuye anene icho, ndipo ine ndi. . . Ine ndiri pomwepo kuti ndithane nazo. Chirichonse chimene Mawu a Mulungu akunena, ndi chimene ine ndikufuna kuti ndikhale. Ndikufuna kukhala a—Mkhristu mu Mawu a Mulungu, “Kulola mawu a munthu aliyense kukhala bodza, ndipo a Mulungu akhale woona.” Kodi chimenecho sichingakhale chikhalidwe cha nthawiyi, icho sichingakhale? Umo ndi momwe inu mumakhulupirira izo?

³⁹⁴ Ukuyang’anayang’ana malo obatizidwira, mwana? Eya, kumbuyo kuno, m’bale, usachite kudikirira. Chabwino, udutsire cha uku.

³⁹⁵ Ambiri a inu mukuyenera kuti muzibwera, amuna ndi akazi amene muli okhulupirira, amene ali. . . kudzavomereza machimo awo, kudzabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. (Mudzere *uku*, m’bale.) “Mu Dzina la Yesu Khristu ku chikhululukiro cha machimo awo, ndipo iwo adzadzazidwa ndi Mzimu Woyera.”

³⁹⁶ Tsopano, kwa inu anthu Achikatolika pano, ndicho chimene chikhululukiro cha tchimo chiri. Inu mumanena kuti mpingo uli ndi mphamvu yochotsera machimo, kodi mpingo unachotsa bwanji machimo? Mulungu. . . Yesu anawuwuza mpingo, “Machimo a aliyense amene inu muwakhulukira, kwa iwo akhululukidwa. Aliyense amene muwasunga, kwa iwo asungidwa.” Iwo anachotsa bwanji oyamba, machimo mu mpingo woyamba? Iwo ankawaitanira iwo ku kulapa, ndipo ankawabatiza iwo mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo awo. Osati pansi pa kachipinda kolapira; ayi, ndithudi. Koma iwo ankalapa pamaso pa Mulungu, mmitima yawo pamene iwo anali atayima pamenepo, ndipo iwo ankakhulupirira. “Ndipo onse amene anabati- . . . anakhulupirira amabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera.” Amen. Inu mukunkonda Iye?

Tsopano tiyeni ife tiimirire.

³⁹⁷ Tsopano, pakhala ambiri amene akufuna kudikirira msonkhano wa ubatizo. Enanso akufuna azibwera, enanso amene akhulupirira? Bwerani, mbali iliyonse; amuna kumanzere; kumanja, akazi. Mukhulupirire pa Ambuye Yesu ndi mtima wanu wonse, ndi zonse zimene ziri mwa inu.

³⁹⁸ Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu limodzi, pamene tikubwereza pemphero lachitsanzo ili palimodzi, pamene ine ndikumverera kutsogozedwa mwachirendo kuti ndichite ichi pakali pano. Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, inu mupemphere ndi ine:

Atate athu Amene muli Kumwamba, Dzina lanu Liyeretsedwe.


Ufumu Wanu udze. Kufuna Kwanu kuchitidwe pansu pano, monganso Kumwamba.

Mutipatse ife lero chakudya chathu chalero.

Ndipo mutikhululukire ife zolakwa zathu, monga ife tiwakhululukira iwo amene atilakwira ife.

Ndipo musatitsogolere ife mu mayesero, koma mutipulumutse ife kwa zoyipa. Pakuti Wanu ndi Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemelero, kwa nthawizonse. Amen.

³⁹⁹ Tsopano tiyeni ife tikhalebe ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ndipo ine ndimupempha M'bale Neville kuti abwere ndi kudzanena madalitso, adzanene chimene chiri pa mtima wake, ndipo kenako adzalengeze za msonkhano wa ubatizo umene ukukonzedwa tsopano.

⁴⁰⁰ Mulungu akudalitseni inu, ndiro pemphero langa. Ine ndizikupemphererani inu, inu muzindipempherera ine. Ine ndikufunadi mapemphero anu kwenikweni. 

61-1119 Mphamvu Yangwiro Mu Chifooko Changwiro
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org